

Inde, Ndikufuna...



Kumvetsetsa

Chifuniro cha Mulungu

pa moyo wanga

Kulengedwa chifukwa cha cholinga

Jim Harper

www.UnderstandGodsWill.com

Inde, Ndikufuna...

Kumvetsetsa Chifuniro cha Mulungu pa moyo wanga

www.UnderstandGodsWill.com

{Pali ma vesi 700 omwe atengedwa mu
baibulo ndipo ali kumapeto kwa bukuli}

Copyright © 2019 I was made for a mission inc.

All rights reserved.

Please visit us at www.UnderstandGodsWill.com for more information about this book, the author, and our worldwide ministry. We are looking for partners who would like to help us print and distribute this book around the world, and also to help us translate the book into many other languages. Send all inquiries to: Jim@UnderstandGodsWill.com

Donations to support this ministry can be sent to:

Understand God's Will
P.O. Box 846
Wayzata, MN 55391
U.S.A.

Email: info@understandgodswill.com

Bukhu ili latathauziridwa m'chichewa ndi:

Pastor Mark K. Zimbiri
P.O. Box 44
Chileka, Blantyre,
Malawi C. Africa
Email: markdzimbiri@gmail.com
Phone: +265 882835711

Mulungu akudalitse mark zimbiri chifukwa cha kukhulupirika kwako pofuna kuthandiza anthu ambiri kuti atseguke maso pa dziko lapansi chifukwa cha ulemmerero wa mulungu kudzera mwa mwana wke yesu kristu.

Wolemba, Jim Harper

Ndichifukwa chiyani bukuli linalembedwa



Charlene & Jim Harper

Ndakhala ndili pa banja ndi mkazi wanga Charline kwa zaka 35 ndipo tili ndi ana aakazi okongola awiri nthawi yonse ndinalibe khumbo ndi luso lolemba buku. Ndinayamba kumva kuti ndilembe buku yokhudza ntchito imene Mulungu alinayo pa ife. Kunali kunva kosamvetsetseka ndipo sizimanveka bwino bwino, Kenako ndinangochotsa zimene ndimabvazo. Chifukwa ndikanalemba bwanji zinthu za chinthu chimene sindikuchimvetsa. Zikadakhala zopusa kapena zamisala zinalibe bvuto ndikadatha kulemba.

Kunva kuja kudapitililabe, kunvako kunakhalabe ndi ine kwa zaka zingapo ndipo zinayamba kunveka ngati nkawa yosachoka pa moyo wanga. Zidayamba kumveka kwa ine ngati Mulungu akufuna ndilembe china chake ndipo ndinayamba kuzifunsa ndekha chifukwa chiyani nanga. Chifukwa chiyani ine? Mkati mwa maganizo anga ndinkadabwa kuti kodi ndingakwanilitse bwanji chinthu ngati ichi popanda kukhala ndi luso lopangila chinthuchi. Ndimakonda mavuto koma izi zinali zovuta kuposera utsinkhu wanga. Ndichifukwa chiyani zinakhala m'maganizo anga. Zinapotsera usinkhu ndipo ndinalibe chochita china koposa kuzitaya koma kumva kuja sikunasiyebe.

Zitatha zaka zingapo kumva kuja kunakhala kwakukulu ndi kwamphanvu ndipo ndimapemphera kuti ngati ali iyeyo akundilankhula wasankha munthu wolakwika. Si ine wolemba si ine wopeka komanso sindimaziwa zokhudzana ndi ntchito (Mission) imene ali nayo pa anthu tonse komanso chofunika kwambili ndinalibe luso lililonse limene limafunika polemba buku sizinali mkati mwa maluso anga komanso Mulungu amaziwa kuti ndimalemba ndi zala ziwiri zokha ndipo anati peza wina amene angalembe.

Munthawi imeneyi ndinakumana ndi Nikki Frizzell ku mpingo wanga chimene sindimaziwa za Nikki ndichoti analembapo nyimbo zina. Mmawa wina titangotha amodzi mwa mapemphero ochezera amene anali bwino pamoyo wanga ndinamva imodzi mwa nyimbo za Nikki mutu wake Kupangidwa kuti ndigwire ntchito. Munali phokoso koma phokoso ili ndiye linakula kwambiri limene sindingathe kunyalanyaza makamaka pamene ndinamphempha ambuye kuti andipatse chizindikilo, Chizindikilo chomwe sindingaphonyane nacho chizindikilo ichi chinandililitsa mpaka misozi mmaso mwanga zinali zowawa kwambili ndipamene ndinatulukira kuti kukumana ndi Nikki siinali ngozi sindinamve bwino Ambuye anapitilizabe kundilankhula ndinapitilizabe kumkana. Amatha kuona kusowa kwachikhulupiriro kwanga. Nkhani za Petro zinayamba kuyenda m'maganizo anga pamene Petro anamkana Yesu kunali kulankhulidwa kolimba zinalenga zaka zovuta zambiri koma mapeto ake Ambuye anayankha pemphero langa ndipo yankho linali lonveka bwino lomwe. Ukulondola ulibe

kuthekela kolemba buku popanda ine. Nditamuuza Nikki za zimene ndimalandilazi ndikunva za iye, tonse tinazizwa kuti kukumana kwathu siikunali kwa ngozi tonse tinadziwa kuti nyimbo yake ndi buku limene ndikufuna kudzalemba zinapangidwa limodzi kuwathandiza anthu kumvetsetsa kuti Yesu ndindani ndikuthandiza wina aliyense wa ife kuti adziwe kuti Mulungu ali ndi dongosolo ndi ntchito ya Munthu wina aliyense tinapangidwa kuti tikagwire ntchito. Ziliba kanthu kuti ndiyaling'ono zinali bwino ndipo zinakonza maitanidwe athu komabe buku linayenera kulembedwa inde Ambuye wathu kulowa ndikukhulupirila koma ndithandizeni kugonjetsa kusakhulupilira kwanga. Ndinalibe luntha lililonse mdela limeneli komanso sindimadziwa mutu wake. Izi zinali ngati phiri lilikulu patsogolo panga lomwe ndikuyenera kulikwera ndisanasoweka kukhala ndi khumbo loti ndichitire. Ndinadzipempherela ndipo Ambuye anandiyankha, anandipatsa khumbo lotsegula mau ake kuti nipeze mayankho a Mafunso ofunikilawa mmmmm chinali chozizwa chanji anandipatsa khumbo lochitira kanthu kamene sindinayambe ndalotako ndiye kudzera mwa chikhulupirilo bukuli linalembedwa kunali ngati kukwera phiri la Mulanje koma ndi iye zinthu zones zinatheka.

Ndikudziwa tsopano ndikumvetsetsa zimatengera chikhulupiriro chaching'ono ngati mbeu yampiru Mulungu anatiuza kuti ngati tingakhale ndi chikhulupiriro chaching'ono ngati kambeu kampiru palibe chimene chidzakhala chokanika. Timadziwa ngati chinachake chikuoneka kukhala chosatheka (ngati kulemba bukuli) chimachokera kwa Mulungu? Ndizophweka ngati tingazikwanilitse tokha ndipo sitikusowa Mulungu. Ndiye sitikanafunanso chikhulupiriro kuti tikwanitse ndiye chikhulupirilo ndi chofunika kuti tikwanilitse zosatheka popanda chikhulupirilo ndikosatheka mumkondweletsa Mulungu ndipo chifukwa wina aliyense amene abwera kwa Mulungu akuyenera kukhulupilira kuti alipo ndipo apereka mphoto kwa yense womphempha iye ndikudzera m'chikhulupirilo chathu kuti tithakuchitita moposa mmene tapemphera kapena kuganiza ndiye kudzera m'chikhulupiriro bukuli linalembedwa.

Ndikukhulupirila kuti izi zakusunthani kuti muchite zinthu zosatheka mvetselani kwa Ambuye adzakudalitsani kumvetsera kwa iye ndikukhulupirila zonse ndizotheka kwa iwo amene akhulupirila

Ndalemba bukuli koma si ine wolemba ndatulutsa bukuli koma si ine wotulutsa bukuli, si ine m'busa, wamsembe, mtumiki, Bishop kapena waukachenjede wa Baibulo ndinangochita pazimene Ambuye anaika pamtima panga ndipo mwachisomo chake ndinalimba Bukuli mvetselani ku zimene akulankhula pamtima panu Ambuye safuna china chilichonse koma chabwino kwambiri pamoyo wanu mwa zonse akufuna akupatseni mtanda wa madalitso pa inu

Mulungu adalitse

Jim Harper

AMENE ANALEMBA

MAUMBONI A ANTHU AMENE AWERENGA BUKULI

Kuchokera kwa David

Jim ndi buku lamphamvu mafunso anga ambiri ayankhidwa moyo wanga ndi chikhulupiriro change zichita zosintha zambiri komanso zayamba kale ndikunwa kusintha tsopano.

Kuchokera kwa Abusa a Charles (Rwanda)

Ndine wokondwa ndipo ndikuthokoza Jim Harper amene akundiphunzitsa zambiri zokhudza Mau a Mulungu kudzera m'buku lakeli lodabwitsali likundithandiza kwambiri kuunikira mzimu wanga mukulalikira kwanga ndikudzoza kwa mphatso yanga kukhala m'busa wankhosa zake.

Kuchokera Kwa Abusa a Jean (Haiti ndi Dominic Republic)

Ndimakonda buku limene unandipatsa titakumana Mutu 6 wa buku lako ndi umene ukunditakasa kwambiri ndikufuna kukuitana ubwere ku Santiago los Caballeros kuti udzatumikire kagulu la azibusa limene ndimakhala nalo.

Kuchokera kwa Pamela

Buku lako lasintha moyo wanga ndakhala ndikuphunzira Baibulo kwa zaka 4 zomwe ndinakondwa nazo kwambiri ndinali ndi nthawi yovuta kumvetsetsa chithuzi thunzi chachikulu. Buku lako linali lophweka powelenga koma muli ndondomeko ndi chitsogozo chabwino ndimamva kuti Mulungu amandilankhula kudzera mzolemba zako Buku lako ndagawana ndi abanja langa ndi abwenzi anga kuti nawonso achite chimodzimodzi.

Kuchokera Kwa abusa Theodore (Kenya)

Ndine wobadwa mwatsopano komanso mlaliki Buku lako ndilotakasa komanso lothandiza landipatsa mzeru komanso maso oonera kuchokera mmawu a Mulungu ndipo tsopano ndikumvetsetsa chifuniro cha Mulungu pa moyo wanga. Buku lako landipanga kusamala pa zimene ndimakwanitsa.

Kuchokera kwa Jacqueline (Rwanda)

Buku lako ndilodabwitso komanso chuma chachikulu. Nditapita kumudzi kwathu kutchuthi ndinawuza abanja lakwathu ndi abwezi anga onse akhale nalo bukuli Mulungu amandilankhula kudzera m'buku lako Mulungu akudalitse, ndikudikilira buku lina lotsatira.

Kuchokera kwa abusa a David (India)

Ndinali ndi nkhuli ndi buku lanu matsamba onse 124, Ambuye alemekezeke chifukwa cha Buku lamphamvu nditawerenga tsamba lililonse ndikupemphera kuti nditanthauzire bukuli Mu Telugu chilankhulo cha kwathu kuno kumwela chakummawa kwa India, chonde ndilore monga wogwira naye ntchito mu utumiki wako.

Kuchokera kwa Abusa Jean (Rwanda)

Zikomo m'bale wokondedwa Jim Harper ziphunzitsa zako ndapeza kuti Yesu ndi njira yokhayo ya chisangalalo chenicheni ndazipereka kugawa zimene ndawerenga m'buku lako ndi ena ndiye ndikupemphera kwa Ambuye kuti andisankhe mwa opambana kumwamba.

Kuchokera kwa abusa a Paul

Jim harper ali ndi chikhulupiriro choona ndipo zikuonetsa mu buku lake lolimbikitsali Jim wapereka mayankho ndikumumikizana ndi moyo watsiku ndi tsiku ndipo mfundo zake zakhazikika mu Baibulo.

Kuchokera kwa abusa a Jean Felix (Rwanda)

Utumiki wanga kuRwanda ukuvomereza ndipakamwa pawo kuti buku la Jim Harper lakweza uzimu wathu ndipo latibweretsa chifupi ndi chisomo chodabwitsa cha Mulungu Jim ndimaliki wathu ngakhale sakhala nafe ku Rwanda koma tikupempherera kuti tsiku lina tizamuona ku Rwanda akutiphunzitsa maso ndi maso Buku la Jim ndilodabwitsa ndipo ndi buku lamphamvu lomwe sindinalionepo. Buku lake lithandiza kutsutsa ndi kukopa ambiri kubwera kwa khristu.

Kuchokera kwa Adecaide (Rwanda)

Jim ndikukuthokoza chifukwa mafunso anga ambiri ayankhidwa. Buku lako lodabwitsali landithandiza kudziwa dongosolo la Mulungu. Bukuli ndimalitenga ngati chuma changa.

Kuchokera kwa Joyce

Ndikudalitsika ndikamawerenga bukuli chimodzi mwa khumbo langa ndikulemba. Sindingalingalire kuchuluka kwa nthawi imene unali nayo kuika pamodzi buku lodabwitsali losavuta kuwerenga. Ndalikonda bukuli makamaka mmene wayalira mfundo zako kolinganaso ndi malemba pano popeza ndili ndi buku ndikuganizila za abwezi anga kuti ndawapatsenso ndalimbikitsidwa.

Maumboni ambiri atha kupezeka pa website yathu ya

www.understandGodswill.com

ZAM’KATIMU

Mutu 1

NDINAPANGIDWA KUTI NDI MUDZIWE MULUNGU

Mulungu adzadikila mofatsa lye anatiuza kuti adzabweranso ndi chifukwa chiyani Mulungu anafuna kukhala pakati pathu?

Mulungu akufuna kuti tidziwe

Mutu 2

NDINAPANGIDWA M’CHIFANIZO CHAKE

Mulungu amadziwa chomwe amachita anakupangani kukhala ali ndi dongosolo nawe

Mutu 3

NDINAPANGIDWA KUTI NDIKHALE KUDZERA MZOVUTA ZAMBIRI

Mchikhalidwe cha uchimo nditha kumakumana ndi zovuta chifukwa ndikunyengedwa

Nditha kumakumana ndi mavuto chifukwa ndikukhala m’dziko lokugwa nditha kumakumana ndi mavuto chifukwa Mulungu akupatsa chilango kodi mfundo zaMulungu

Mutu 4

NDINAPANGIDWA KUTI TIDZIWE DONGOSOLO LA MULUNGU

Kuulula dongosolo la Satana (Plan)

Dongosolo la Mulungu

Nditha kumdziwa Mulungu zoona? Kukhulupilira usanaone

Mutu 5

NDINAPANGIDWIRA KUSANKHA

Tisanafe tikuyenera kusankha ndingakhale ndi moyo motani nditatha kudalira Mulungu

Mukutanthauza atha kunditeteza ndi kundtonthoza?

Ambuye adzadalitsa amene akumvera Mau

Mutu 6

NDINAPANGIDWA KUTI NDI GWIRE NTCHITO MUNALI MU DONGOSOLO LA MULUNGU MUSANABABWE

Mphatso zomwe mwapatsidwa sizanu khalani a khungu

Chifuniro cha Mulungu chichitike

ZOONJEZERA

1. Ukumwa kudalitsidwa? Utha kudalitsa enanso
 2. Kuwotchedwa ndi lawi la Mphatso za Mulungu
 3. Ndizophweka kukhala khungu
 4. Mphatso ya Mulungu ndiyaulele kotero kuti chilichonse chomwe tilinacho ndichaulele
-

Malemba a M'musi

Chidziwitso chokhudzana ndi zolembedwa za Mmusi mwa bukuli mu buku lathuli zolembedwa za mmusi zonse muli pafupifupi ma vesi a baibulo 700 onse aikidwa kuseli kwa bukuli anthu ambili amanena kuti ndilophweka kuwerenga chifukwa sitinasiye mmusi mwa tsamba tili ndi mtundu wina wa bukuli lomweli imene ma vesi ali mmusi mwa tsamba ndiye tsamba lililonse limakhala ngati buku lowerenga.

Pakuti vesi ya m'baibulo imene mukuwerenga ili patsamba lanu pomwepo mutha kuona lemba lonse mukufuna kuwerenga mavesiwa muwapeza pa webusaiti yathu mmusimu.

Bukuli lapangidwa kuti litha kuwerengedwa pa mitundu yonse ya ma Computer monga Desktop, Laptop, Tablet Computers, Kindle/tire readers, Ipad/Iphones ndi ma Android onse ndi mafoni kawirinso mutha kuzipezans pa webusaiti yathu mmusimu.

Tili ndi buku lomwelinsu lomvera zimene zikutanthauza kuti mutha kukhala pa ndalema wanu kapena mukugwira ntchito yanu yammawa muli ndi Ipod uku mukumvetsera bukuli. Izinsu zimakhala bwino mukamayendetsa galimoto imene ili ndi a sipika a Bluetooth pitani pa website yathu pamsipa ndi kuyamba kumvetsela buku lathu ndipo mukamamvetsera mukhale ndi chida chopititsa mau ku ma Bluetooth speakers.

Yesetsani kuwauza ena zokhudzana ndi mabuku athu ndi omvera omwe.

MUTU 1

NDINAPANGIDWA - KUTI NDIMDZIWE MULUNGU

MULUNGU ADZADIKIRA MOFATSA

Ngati mwatsegula buku ili ndipo mwatsegula mutu woyambawu ndikuyamba kuwerenga ndiye kuti mwapanga chiganizo chachiwiri chofunikira koposa chokhudza kum'dziwa Mulungu kuti iyeyo ndi ndani. Mwatsegula mtima wanu. Mukuona kodi, Mulungu sadzadziumiliza kuti alowe mu mtima mwanu. Iye nthawi zonse adzadikira kufikira inu mutamulora kuti alowe. Iye anadziwa kuti inu munakonzedwa ndiponso kulengedwa kuti mukam'dziwe kuti iyeyo ndi ndani. Iye anakupatsani inu malinga liro oti mudzitha kuganiza, kusinkhasinkha komanso kumvetsetsa, ndiponso malingaliro omwe angakupangeni inu kudziwa kuti ndinu cholengedwa kuti ndinu cholengedwa chapadera - dera komanso chopatulika. Palibe munthu wofanana ndi inuyo.

Mulungu wakupatsaninso inu chikhumbokhumbo chofuna kudziwa chifukwa chomwe inu munalengedwera komanso kuphunzira kuti kodi mlengi wanuyo ndi ndani. Tonsefe tinalengedwa kuti tikhale womvetsetsa kuti kodi Mulungu ndi ndani, komanso kupeza kuti kodi ndife ndani, ndiyo kutsegula mtima wathu. Mitima yathu iyenera kukhala yotsegula kuti tili ofuna kuphunzira kuti kodi Mulungu ndi ndani.

Choncho mwinatu inu mukudabwa ngati kutsegula mtima chiri chinthu chofunika chachiwiri chomwe inu mungathe kuchita kutimumvetsetse kuti kodi Mulungu ndi ndani, chiganizo chofunikira koposa ndi chani? Chabwino, mtima wan ukuyenera kukhala uli chitsegulire kwa kanthawi pang'ono kuti muthe kudziwa yankho lafunso limeneli. Pali zinthu zambiri zomwe mukusowekera kuti muziphunzire poyamba ngati kuli koti funsoli nlofunikira bwanji. Mtima wanuwo ndilo khomo lomwe Mulungu angathe kulowerapo kutero kuti muthe kumvetsa chomwe iyeyo ali, choncho mtima wanuwo ukhale chitsegukire kwakanthawi pang'ono Mulungu sangathe kudziulura yekha kwa inu ngati mtima wanuwo uli wotseka. Ngati mudamfunafuna iye ndi mtima wanu wonse, iye akulonjeza kwa inu kuti mudzampeza iye.

ITYE ANATIUZA KUTI ADZABWELANSO

Kodi inu munalii kudziwa kuti Mulungu anatiuza kuti iye analinkudza kudzakhala pakati pathu zaka zambiri zapitazo iyeyo asanafike? Pakati pa zaka mazana anai ndi mazana khumi ndi awiri. Mulungu asanadze kudza khala pakati pathu iye anatipatsa ife tsatanetsane wokhuza chikonzero chake:

- Iye anatiuza kuti adzakhala pakati pathu ndipo kuti adzayendayenda pakati pa ife. ^{3 4}
- Iye anatiuza kuti adzabadwa mwa namwali ndipo dzina lake lidzatchedwa Emmaueli, kalonga wa mtendere, phungu wodabwitsa, ndi Mulungu wamphamvu zonse. ^{5 6}
- Anatiuza kuti kwa nthawi yaitali iye anali chete zokhuza kutumiza mwana wake kudziko lapansi, kudzatipulumutsa ife. ⁷
- Anatiuza kuti iye adzatengera (adzabweretsa) chilungamo ku maiko ⁸ ndipo adzapanga pangano latsopano kwa anthu ake. ⁹
- Iye anatiuza kuti adzalemba malamulo ake m'maganizo athu ndim'mitima yathu. ¹⁰
- Iye anatiuza kuti adzasenza machimo a ambiri ndipo kuti machimo athu adzakhululukidwa. ^{11 12 13}
- Anatiuza kuti adzafa kulasidwa chifukwa cha machimo athu (zolakwa zathu), kumenyedwa chifukwa cha mphulupulu zathu, ndipo ndi mikwingwirima yake ife tidzachiritsidwa. ¹⁴
- Anatiuza kuti adzauka kwa akufa. ¹⁵
- Anatiuza kuti adzakwera kunka kumwamba. ¹⁶
- Anatiuza kuti adzatsanulira mzimu wake pa anthu onse. ^{17 18 19}

ZONSE IZI ZINAUZIDWA KWA IFE ZAKA MAZANA MULUNGU ASANABWERE KUDZAKHALA NAFE PAKATI PATHU

Aneneri a Mulungu ku chipangano chakale chonse anafotokozera kwa ife chifukwa chomwe Mulungu anayenera kudza kudzakhala nafe pakati pathu. kuti pokhapokha iye atadza, chifukwa ife ndiye ochimwa tonse, tonse

tikadaonongeka.²⁰ Njira yokhayo yomwe mulungu akadakhonza kutipulumutsira ife kuchoka ku uchimo wathu inali yoti abwere kudziko lapansi, kukhala pakati pathu, ndipo adakali ndi ife pansi pano, ationetsere momwe tiyenera kukhalira, komanso kutifotokoza chifukwa chomwe iye adzasowekera kufa chifukwa cha ife. Iye adzakhaladi nsembe yeniyeni yotipulumutsa ife kuchokera ku machimo athu-chinthu china chake chomwe ndi Mulungu yekha yemwe akadatha kuchichita.

Choncho, nkhani yonse yomwe yalankhulidwa m'chipangano chakale chonse ndi chipangano chatsopano chomwe ndi nkhani yokwanira bwino ndithu. Chipangano chatsopano chimakwaniitsa chipanano chakale, ndipo chipangano chatsopano chimatipatsa ife mfundo yeniyeni ya zomwezilinkudza mtsogolo mwathu. M'chipangano cha tsopano nkhanayi ikupitilira, ndiponso ikukwaniritsidwa:

- Iye anatiuza ife kuti ali chifanizo cha mulungu wosaonekayo.^{21 22}
- Iye anatiuza ifechifukwa chomwe anayenera kupangidwa kukhala munthu m'njira zonse.
- Anatiuza kuti anayenera kubwera kudzafikira ochimwa.^{24 25}
- Anatiuza kuti adzapereka kachisi watsopano (iye mwini) pakutha pa masiku atatu-wosamangidwa ndi manja²⁶
- Anatiuza kuti iye anadza kudzapereka moyo wake chifukwa cha ambiri.
- Anauzam'modzi wa otsatira ake (Yudasi) kuti adzampereka iye -nthawiyi isana isanafike^{29 30}
- Anauza omtsira ake kuti iye adzatsutsidwa ndikuweruzidwa kuti aphedwe ndipo kuti iye adzanyozedwa, kuchitidwa chipongwe, kumenyedwa, kulavulilira, ndikuphedwa. Anauza omtsira ake kuti zikadzatha kuchitika zonsezi iye adzanka kwa akufa akatha masiku atatu.^{31 32 33 34 35 36 37 38 39 40}
- Anatiuza kuti imfa yake idzayambitsa pangano latsopano pa anthu.⁴¹
- Anatiuza kuti kwa iwo omwe adzakhulupilira mwa iye machimo ao adzakhululukidwa ndipo adzapeza moyo.^{42 43}
- Atauka kwa akufa amitiuza kuti angonjetsa satana ndipo kuti pokhapokha iye atachoka mdziko lapansi- Mzimu wa Mulungu sadzaza kudzakhalala pakati pathu.⁴⁴
- Mulungu anabwera m'dziko lapansi munthu. Iye anayenera kuterodi; iyi inali njira yokhayo yoti iye athe kutipulumutsa ife. Dzina lake, ndiye Yesu.
- Kutsimikiza kuti iye chikonzero chake chinakwanilitsidwa mwa ngwiro, Yesu atauka kwa akufa iye anattipatsa ife zitsimikizo zamphamvu kuti analidi wamoyo. Yesu anaonekera kwa anthu 500 pa masiku makuni anai otsatira kuuka kwake ndipo iye anapitirira kulankhula za ufumu wa Mulungu.^{45 46} Iye anauza wina aliyense kuti pamene achoka, mwachitsanzo, iye atakwera kumwamba⁴⁷ adzasiya Mzimu wa Mulungu yemwe adzakhale mwa ife. Mzimu wake udzatitsogolera ife m'ziganizo zathu zonse ndipo Mzimu wake udzatipatsanso mtendere ndi chithonhozo.

- Choncho, zomwe Mulungu anatiuza m'chipangano chakale kuti zidzachitika zinachitikadi. Zinachitika nde nde nde monga momwe iye adanenera kuti zidzachitika zinali, ndipo ziri chokonzero cholungama, zokwaniritsidwa mwangwiro.

NCHIFUKWA CHIYANI MULUNGU ANASOWEKERA KUDZAKHALA PAKATIPATHU?

KUPEREKA CHOONADI MD'ZIKO LODZALA NDI ZOSALUNGAMA

Mulungu anatuma Mwana wake Yesu, kudzakhala pakati pathu, chifukwa kaya ndife ndani kapena kya tachita chani, kapena kaya tachita chani, Mulungu ali ndi chikondi chopanda malire pa munthu wina aliyense wa ife. Ndipo munthu ameneyo ndi inuyo. Tangodziyang'anani pa galasi kwa kamphindi. Mulungu amakukandani. Inde, inuyo.

Pakuti Mulungu anaconda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asataike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu samatuma mwana wake kudziko lapansi kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye.

Yohane 3:16-17

Chokhumba cha Mulungu chinali, ndiponso chidakali cholinga chake, kupereka choonadi chake m'dziko limene liri lodzala ndi chisalungamo. Chifukwa choti iye anadziwa kuti munthuyo adzachimwa, iye anadziwanso kuti adzasowekera momboli. Iye anadziwanso kuti ife sitingadzipulumutse tokha. Palibe munthu wokhala ndi mulingo uliwonse wauchimo yemwe akadakhala ndi kuyenera kutipulumutsa ife ndi moyo wake ai.

Uku kukanangokhala kuti munthu wochimwa akuyeserera kupulumutsa munthu wochimwa wochimwa nzake -ndipo m'chitidwe woterewu sugwira ntchito konse. Kunayenera kukhala munthu wopanda ntchimo -ndipo mwa anthu onse adziko lapansi palibe amene akadafikira pamenepo.

MALINGALIRO AKALE LOMWE

Motero, pena pake m'nthawi zakalelo Mulungu anadziwa kuti adzasowekera kutuniza mwana wa iye yekha, Yesu (mwachitsanzo, Mulungu m'thupi), kudziko lapansi kukakwanilitsa utumiki wofunikirawu. Mosemphana ndi Chipangano chakale pomwe nsembe sidzinathe kuchoketsa machimo, nsembe ya Yesu inayenera kuchitika kamodzi basi ⁴⁸ chifukwa idzakhala nsembe.⁴⁹ Mulungu

akadakhocha, ndipo adzakhonza kudza ku dziko kudzakhalana monga munthu wosachimwa kukatsuka chikhalidwe cha uchimo wobadwa nao ndi ife tonse.⁵⁰

*Pa zanu ziri zofiira zidzayera ngati matalala: ngakhale Ngakhale
zoiziri zofiira ngati kapezi, zidzakhalana ngati ubweya wankhosa,
woti mbu.*

Yesaya 1:18

Ndichikonzero champhamvu motani ichi! Mulungu anadziwa kuti iyi ndiyo njira yokhayo yolumikizana ndi iye, kumva ululu wofanana komanso nsautso ndi kukanidwa zomwe ife timamvazi, kukumana ndi zokumana nazo zofanana zomwe timakumana nazo, ndipo iye adakali m'dziko lino lapansi akadankonzanso kutiphunzitsa momwe ife tiyenera kukhalalira. Iye adzakhalanso Mpulumutsi wathu weni weni. Iye analankhula momveka bwino kwa ife kunena kuti iye anatsika kuno kudziko lapansi osati kudzachita chifuniro chake ai- koma kudzachita chifuniro chake cha Atate chifuniro anamtuma iye.⁵¹

ASATAYE NGAKHALE MOYO UMODZI

Mulungu amagwiritsa ntchito abusa a umunthu kuti afotokozere m'mene m'busa wabwino amachitira pamene ngakhale nkhoa yake imodzi yokha isowa. M'busa wabwino adzayendayenda kuno ndi uko kuifunafuna ndi kuipulumutsa ngakhale nkhoa imodzi imeneyo.

*Ine ndine m'busa wabwino; m'busa wabwino ataya moyo
wake chifukwa cha nkhoa.*

Yohane 10:11

Choncho ichi ndicho chinali cholinga cha Mulungu. Iye anabwera kudziko lapansi kuti atipulumutsa. Pamene ife tataika, kapena tikalowerera, Mulungu satisiya ndi kutinyanyala ai. iye nthawi zonse amakhala pamenepo-kufunafuna. Iye anabwera a dziko lapansi kuti adzafufuze wina aliyense chifukwa kuti munthu wina aliyense amakhala wotaika mu nthawi ina kapena imzake. Tingophonyana ndi kukhudza kwa mlengi wathu timasokera (kutaika), kupanduka ndipo pomwepo timachimwa.⁵³ Timakhala mwa njira imeneyi chifukwa sitimadziwa chifukwa chomwe tinabadwira kuti zizitero ai.

Chinthu chomwetsa chisoni chokhuza kukhala wotaika ndi chakuti kutaika ndi chakuti kutaika kumatiika ife pansu pa ulamuliro wa satana-yemwe ali ngati mkango wobuma. Satana amadziwa bwino lomwe kuti ngati ife adzatha kutitengera kuchitaiko choopsa cha dziko lapansi, motere amabweretsa pa ife mayesero osiyanasiyana kuti atipangitse ife kutaika. Mayesero osiyanasiyana kuti atipangitse ife kutaika. Mayesero, omwe iye amabweretsa pa ife ndi monga mayesero a chuma, kunyada (kudzikuza) kufuna kutchuka, kutikopa ife kuti

tikakhala ndi “zochuruka” ndiye kuti tidzakhala wosangalala, kuti tidzatha kukhutitsitsa moyo wathu wathupi wapansi pano (inde, chiwerewere) pena pali ponse mu nthawi ina iriyonse, ndiponso china chirichonse chomwe chingatisocheretse ife kuchoka pamaso pa Mulungu. Satana amatinyenga ife kuti tidziganiza kuti pali choopsa chilichonse tikachita zofuna tokha, kapena kukhala moyo wanthawi, yochepa, kapena tikadziika ife eni patsogolo-kuposera ena onse. Koma iyi si pulani ya Mulungu ai-sizidzabweretsa chimwemwe kwa iye konse. Ife kawirikawiri timaganiza zidzatipatsa mtendere, koma ichi ndi chimodzi cha zinyengo zikuluzikulu za satana.

Satana amakondwera kwakukulu pamene anthu akhala mu umbuli wa pa Mulungu ndi mphamvu yake.

Taonani: Pokhala mau oti umbuli (kukhala mbuli) agwiritsidwa ntchito nthawi zochuruka m'buku lino, tidzakuonetserani m'mene Bukula mtanthauzira mau (dikishonare) la Webster limatanthauzira mau ofunika amenewa. Akuyenera kukhala cha pamtima chathu pofuna kupewa kukhala mbuli pa ziphunzitso za Baibulo. Monga momwe Satana anakondera pamene anthu ali mbuli pa za mulungu ndi mphamvu yake pamene tichulukira kukhala mbuli pa za Mulungu pamodzi ndi cholinga chake cha pa ife, pameneponso satana adzakhala ndi mphamvu zoposa pa ife.

Kukhala mbuli:

1. Kusowekera chidziwitso mkati kapena maphunziro; munthu wosaphunzira.
2. Wosazindikira; wosadziwa kanthu/ wosadziwitsidwa.
3. Kuonesera kusowekera kwa chidziwitso kapena maphunziro.
4. Kupanda chidziwitso kapena mfundo/mau pa mutu wina wake kapena mfundo ina yake.

IYE ANABWERA KUDZAGONJETSJA CHOIPA

M'baibulo m'dima umaimilira tchimo ndiponso chiweruzo.⁵⁴ Tchimo m'miyoyo yathu limadetsa mamvetsetsedwe athu komanso limatigwetsa kutichita chifuniro chake cha Mulungu. Kuli ngati kulowa m'dzenje pamene uli kuyendetsa galimoto. Tonse timagwa m'dzenje ndithu (mwachitsanzo, tonse timatha kuchimwa ndithu), ndipo nthawi iriyonse, yomwe ife tigwera m'dzenje m'menemu timachoka pa kuchita chifuniro chake cha Mulungu. Ngati tingagwere m'dzenje lomwe ndi lakuya kwambiri tingathe kuvulala kwambiri ngakhalenso kufa kumene.

Pamene tikhala kunja kwa kuchita chifuniro chake cha Mulungu sitingathe kuongolera bwino chiongolero chathu molunjika komanso moona. Pangathe kukhala masiku ena pomwe zinthu sizikuoneka zoipa kwenikweni, komabe kukhala kunja kwa kuchita chifuniro chake cha Mulungu ndi zinthu zoopsa kwambiri. Kukhalamo. Miyoyo yathu idzakhala ya pendapenda, yosakhadzikika ndiponso yosautsika monganso monwe ingachitire galimoto yomwe yaphonya

mseu. Nseu. Ndipo ngati sitingadzibwezeretse m'chifuniro cha Mulungu, ndiye kuti zinthu zina zoipa zidzatha kuyamba kuchitika pa ife. Ichi ndichifukwa chakuti ngati ife tipezeka ochimwa ndiye kuti Mulungu sangathe kutiteteza ai, iye amatilora kuti tikolole zomwe tinafeso.

Anthu ambiri samatha kudziganizira alikuyenda mum'dima - koma ndi momwe Mulungu anayang'anira pa anthu omwe ali mu mdima wa uchimo m'dziko lino la kugwa. Iwo ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu. Anthu omwe akuyenda mopanda kutsatira choonadi. Choonadi chak. Ichi ndicho chifukwa chomwe Yesu amayenera kubwera ku dziko lapansi kudzaononga choipa ndikutiphunzitsa ife choonadi chake. Iye amayenera kudzatiphunzitsa ife choonadi m'dziko lomwe liri lopanda choonadi. Mulungu amafunitsitsa kutiongolera ife kuzemba maenje omwe ali panseu m'chitsogolo mwathu, maenje omwe akumbidwa mochulukira sitimatha kuwaona maenje amenewa mtsogolo mwathu, koma Mulungu amatha kuwaona. Tsatirani mau a Mulungu ndipo kuunika kwake kowala kudzaunikira njira mtsogolo mwanu kotero kuti mudzatha kuongolera bwino kupewa maenje a satana. Ichi chidzakulorani inu kukhazikika molingana ndi chifuniro chake ndipo chidzakupatsani inu chiyembekezo ndi tsogolo lokoma.⁵⁵

MULUNGU SAMAFUNA KUTI IFE TIVULALE (TIPWETEKEKE) AI

Tonse timadziwa kuti kuwala ndi chiyani. Timadalira kuwala pamene tiri mu m'dima kuti tisagwe kapena kupunthwa. Ichi ndicho chifukwa chomwe mau a Mulungu amayenerekezedwa ndi kuwala (kuunika).⁵⁶ Chifukwa amathandizira kuwala ndi chitsogozo pamene ife tiyenda m'dziko lapansi kotero kuti ife tisayende mum'dima. Iye amabwera kuno kudziko lapansi kuti ife tikathe kukhala ndi moyo wochuruka.⁵⁷ Ndipo tikamakhala molingana ndi chifuniro chake (choonadi) nafenso tidzakhala othechera kuwalitsa kuunika kwa mulungu kwa anthu ena omwenso akuyenda molunjika ku maenje-kotero kuti iwonso adzakhocha kuona bwino lomwe ndikupewa mavuto omwe ali mtsogolo mwao.

Pamene Mulungu anatienga ife iye anadziwa kuti ifeyo tidzakhala chiposyinjolo ndipo iye anadziwanso kuti tidzatha kuchimwa - chifukwa anatipatsa ufulu wosankha chochita. Timadziona zoterezi kwa ana athu omwe. Timatha kudziwa kuti ana athu tsiku lina adzatha kuphwanya malamulo athu. Timadziwa kuti nthawi zina angathe kudzatipandukira ife. Timadziwa kuti nthawi zina adzatha kunyalanyaza malangizo athu kholo nthawi zonse limalira kukhala ndi mwana yemwe amakhala ndi makhalidwe abwino ndiponso kutsatira maweruzo kuti motero asavulare.

Motero, Mulungunso ali chimodzimodzi. Iye samafuna kuti ana ake avulazike. Iye anabwera kudziko lapansi kotero kuti athe kukhala nafe pafupi pafupi ndikutiphunzitsa ife m'mene tingathe kukhalira. Mwatsoka, ambiri a ife timamukana iye. Sitimasamala nkomwe. Timachita zomwe tifuna osadziwa kuti

pamene ife tituluka m'chifuniro cha Mulungu timampangitsa satana kukhala wokondwa kwambiri. Satana amadziwa kuti ngati ife tipandukira Mulungu, kapena ngati tinalanyaza Mulungu, ndiye kuti pomwepo tatengapo sitepe yotsatira njira za satanayo, njira yomwe iye (satana) angathe kuwagiritisa ntchito kutichotsera ife ku chifuniro cha Mulungu-maenje omwe anakonzedwera kutiononga ife.

Tonsefe timadziwa bwino momwe tizikhalira munthu ukagwera m'dzenje lomwe sunali kuliona, zimawawa kwambiri. Koma ngati tingathe kuvomereza, tidzatha kukumbukira kuti mwina mwake chinali chifukwa choti ifeyo pena pake tinachotsa maso anthu pamseupo kwa kwa kamphindi kena kake. Tinaphonyana ndi zikwangwani za mchenjezo za panseu za mulungu. Sitinamvetsere ku chikumbumtima chathu. Ndipo izi ndi zomwe satana amafunitsitsa kuti ifeyo tichite. Iye amafunitsitsa kuti potoza ife amafunitsitsa kuti ifeyo tichite. Iye amafunitsitsa kutipotoza ife ndikutinong'oneza m'makutu mwathu-kotero kuti sitimasowanso kukhala ochenjera pa maenje ake oopsa (mwachitsanzo machitachita oopsa m'miyoyo mwathu), kapena kutsatira ndondomeko za Mulungu.

Pamene ife tinapandukira monga mwana sitingathe kumvetsa chifukwa chomwe atate athu anachita chomwe anachita chija. Tikudziwa tsopano lino monga makolo kuti iwo anachita chonchija chifukwa choti atate athuwo anatikonda ife; timaoneka kuti taiwala phunziro lofunika kwambiri limeneli. Monga achikulire nsinkhu taiwala kuti Atate wathu a kumwama amafuna zabwino zokha pa ife. Komabe ife timamukana iye, ndipo timamunyalanyaza iye, ndipo timachimwa. Timaiwala msanga ndithu.

MULUNGU AMAFUNA KUTI IFE TIMDZIWE IYE

IYE AMAFUNITSITSA KUTIPATSA IFE NZERU NDI CHIDZIWITSO

Kodi mumadziwa kuti Mulungu amakukondani angakhale inuyo simumamukonda?⁵⁹ Mulungu amakhala pa ntchito m'moyo wanuwo angakhale inuyo simukudziwa iye, kapena kumkonda iye.

Kusafuna kuphunzira chomwe Mulungu ali kungathe kubweretsa imfa zauzimu m'moyo mwanu zomwe zimapangitsa kulekanitsidwa ndi iye amene anakulengani inu. Ngati inu muli osiyana ndi zochita za Mulungu (mwachitsanzo mukusankha kumunyanjala iye), Kapena ngati mwasankha kutsutsana naye mwamachitidwe anu (mwachitsanzo kunkana iye) zonse za izi zingathe kubweretsa chilekano ndi Mulungu ndipo simudzatha kudziwa mapulani ake pa moyo wanu.

Ngati tivomereza Mulungu pamodzi ndi Mau ake tidzayamba kapeza nzeru ndi chidziwitso zomwe iye amafuna pa iye.⁶⁰ Ndi mphatso yaulele, koma tiyenera kuvomeleza ifeyo mphatso yakeyo. Tikuyenera kuvomereza ifeyo mphatso yakeyo. Tikuyenera kumuitanira iye m'mitima yathu kotero kuti iye athe kudzionetsera (kudziulura) yekha kwa ife.

TIYENERA KUPHUNZIRA KUZINDIKIRA LIU LA MULUNGU

Koma kudziwa Mulungu, kumd'ziwitsitsadi iye, tikuyenera choyambirira kuzindikira liu lake. Tikuyenera kuzindikira liu lake chifukwa woipayo adzachita chotheke chirichonse kuti atilande liu la Mulungu. Satana ndi katakwe pa kusokoneza chomwe Mulungu akuyesera kuuzani in. tangoyerekezani kuyesera kuchita chinachake chomwe chikukweza chokonzero cha Mulungu pa Moyo wanu ndipo mudzaona momwe satana adzachitire pa kukusokonezani, kukusokeretsani komanso kukuphophonyetsani ndikukutembenezani kukuchotsani kukumvetsera liu la Mulungu. Mukuona kodi, satana amafuna kuti inu mukhalebe mbuli ku chikonzero cha Mulungu pa moyo wanu komanso cholowa chomwe chomwe ali nao pa inu. Satana ndiwotsutsana nthawi zomwe ndi chikonzero cha Mulungu ndipo iye amafuna kuti wina aliyense amene walengedwa m'chifanizo cha Mulungu akaonongeke.⁶³

Satana adzafunitsitsa kufuna kuononga Mulungu, koma sadzachita izi (sadzatha), choncho wina woti athane naye ndiye inuyo, ndi ine satana amadziwa kuti ngati sangathe kumpanga Mulungu kukhala wachisoni ndipo satana akugwira ntchito usiku ndi usana kuchita zimenezi. Tangomvetserani nkhani pa maulesi anu ndipo mudzamva zoopsa zomwe zikuchitika m'dziko lapansi, ndipo mudzatsimikizadi kuti akugwiradi ntchito. Tsiku lina, satana pamodzi ndi amithenga ake onse adzathedwa psiti, koma pakadli pano ali ndi ufulu wolamulira ndipo akuwonongadi anthu kuzungulira pa dziko lapansi, mwapang'ono pang'ono. Komatu izi sizinayenere kukhala motero. Ife tikungoyenera kukhala wozindikira machenjerero ake. Tikuyenera kukhala a nzeru zinyengo zake, ndipo tisoweke kuphunzira momwe tingapewere maenje a satana omwe aikidwa m't'sogolo mwathu.

Umodzi wa mizimu ya Satana m'ngero wakugwa, anayesera kusokoneza Yesu tsiku lina pamene Yesuyo anali kulalikira m'sunagoge.⁶⁴ Ngati satana adzayesera kusokoneza Yesu m'sunagoge muja, ndithu adzayesera kukusokonezani pamene inu mukuyesera kuphunzira chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu, choncho, khalani tcheru. Tonse tikuyenera kuphunzira kuzindikira liu la Mulungu mofanana ndi momwe timamvera liu la munthu mzathu. Tikuyeneranso kuphunzira kuzindikira zisokeretso za woipayo. Pamene tidzazindikira zisokonezo zake, tidzatha kutchinga chifuniro cha Mulungu pa moyo wathu wapang'onopang'ono. Tatsekani TV, tatsekani mawailesi anu, Ikani panso zowerenga (magazini) zanu, khalani ndi nthawi yophunzira Baibulo pa inu

nokha ndipo mukhale kumetsetsa zoterezi. Ndithu inu mudzadabwitsika kwakukulu.

Satana alibe mphamvu zeni zeni

Kodi mumadziwa kuti Satana sangakhonzedi kukuonongani? Iyetu alibe mphamvu zeni zeni painu kupatulapo kungokunyengani. Iye ali ngati mkango wobuma umene ulibe mano kapena dzala zokandilira. Nkango wongobangula ndikuoipseza koma wopanda mano ndi zikadabo uyenera kukunamizani inu kuti mudzikhulupilira kuti ulidi ndi mphamvu zeni zeni satana ayenera kudalira pa zinyengo kuti athe kukwanilitsa zilinga zake. Iye ngati angakwanitse kukunyengani ndikupotozera kulowa mnjira zake zooneka zokongola zozungulidwa ndi zosangalatsa zokukopani uku ndi uku (zokonzedwa kuti zikuchotseni maso anu pa mseu womwe mukuyendamo) iye amadziwa kuti inu mungathe kuphonya zikwangwani za machenjezo za mulungu ndi kugwera m'maenje ake omwe akonzedwa kuti akuonongeni inu. Ngati titangokhala kuti ndife a nzeru ku zinyengo za satana ndiye kuti sitidzanyengedwa moyo wathu ndi chidziwitso chokwanira zomwe zikwangwani za machenjezo a Mulungu (monga mau a Mulungu) zakonzedwa kuti zitisogolere ndikutipewetsa kulowa m'maenje, zomwe zidzatipanje ife kukhala molingana ndi chifuniro chake.⁶⁵

Ambiri aife takumanapo ndi zinyengo za satana maso ndi maso. Tinanyengedwapo ndipo tinapanga zisankho zolakwika-ndipo pambuyo pake tinayenera kulipira mtengo wa kusankha kwathu kolakwikako.⁶⁶ Ndizomvetsa chisoni koma zimachitika ndithu. Nthawi zambiri izi zimachitika chifukwa tinamizidwa ndi mau monga ukudziwa m'bale". Sipadzakhala choipa chilichonse ai" Satana amadziwa kufooka kwathu ndiponso kuperewera kwa maganizo athu. Iye amadziwa kuti ife sitingathe kudziwa zomwe tidzakumane nazo; timapanga ziganizo zolakwika, timavulala, ndipo zotsatira zake osathanso kumvetsa pamapeto pake chifukwa chani zinthu zafika potero. Nthawi zambiri timavulala chifukwa tsiku lina tinanyalanyaza kutsatira machenjezo a Mulungu. Tinali mbuli pa ziphunzitsa za Mulungu. Satana amakondwera nako kupulikira kotereku. Zimampatsa iye machiri (mphamvu) kuti azizichita.

Satana amagwiritsa ntchito njira zonse zothekera

Satana angathe kutinyenga ife pogwiritsa ntchito njira zonse zomwe iye angathe kuphatikizapo ma wailesi, TV, Intaneti, nyuzi pepala, magazine, ndiponso ngakhale abwenzi komanso amzathu. Kodi ngati timamvetsera kwa iye ndikumaona ngati zonyengerera zakezo nzabwino, koposa kotani nanga, kukhala womvetsera ku liu la Atate wakumwamba? Tiyenera nthawi zonse kumadziyeza zonse zomwe ife tamva, tawerenga ndi kuona molingana ndi mau a Mulungu.⁶⁷ Kunena zoonza izi nzofunikira kwambiri. Pkupita pa nthawi tidzayamba kuyesa (kuika pa muyeso) Uthenga uliwonse womwe tamva ndi kuona molingana ndi Mau a Mulungu. Tikatero, ndi ulamuliro komanso

kutsikimizika mtima tidzakhala othekera kulankhula, “Chabwino, satana, ndikudziwa machenjerero ako, ndipo ine sindipita kumeneko. Ndikuona Maenje ako, komanso ndikudziwa zomwe Ambuye akunena - choncho ndikuongolera chiongolero change mozemba dzenje lakolo. Mwina ungather kupeza anthu ena, koma ine ndekha sundipeza ai.”

Pali chitetezo chimodzi chokha basi

Kodi mukuganiza kuti Mulungu amakhala pambali pathu pamene satana akubangula mauthenga ake achinyengo kwa ife ndipo Mulungu ndikungokhala chete? Sichoncho ai⁶⁸ Mulungu nthawi zonse amakhala akutiguguda m’chitira umboni ku choonadi chake.⁶⁹ Ngati tingatenge nthawi yathu ndikumvetsera-Mau a Mulungu pamodzi ndichoonadi chake zidzapyoza m’chikumbumtima chathu. Koma tiyenera kukhala ochenjera chifukwa mauthenga asatana nthawi zonse ngosakhazikika. Ngati tingathe kuyamba kuzindikira kuti mauthenga ena Sali monga mwa choonadi cha Mulungu ndiye kuti tidzakhala nacho chitsikimizo cha kunena kuti ai ku mauthenga amenewo, ndipo moterotidzakhala othekera kuwongelera chiongolero chathu mopewa maenje a Satana.

Ndikofunikira kwambiri kuzindikira kuti anthu enanso, angakhale ena mwa abwenzi athu apamtima kwambiri, angathe kupangitsa chisokonezo chachikuru pamene ife tayamba kuphunzira zambiri zachoonadi cha Mulungu. Kutimamatira kwaoko. Tchimo ndi tchimo ndithu ndipo palibe m’modzi wa abwenzi anuwo (monga maganizo awo) angathe kusintha chimenechi. Musalore kuti kukopakopa kwa abwenzi anu kuyesere kukusinthani inu kuti aa-palibe vuto poti “wina aliyense akuchita zoterezi” sichoncho ai. Werengani malangizo ku mayambiro a bukuli. Mulungu samasintha ai.

TONSE TIRI NDI MADONTHO AKUDA M’MITIMA MWATHU

Mwatsoka, tchimo ndi phunziro lovuta kwambiri ndipo anthu ambiri samafuna kulankhula za ilo. Sitimafuna kuona kuti talakwa kapena kuona kutsutsika kapena kuona kuipa zokhudza momwe ife tikukhalira m’moyo wathu. Tikusowekera kudziwa kuti kodi tchimo ndi chani, kuti tchimo ndi madera ati amoyo wathu omwe sakulingana ndi malamulo a Mulungu ndipo, tiyenera kufunitsitsa kusintha madera amenewo.

Khristu ndiwofunitsitsa kuchotsa tchimo m’moyo wathu wonse pa zolingalira za abwenzi athu (anzathu) m’malo moika moyo wathunso pa chomwe Baibulo likunena ndiye tidzaphonyana ndi madalitso eni eni pamodzi ndikukonderedwa zomwe Mulungu anazikonzeratu pa ife. Mzimu wa Mulungu wokhala mkati mwathu adzakhala akusanthula, kutsitsa, ndipo adzatithangata ife kumva iyepamene alikunena kw aife timve, timvedi mwa mve mve mve, tiyenera kukhala omvetsera. Kodi inu mukumvetsera? Kuti mumvetsera ku machenjezo a Mulungu muyenera kupita pa malo pomwe satana sangathe kukusokonezani.

Mukuyenera kudziyanyitsa ndi dziko lapansi kwa kanthawi, dziko lomwe liri mu ulamuliro wa satana.

Mulungu amafuna mtima wathu wonse

Mulungu amalankhula kwa ife ndi cholinga chimodzi. Iye amafunitsitsa kutenga mtima wanu wonse, kukuthandizani inu kuononga zilakolako zonse, Mafano onse, kudzikonda konse, ndikukuthandizani inu kuchotsa machismo onse m'moyo wanu kotero kuti athe kukudalitsani, kukupatsani kukonderedwa, komanso kukupantsani inu mphotho.⁷⁰

Ngati inu mufuna kumva liu la Mulungu komanso chitsogozo chake muyenera kukhala wofunitsitsa kukhala ndi mtima wanu woyeretsedwa. “ichi ndicho chomwe iye amafuna komanso kusowa kuchokera kwa ife, kulapa machismo athu onse ndikumtsata iye. Choonadi chake chonse chochuruka chinapangidwa kuti chititeteze ife. Choonadi chake chimenechi ndizo zikwangwani zamachenjezo zomwe zidatiteteza ife ku maenje ambiri a satana.

DZIKO LATHULI LIKULAMULILIDWA NDI SATANA

Kodi inu mukudziwa kuti Mulungu amafuna kuti inu mudziwe chifuniro chake.⁷² Iye amafunadi kutero, koma izi zidzatengera inuyo kusintha - kusintha m'maganizidwe anu komanso momwe inuyo mumamvetsera ndinso kutsatira ndinso kutsatira Mau ake. Dziko lomwe tikukhalamoli likulamulilidwa ndi satana Izi zikutanthauza kuti zochuruka za zomwe inu mamamva komanso kuona siziri zolingana ndi ndondomeko za Mulungu. Ochuruka a mauthenga omwe inu mumawamva tsiku ndi tsiku akonzedwa kuti inu musocheretsedwe nao; awa ndiwo machitidwe a satana otsatira malonda ake. Ndipo iye ndiwaluso kwambiri pa zomwe amachita.

Mulungu wapatsa ulamuliro kwa satana kudziko lino lapansi kufikira chimaliziro.^{73 74} Pamene satana adzamangidwa ndi kuponyedwa ku gehena kwa nthawi zamuyaya. Koma kufikira nthawi imeneyo tiyenera kukhala anzeru ndipo tiyenera kukhala osandulika⁷⁵ kotero kuti tikathe kuzindikira machenjerero ochuruka a satana. Kumbukirani, satana nthawi zonse akufunafuna anthu mosalekeza kuti awaononge.⁷⁶ Iye ndi wochenjera kwambiri kotero amayeserera ngakhale kunyenga ndi aphunzitsi a Baibulo omwe.⁷⁷ Koma Mulungu akutizonjeza ife kuti adzatiteteza ndiponso kutilangiza ndi kutitsogolera ife.⁷⁸ Ndipo adzatitsogolera m'njira yolondola -kutipewetsa maenje onse a satana-ngati ifeyo tidzamtatira iye. Izi zidzafunikira kuti ifeyo tiphunzire Baibulo (mau ake) kotero kuti tingathe kupanga ziganizo zomwe ziri zogwirizana ndi chifuniro chake.

KHALANI ANZERU MONGA ANA ANKHOSA

Mulungu sadzakutsolerani mpang'ono pomwe kulowa mnyengo yomwe idzakuphwanyitsani ndondomeko zake - monga ngati kudzivulaza nokha, kapena kuvulaza ena. Ngati inu muphonzira Mau a Mulungu mudzakhoza kukhala okonzeka kupewa maenje omwe ali mtsogolo mwanu. Tidzakhalabe m'mazunzo ngati sitidzatha kuzindikira liu la Mulungu. Kumbukirani kuti ana ankhosa ndi omwe amazindikira liu la m'busa wao ndipo amatha kutsatira liu limenelo. Ana a nkhosa ndi omwe amamva liu lomwe salidziwa -amadziwa kuti sayenera kulitsatira liu limenelo. Amadziwa kuti liu lachilendo sichitetezo chao ai. Tikuyenera kuyetseta kukhala anzeru monga ana ankhosa. Tatembenukani muzungulire ndikuyenda njira ina.

Nazi zinthu zina zomwe Mulungu akufuna kuti inu muzidziwe;

- Iye adzakupatsani nzeru ngati mudzampempha ndikukhulupirira kuti iyeyo angakupatseni inu.⁷⁹
- Iye ali ndi pulani pa moyo wanu.⁸⁰
- Chifuniro cha Mulungu ndichakuti inu mukhale ndi ubale ndi iye kupyolera mwa mwana wake.⁸¹
- Lemekezani Mulungu ndipo khulupilirani mwa iye kotero kuti iye athe kudzivumbulutsa yekha kwa inu.⁸²

Monga momwe mumvera liu la mulungu ndikulizindikira ilo, muyenera kukhala ofunitsitsa kusintha njira pamene iye ali kukutsogolerani.⁸³

MUTU 2

Ndinapangidwa - m'chifanizo cha Mulungu

Mulungu ankadziwa chomwe iye ankachita

Onse anali pomwepo

Pachiyambi Mulungu anati, “Tipange munthu m’chifaniziro chathu.”⁸⁴ Kodi munayamba mwaona mau oti “ife” ndiponso “chathu” mndime imeneyi? Mukuganiza kuti “ife” ndi “chathu” amenewa ndi ndani? Izi tizifotokoza mozama bwino lomwe mtsogolo muno, koma “ife” ndi chathu” amenewa ndiwo 1. Mulungu Atate, 2 Mwana wa Mulungu, yemwe ndi yesu ndi 3 Mzimu woyera wa Mulungu.

Pamene Mulungu amkati ‘Tipange munthu m’chifanizo chathu” - izi zikutanthauza kuti Mulungu Atate, Yesu ndi Mzimu woyera wa Mulungu onse anali pomwepo pamene munthu anali kupangidwa.⁸⁵ Inde, ngakhale yesu anali pomwepo. Yesu anali pomwepo pamene kumwamba ndi dziko lapansi zinali kulengedwa,⁸⁶ ndiponso. Yesu anali pomwepo pamene dziko lapansi linali kuumbidwa.⁸⁹ Ndiponso inde, Yesu anali pomwepo pamene m’malo mwake pachiyambi cha nthawi chakugonjetsa tchimo ndi zoipa.

Mulungu amkadziwa chomwe iye ankachita. Chikonzero chake chinali chidakali. M'malo mwake kale pamene Adamu adachimwa m'munda muja wa Edeni-ndipo Yesu anali pakatikati penipeni ku chikonzero chimenecho.

Cholengedwa chopambana koposa

Choncho tinapangidwa motani m'chifanizo cha Mulungu? Kodi timaoneka mofanana ndi iye, Kapena kodi tikufanana ndi iye mumzimu? Baibulo limanena kuti tonse tanyamula chifanizo cha Mulungu mkati mwathu.

Tayang'ana mofatsa bwino pa gala si (kalilore) kwa kamphindi. Kodi mungathe kuyamba ngakhale kulingalira momwe munapangidwira modabwitsa? Inu sicholengedwa chobwerera mwadzidzidzi ai, kapena chinachake chofanana ndi nyama ai. Ndinu cholengedwa chomwe ndichachikuru komanso chopangidwa modabwitsa.⁸⁸ Chopambana kwambirimwa zolengedwa zonse komanso chionetsero chapaderadera cha chikhalidwe cha Mulungu wake. Inu ndi cholengedwa chopambana koposa chomwe ndi mphatso yaikuru kwambiri yochokera kwa Mulungu. Mulungu anakudziwani inu musanabadwe ndipo iye anakonzeratu kuti inuyo mulengedwe m'nchikwalidwe cha mwana wake Yesu.⁹⁰

Komatu izi sizitanthauza kuti ifeyo munga anthu chikhalidwe china chili chonse cha zomwe Mulungu ali munga kukhala wamphamvu zonse, wodziwa zonse, kapena wopezeka paliponse ai. Ndife okhala ndi malire m'mpamvu zathu komabe tiri nako kufanana kwa umulungu m'madera ambiri. Tiyeni tiunike ena mwa madera amenewa -

1. M'zimu

Mulungu ndi mzimu - zomwe zikutanthauza kuti Mulungu ndiosaneke. Pamene Baibulo likunena kuti ife tinalengedwa m'chifanizo cha Mulungu likutanthauza kuti ife tinapatsidwa mzimu. Sizitanthauza kuti Mulungu ndi chinthu chathupi ai, kapena kuti ndife ofanana ndi Mulungu m'chikhalidwe chathupi. Kodi mumkadziwa kuti thupi lanulo longokhala nyumba chabe yokhalamo moyo ndi mzimu wanu. zomwe ndi inuyo weniweni? Mulungu analenga thupi lanu la umunthulo kuti moyo wanu udzikhalamo kufikira nthawi yakuti thupi lanu la umunthulo lidzafa.

Mkati mwathupi lanu Mulungu anaikamo zonse za zigawo zodabwitsa zokhala ndi ntchito zenizeni ndipo kuti chigawo chirichonse chimadziwa bwino lomwe chomwe chikuyenera kuchita. Thupi lanulo linapangidwa ndi maselo (cells) pafupipafupi 100,000,000,000,000 (trillion cells) ndipo selo iliyonse ya amenewa inaumbidwa pamodzi kuti igwire ntchito mogwirizana ndi ina ndi mzake. Tangoganizanzirani chinthu china chirichonse chokhala ndi zinthu 100 thiriliyoni koma chogwira ntchito ngati chinthu chimodzi? Ngakhale makina (machine) opangidwa mwa pamwamba amangokhala ndi

magawo ochitachita 500 okha ndipo zinawatengera akatswiri oposera dzana limodzi kuti akhonze makinawa mzaka dzana limodzi. Thupi lanulo ndi chozizwa chachikulu ndipo simungadzimvetsetse kuti maselo anu okwanira 100 triliyoniyo mwa ali ndikuthekera kogwira ntchito mogwirizana kwa wina ndi mzake- mwa kuthekera kwao.

Kodi maselo 100 triliyoni m'nthupi mwanu amakwanitsa bwanji. Kugwilira ntchito pamodzi ndipo pambuyo pake ndikutumiza nkhani zao ku ziwalo zina za m'thupi mwanu?

Maso anu amdziwa bwanji momwe angaonere-ndi kuwala komanso mitundu mitundu yazinthu zooneka mwaukadaulo-ndipo kenako kukalumikizitsa uthengawu ndi makutu anu komanso bongo wanu kuti mikono ndi miyendo yanu ziyambe kuchitachita?

Kodi mphuno zanu zimadziwa bwanji kununkhiza- ndikuthekera kodziwa kusiyanyitsa fungo loipa ndi labwino-ndipo pa mbuyo pake ndikuwalumikizitsa mafungo amenewa ku bongo wanu wodziwitsa chokoma kapena chowana kuti inu mukathe kudzionza zonsezi mosiyana?

Kodi bongo wanu umadziwa bwanji kulenga zinthu, kuchitira chifundo, kumva chimwemwe, kutsutsika kupsa mtima ndikukhala nako kumva kukhumudwa kapena kukonda wina? Munthu sangathe ngakhale kulenga moyo nanga koposa kotani kulenga chinthu china chomwe chimafunikira kulumikizitsa zinthu zoposa mabiliyoni kapena matiriliyoni kuti munthu munthu umve machitachita a mthupimu (feeling).

Inu ndi dongosolo lapamwamba kwambiri komanso losatheka kulimvetsetsa lomwe ndilosafanana ndi cholengedwa chilichonse - ndipo nkovuta kuganizira kuti chilengedwe chonga ichi chinachitika popanda wodongosola zonsezi (popanda mlengi).

Tangotengani chimodzi chokha cha zinthu izi (mwachitsanzo kuona kununkhiza, kumva, kulawa, kukhudza) ndi kudziyerekeza monena kuti china chirichonse cha zinthu zimenezi tingathe kudzipenekera kuti mwina zinalengedwa mwamwai (zinangopezeka mosayembekezera) - ai mpang'ono pomwe sizingatheke kutero. Ndipo muli nazo zikwi zochuruka za magawo odabwitsa ngati amenewa m'nthupi mwanumo, chirichonse cha zimenezi chiri ndi mapangidwe odabwitsa kwambiri komanso osamvetsetseka.

Ndipo pano pali chomwe chiri chinthu chodabwitsa kwambiri pa zokhudza mfundo imeneyi: Mulungu analenga yense waife m'chikhalidwe chofanana cha thupi kuti tsiku lina lake iye adzakhoza.

Chikhaliidwe chotere cha uthupi momwe adzatsankhe kudzivumbulutsamo iye mwini. Pano pa dziko lapansi.⁹² Ndi m'thupi m'mene mu momwe adzadzere pobwera pansu pano kudzakhala pakati pathu, ndipo pambuyo pake kudzatifera ife kutipulumutsa ku zochimwa zathu. Linali thupi lake la umunthu longa lathuli, lokhala nazo zonse zomwe tatchula pamwamba mkati mwache - lomwe linali loti lidzalasidwe chifukwa cha zolakwa zathu.⁹³

2. Mtima - Machitachita amkati mwanu ndi zochitika zam'nthupi lanu.

Mulungu anaika kanthu kena kake m'moyo mwanu pamene anakulengani inu. Iye anakupatsani inu mtima. Sitikunena za mtima womwe umapopa magari anu ai. Tikunena za mtima umene umakupangitsani inu kukhala othejera kumva, kuganiza ndi kukhulupilira zinthu mkati mwanu. Mulungu anakupatsani inu mtima kuti muzitha kukhala ndi chikondi, chifundo komanso zina zambiri zikwi zikwi. Iye anakupatsani zonsezi kuti kuteri mukathe kumumvetsetsa bwino chomwe iye ali. Mulungu amafunitsitsa kuti inu mukhale ozindikira bwino malingaliro a mtima wake. Mulungu anakupatsani inu kuthejera komva zinthu mkati mwanu zofanana ndi zomwe amazimva iye mkati mwake; amafuna kuti inu mudzikonda zinthu zimene iye amakonda ndiponso kudana ndi zomwe iye amadana nazo. Mulungu amafuna kuti inu mudzimukonda ndi mtima wanu wonse, moyo wanu wonse, ndiponso nzeru zanu zonse.⁹⁴ Ichi ndiye chifukwa chomwe iye anakulengani inu monga mwa chifanizo chake ndiponso ichi ndichifukwa chomwe iye anakupatsani inu mtima.

3. Maubale komanso chiyanjano

Mlengi wathu anatilenganso ife kuti tikhale pa ubale ndi iye. Mulungu amafuna kukhala pa ubale wabwino komanso watanthauzo ndi yense waiye olengedwa ake. Nkhani yabwino ndiyoti, tonse tingathe kutero-koma wina ali yense wa ife ayenera kusankha kukhala ndi ubale umenewu. Mulungu sadzakakamiza munthu ai. Iye sadzaumiliza kuti alowe mumtima wamunthu kapena kukukakamizani kuti alowe mu mtima mwanu ai. Ngati iye angakakamize kuti alowe mwa inu, ndiye sungakhale ubale ai. Iye adzagogoda pa chitseko cha mtima wanu, ndipo adzadikilira. Sadzagweramo mwadzidzidzi ai, chifukwa iye ndiwofatsa ndi wodekha. Adzadikilira kufikira inuyo mumulore alowe. Iye amadziwa bwino lomwe kuti inuyo munakonzedwa komanso kulengedwa kuti mukam'dziwe iye chomwe ali. Koma ndi chisankho chanu kutero kapena ai. Mungathe kutsegula chitseko ndikumulora iye alowe kapenansomungathe kusankha kusungula chitseko chanu chotseka. Mungathe kuvomera kuitana kwake, kapena mungathe kulolera kuti mwakunyada kwanu iye akhale kunja. Mungathe kusankha kuphunzira kuti mudziwe kuti iye ndi ndani kapena mungathe kumakhalabe mu umbuli wa chomwe iyeyo ali. Koma nkhani yaikulu ndiyoti ichi ndi chisankho chanu, chifukwa inu munapatsidwa kukhala ndi ufulu

wosankha chifuniro chanu (ichi ndi chimodzi cha zikhalidwe zazikulu kwambiri zoikika m'nthupi mwanu komanso zodziwika monga “chisankho”). Mumafunikira kuti muchite chiganizo inuyo panokha.

Pamene iye agogoda pa khomo la mtima wanu, ndiye kuti amayembekezera kuti inuyo mudzamulora kuti iye alowe kotero kuti iye alowe kotero kuti akathe kukuuzani komwe inu mukulowera. Iye amakhala ndi ulendo wopambana kwambiri wokonzekeredwa bwino. Koma ndi pokhapokha inu mudzatsegulira mtima wanu, apo ai simudzatha kuphunzira komwe iyeyo ulendo wakewo udzapita nanu. Uwu ndi ulendo womwe kothera kwake simukuyenera kuphonyana nako. Mtsogolo mwake m'bukuli mndzatha kumvetsetsa bwino chifukwa chomwe Mulungu anakupatsani zisankho zopambana zonga izi kuti inuyo mukhale ndi mwayi wosankha.

4. Ufulu wochita zomwe ufuna

Mulungu amavomereza munthu wina aliyense kusankha njira ya iye mwini ndikupanga maganizo a iwo eni. Ichi chimatchedwa “ufulu wachifuniro” Monga tamva pachiyambi, satana anagwiritsa ntchito ufulu wachifuniro umenewu kupandukira Mulungu. Ifenso tonse tapatsidwa chisankho chofanana chomwechi. Tingathe kutsatira njira ya Mulungu (Mwachitsanzo ndondomeko za mulungu, zomwe zinakonzedwa kuti zititetezere ife) kapena tingathe kutsata njira zaife eni. Ngati ife sitingakhoze kumsata Mulungu m'njira zake tisayembekezere chitetezero chake. Iye adzatilora kutitute zomwe ifeyo tafetsa-kutanthauza kuti iye adzalola kuti ife tizunzike ndi zotsatira za zomwe ifeyo tinasankha.

Ngati inu simutsatira kuunika kwake njira yomwe mudzatenge ingathe kubwera mdima waukulu mofulumira. Mungathe kutsogoleredwa kulowa m'malo momwe inu mudzatha kuvulalamo. Kudzakhala monga ngati kulowa m'dzenje. Kuyenda kwanu kolowa m'ndzenje kumazimira mumdima pa sitepe iliyonse yomwe inu mungatenge. Popanda kuunika kwake mwina inusimungathe kuona miyala ndizitsa pa njira yanu choncho mungathe kupunthwa, Popanda kuunika kwake kudzakhala kovuta kuti inu muone zisonga ndi zobaya choncho mungathe kulasidwa ndikuvulala. Mwina simudzatha kuona malo okhota komanso mphambano za njira motero mungathe kugwa. Ngati mungakhoze kupitilira ndi ulendo woterewu ndikuomba china chake choopsa (monga wina wakekukunyengererani kuti mumwe mankhwala ozunguza bongo) mudzatha kuvulala, ndiponso mwina mwake kufa kumene. Satana adzagwiritsa ntchito machenjerero a mtundu uliwonse kuti akukopeni inu kutsata njira yake, ndipo ngati angakwanitse kugwiritsa ntchito azimzanu kuti akuthandizileni kukopeka ndi kunyengeka ndithu iye adzagwiritsadi ntchito gawo limenelo. Satana ndi bwenzi la mdima ndithu.

Koma njira ya Mulungu ndi yowala. Mudzakhala othechera kuona kuunika kwa Mulungu ngakhale mutayenda kotalika bwanji. Kutsatira kuunika kwa Mulungu kudzakutulutsani inu mu m'dima mwansanga kunena zoonza, ngati mukumva kutaika ndipo mwavomereza Yesu monga mtsogoleri wa moyo wanu, mungathe kubwezeretsedwa m'njira yake yowala pompompomo. Kuunika kwa kuwala kwake kunakonzedwa kuti kukupulumutsani inu, ndipo kupulumutsa kumeneku iye adzakuchitadi.

Mulungu anakupatsani inu ufulu wochita chifuniro kotero kuti inu mukathe kusankha kumvera iye kapena ai, Mulungu sanafune kulenga chiloboti chomwe nthawi zonse chidzamvere malamulo ake. Iye samafuna kuumiriza chifuniro chake pa wina aliyense ai. Pamene iye akuyeselera kukufikirani inu kuti mupange naye ubale, inuyo ndi amene mukuyenera kuvomereza kuitana kwakeko. Kuitana kwake nthawi zonse kumadikira mayankhidwe anu. Iye akukuitanirani inu moyo wosatha. Koma funso lalikuru ndiloti, kodi inuyo mudzasankha kumtsata iye kapena mudzasankha kutenga njira yanu yanu njira yomwe idzakutsogolerani inu kupita kumalo ena ake oopsa-zonse ziri ndi inukusaankha. Mulungu ndi satana yemwe, onsewa akudikira chiganizo chanu.

Tonse tiyenera kusankha kutsatira kapena kukana Mulungu. Kusapanga chiganizo-ndiye kupanga chiganizoko. Musakhulupilire kuti mungathe kungochedwetsa chiganizo chanucho ai. Kuchedwako ndiye kukanako. Pachimaliziro mulungu adzaweruzana munthu wina aliyense yemwe akukana Mau ake chifukwa Mulungu analenga munthu chifukwa cha iye mwini. Tingathe kusankha njira yake ya Kuunika, kapena tingathe kusankha njira yam'dima. Mulungu adzadikira mofatsa kuti mupange chiganizo chanu. Koma musadikire nthawi yaitali popeza nthawi yanu ya moyo wanu wa panso pano ungather kutha nthawi ina iriyonse.

Onetsetsani kuti mwawerenga mutu 5 m'buku lino ndipo pangani chiganizo. Ngati mutsiliza kuwerenga buku lino ndipo simunapange chiganizo, ndiye kuti mwapanga ndithu chiganizo.

5. Chikumbumtima ndi Chidziwitso

Inu munapatsidwa nzeru yomwe ndiyopambana kuposa nyama ina iliyonse, ndiponso munaikidwira maganizi omwe ndi othechera kumvetsetsa (kuzindikira) zinthu. Koma pamene chidziwitso cha Mulungu chiri chopanda malire,^{95 96} inu muli ndi malirem'chidziwitso chanu.⁹⁷ Pamenenso nyama zimangochitika zinthu molota ndi modzidzimuka, inuyo ndiothechera kupanga ndikulingalira bwino chitsogolo.

Baibulo limafotokoza kuti tonse aife tiri nacho chidziwitso cha zabwino ndi zoipa choikidwa m'mitima mwathu.⁹⁸ Mwina mwakenso kuthekera kwathu kozindikira chomwe chiri chabwino ndi chomwe chiri choipa chikuonetsera bwino kwambiri momwe ife takhalira ofanana ndi Mulungu. Chimodzimodzi monga pali dongosolo loyendetsera chilengedwe chonse, palinso madongosolo omwe amayendetsa (amayang'anira) chichikhalidwe chathu komanso maganizidwe athu.

Mphatso za maluso anthu zimaonekera kupyolera m'kuthekera kwathu kodziwa kupanga mapulani, kumanga kulemba komanso kukonga zinthu kudzapanga tokha kukhala oyenerera kusankha kuganiza kuseka kukongoletsa chinthu china chake komanso zina zambiri. Ambiri. Aliyense wa ife ali nao mitundu yosiyanasiyana ya nzeru imeneyi, ndipo wina aliyensenso ayenera kukuza mphamvu yake yakaganizidwe komanso kusinkhasinkha modzaza Koma, angakhale mwa chidziwitso chathu komanso nzeru zathu zonse, tiri nazonso zofooka zazikulu.

Mwachitsanzo kulephera kudyetsa chiwerengero cha anthu onse okhala m'dziko lapansi mopanda kulimbana, kusatha kumvetsetsana pa kusiyana kwa zikhalidwe ndi miyambo yathu, ndiponso kulephera kubweretsa mtendere pa dziko. Chifukwa cha kulephera konseku ndicho-chinyengo. Dziko lanyengedwa ndithu. Wonyenga wamkulu akunyenga anthu nthawi ndi nthawi kuti iwo safunikira kutsatira Mulungu ai. Ndipo mwatsoka lake, anthu ochuruka ku dziko lonse lapansi amamvetsera kwa Wonyenga Wamkuru ameneyu. Iyeyu ali pena paliponse, m'njira zonse zamalumikizandwe, msukuru zonse, ndiponso ngakhale m'mipingo yathu pamodzi ndi malo ena onse a chipembedzo. Palibe malire ena alionse komwe wonyenga Wamkuluyu sangayesere kunyenga anthu.

6. Chilengedwe chonse

Tangoyang'anani mozungulira dzikoli. Tayang'anani pa zinthu zonse zomwe Mulungu wadzilenga padziko lapansi, m'nyanja, pamodzi ndi m'mwamba⁹⁹
^{100 101 102.} Komanso tayang'anani mozungulira ndipo muone zinthu zodabwitsa zomwe munthu wapanga panso pano. Ndidzachidziwikire ndithu kuti munthu ndi waluntha lolenga.

Tayang'anani muone msomba zokongola m'nyanja zathu. Mulungu Sali waluso kokha ai, komanso wanseru zozama. Muli msomba zina m'nyanja zomwe zimadalira pansomba zina ndiponso zomera kuti zikhale ndi moyo.izo ziri ndi ubale wodabwitsa kwambiri. Kodi zina pezana wina ndi mzake motani-zisanafike polekana?

Nanga bwanji zokhuza kambalame kaja kobadwira m'madera aku Nyanja ya Arctic yomwe imakhala ndi chidziwitso chodziwa kuuluka mamailosi zikwi zambiri pamwamba pa Nyanja imeneyi kupita kuti ikapeze ka chisumbu (island) ku mpoto kwa Nyanja ya Pacific komwe siinafiikeko ndi kale lonse.

Kuti ikamangeko chisa chake? Ngati itangophonya pang'ono chabe mu ulendo wakewo ndikusochera ndiye kuti siingakhalenso ndi mphamvu yoti ibwere kupita komwe yachokera. Komatu kambalame kameneka kamakhoza bwino lomwe.

Nanga njira ija yomwe imabadwa kufupi ndi equator (ikweta) ndipo pang'ono pokha imadziwa kuuluka mozungulira Nyanja yonse ya Atlantic paulendo wake wofufuza-ndipo patatha zaka zambiri pambuyo pake imakwanitsa kupezanso malo eni eni omwe aja komwe imabadwira paja kuti iikire mazira ake? Izi zikadatha kuyerekezedwa inuyo ndi ine kuyamba kuyenda kuchokera panyumba ku Los Angels, kupita pa nyumba ina ku New York, kenako kubweranso komwe inachokera kuja-popanda kugwiritsa ntchito mapu.

Nanga bwanji zokhudza gulugufe wamkuru uja amene amayamba ngati kamphutsi kakang'ono m'dziko la Canada ndipo pambuyo pake kupyolera n'kusinthika kodabwitsa kwambiri amasinthikiratu motheratu ndikusandulika gulugufe wokongola kwambiri yemwe amadziwa momwe angakulire ulendo wautali kwambiri mamailosi zikwizikwi kakafika mpaka ku Mexico komwe amayenera kupitako kuti akhale ndi moyo. Ngati iye sangathe kufika ku malo ochepachepa amenewa komwe sanayambe wafikako kale lonse-ndiye kuti sangathenso kukhala ndi moyo. Koma iye amakwanitsa ndithu, Agulugufe okwanira 300,000,000 ku dera lonse la kumpoto kwa dziko lapansi molumikizana pamodzi amadziwa kuchita chinthu ichi chofanana-onse obadwira mkati mwachigoba cha mphutsi. Kusinthika kwake m'makhalidwe nkolondola gulugufe wamkuru ameneyu amapatsira zinthu zina zofunikira kukula kwa azinzake kuzera mu imfa yake komanso ndondomeko yake ya kukula m'chigoba cha mphutsi chija.

Pali zitsanzo zikwi zochuruka zofanana ndi izi zomwe sitingathe kudzilongosola. Zonsezi ndi chilengedwe pa mulingo wozama zedi. Kodi zolengedwa zonse zimenezi zikadatha bwanji kumachita zimenezi popanda mlengi? Tonsefe tinalengedwa ndi Mulungu yemwe ndi wolenga wodabwitsa.¹⁰³ Motero, chomwe Mulungu adachita ndikungotipatsa ife kadhontho chabe ka mphamvu ya kulenga kwake. Pa Genesis 1 mau akunena kuti Mulungu adalenga china chilichonse. Pa nthawi iriyonse yomwe iye analenga amkangolankhula mosavuta mau oti. "kukhale...." Ndipo zinkachitikadi. Mulungu amalenga m'kulankhula (ndi mau) mphamvu ya Mulungu yakulenga ndi chinthu chomwe ife tikusokera kuchigwira. Ndipo tingathedi - ngati mphamvu yake yolenga imeneyi yomwe imaturutsa

machiritso, chikhulupiriro, madalitso a m'moyo mwathu, zozizwa, komanso ndi zina zambiri.

7. Nzeru

Nzeru ndi chimodzinso cha makhalidwe omwe tonse Mulungu ndi ife tonse timakhala nao. Anthu ophunzira zokhudza Mulungu amagwiritsa ntchito mochurukira mau oti “Omniscient” polankhula za chidziwitso chopanda malire cha Mulungu. Mulungu amadziwa chirichonse chokhudza chrichonse. Iye amadziwa chomwe ife tikuganiza¹⁰⁴ ndiponso amadziwa chirichonse chomwe chidzachitike.¹⁰⁵ Mulungu sangakonze mapulani oipa chifukwa iye amadziwa mayankho ake¹⁰⁶ Kudziwa zonse kwake kumavomerezana ndi nzeru zake.

Mulungu amatipatsa nzeru¹⁰⁷ koma nzeru zakeyo ndi nzerru za munthu sizofanana ina ndi imzake ai.¹⁰⁸ Nzeru yoona simachokera kwa munthu, imachokera kwa Mulungu.

Mulungu, kuzera mu nzeru zake adzatitengera chomwe iye, analonjeza m'njira zomwe inu ndi ine sitingathe kudzimvetsetsa.¹⁰⁹ Koma inuyo muyenera kumtsata iye kuti muphunzire kuti nzeruyo njotani. Ngati musowa nzeru-Mulungu akuti mupemphe kwa iye.¹⁰⁰ Nzeru, ngati igwiritsidwa ntchito moyenera, ingathe kutipatsa makhalidwe abwino ndiponso ingathe kukhala kuunika kotitsogolera m'moyo mwathu. Nzeru idzakuongolerani inu kukupewetsani maenje a satana. Nzeru imathandiza kupanga zisankho zoyenera. Kukhulupiriro mwa Mulungu ndi Yesu kungathe kukhala chiyambi cha nzeru yanu.

Koma mukhale ochenjera pamene milikupempha nzeru ina chikwa palinso nzeru ina imeneyi njapadziko lapansi, yosakhala yauzimu, komanso yosakhala yauzimu, komanso yaziwanda.¹¹² Tikuyenera kuonetsera nzeru yathu yoona mwa zochita zathu. Kukhala ndi nzeru yoona sizitanthauza kudziwa zabwino ndi zoipa ai, koma kudziwa chabwino kuchokera ku choipa.¹¹³

Kodi munayamba mwadabwitsika chifukwa chomwe sitione ka kukhala womvetsetsa nzeru ya Mulungu pamodzi ndi zinthu zina zoipa zomwe zikuchitika mdziko lathu lero lino? Monga ngati nkondo, njala, ngozi, zogwa mwadzidzidzi, nthenda, imfa pamodzi zisoni zonse kungotchulapo zochepe chabe. Mulungu wazisiya zonse monga chinsinsi.¹¹⁴ Chifukwa nzeru ya Mulungu ndi yaikulu kwambiri kuposa yathu. Iye ali ndi mathero omwe sanathe kuwavumbulitsa ai. Iye samalakalaka kuti uza chifukwa kutero kukadatha kuyalusa chinsinsi chake chosungira chimaliziro. Komanso izi zikadakhocha kuchotsa chikhulupiriro chathu mwa iye. Choncho tiyeni tikhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo tiyeni tilole nzeru yake, osati yathu ai, kuti kuunika kotitsogolera ife panjira yathu.

8. Ulamuliro / Mphamvu

Ifenso tiri ofanana ndi Mulungu mu lingaliro loti tapatsidwa ulamuliro wachifumu. Mulungu ali ndi ulamuliro waukuru pa chilengedwe chonse, ndipo ifenso tapatsidwa ulamuliro wachifumu wonga uwu pa dziko lomwe tikukhalapo.^{115 116} Ulamuliro wamkuru umenewu mwa njira inanso, siwochita kubadwa nao ai, koma ndi mphamvu yopatsidwa ndi Mulungu.¹¹⁷ Monga momwe Mulungu analenga dziko ali monkomera iye, tsopano ndife okhudzidwa (okhala ndi udindo). Pa kayendetsedwe kake. Uwu ndi udindo wopatsidwa kwa ife ndipo sitiyenera kuutengera mwachisawawa ayi. Tsiku lina tizayankha kwa mulunmguyo pa chikhalidwe chomwe ife tili kukhalamo.

9 Chikhalidwe chamuyaya

Mulungu ndiwa muyaya (wosatha) ngati munali musanaone tanthauzo la mawu oti “muyaya” m'buku la mtanthauzira mau (dikishonale) m'mbuyomu, mawu amenewa akutanthauza chopanda chiyambi, ndiponso chimaliziro, kukhala cha muyaya zitanthauza kuti chinthucho chizakhalapo kopanda mathero. Funso lofunika kwa ife tonse ndi ili: kodi litatha kufa thupi lathu! Tidzakhalanso kosatha kumwamba?¹¹⁹ kapena kosatha ku gahena?^{120 121 122} ¹²³ umuyanjan ndi nthawi yaitali kwambiri.

Kuyenera kwathu, komanso kupatulika kwathu

Ngakhale anthu alinazo zikhalidwe zofanana ndi mulungu zomwe tatchulazi wina aliyense wa ife ali ndi kuthekera kodzionesera izo mosiyana ndi nzake. Ichi ndi chifukwa choti chifanizo cha mulungu chinakhazikitsidwa mwa wina yense wa ife wosiyana. Mwaphamvu yakulenga yopanda malire ya mulungu. Palibe zinthu zokopera ayi. Inuyo ndi inu nokha yemwe adzabadwe ndi zikhalidwe (mapangidwe) zosafanana ndi wina aliyense ngati inu muzakhala othejera kukhoza kulandila (kumvetsa) choonadi ichi zomwe chikutanthauza ndiye kuti mudzadabwitsika kwambiri pakuthekera kwake. Inu muli ndi kuthekera koonetsera mzimu wa mulungu, zochita zake, ubale wake, kulenga kwake, ulamuliro wake komanso mphamvu zake za umuyaya, ndiponso muli ndi kuthekera kochita zinthu izi mosiyana ndi mulungu. Tanenani kuti woo!

Mtumwi Paulo akunena kuti ife nthawi zonse tiri m'dongosolo la kusanduluka kukhala chifanizo cha mulungu mwa mau oyera a mulungu ndipo kuti chifanizo chathucho chidzapangidwa chatsopano m'chilungamo chonse komanso chiyero chake!^{124 125}

Anakupangani inu kukhala wapadera-dera komanso wopatulika ndicholinga

Mulungu anakulengani inu

Inde, inu ndiwosiyana ndi wina aliyense. Ndinu wosiyana ndi munthu wina aliyense yemwe anabadwapo m'dziko muno. Ali chikonzero kuyambira pachiyambi kuti zolengedwa zake zonse zizakhale ndi kudzadza m'dziko lapansi¹²⁶ ndipo kuti munthu wina aliyense adzakhale ndi wina komanso wopangidwa modabwitsa ndi moopsa¹²⁷ Inu simunabadwe mwangozi ai. Mulungu anakumbani inu mwatsatanetsane m'mimba mwa amayi anu.¹²⁸ kuchokera pachiyambi pomwe mulungu amafuna inu kuti mukhale wapaderadera pomweponso kukupatsani inu zikhalidwe zina zotengera kuchokera kwa makolo anu. Ichi ndiye chifukwa chomwe inu mulinazo zinthu zina zofanana ndi makolo anu, komanso mwina mwake ngakhalemachitidwe amakhaliidwe awo, ena abwino enanso oipa.

Pamene mulungu anakalenga inu amathyola chiumbidwe chonse. Palibenso munthu wina wofanana ndi inu. Inu ndi "yekhayo" ndipo "m'modzi" basi. Zafotokozedwa m'baibulo kuti iye ndi wumba ndipo ife tinali dongo.¹²⁹ ¹³⁰ ife tinaumbidwa m'manja mwake pacholinga chopatulika ndiponso chapadera-dera,¹³¹ chomwe tsiku lina chidzabvumbulutsidwa. Mulungu anali wokhuzidwa m'chikhalidwe chanu cha umunthu (thupi) komanso chidziwitso chanu-kuyambira pachiyambi pomwe. Iye amadziwiratu matsiku omwe inu mudzakhalendi moyo ndiponso amaziwiratu zokhuza zinthu zomwe muzakumana nawo m'moyo wanu wonse. Iye ali ndi cholinga ndi inu-cholinga cha ulemelero koma kuti zonse zitheke zidzatsowekera kuti inu mukhulupilire. Iye sangavumbulutse cholinga chakechi pa inu mutatsegula mtima wanu ndikumulola iye kuti alowe.

Mumayenera inu kumva chithonhozo mkati mwanu pozindikira kuti mulungu alinazo zonse zanyengo zanu pansu pa ulamuliro wake. Mulungu sangakutengeni inu mbali yake popanda iye kudziwa kuti mukafika komwe mukupita. Ndipo mulunguyo, zenizeni zake ndiyemwe akuyendetsa basiyo. Iye akudziwa bwino lomwe zonse zomwe zizakuchitikirani inu mkati mwa njira izi zikuphatikizapo zonse zabwino komanso zonse zoipa zomwe muzakumana nazo. Molingana ndi dongosolo la mulungu-chirichonse cha zokomana nazozanu zimatengera ubwino wa kukula kwa uzimu.

Inu mwina simungathe kudzimva ngati munapangidwa modabwitsa, komatu ziri choncho ndithu. Mungathe kukhala ndi masiku pomwe inu mungakhale m'masautso ozama kwambiri, ndiponso mukhathe kukhala ndi masiku pomwe inu muli mzokhumudwitsa zazikulu. Moyo siophweka ai. Koma mulungu akufuna kuti mudziwe momwe iye amakukonderani inu ndiponso kuti iye anakulengani inu momwe mulilimo-pacholinga.

Mulungu amadziwa zonse zokhuza inu

Kaya mukukumanandi mdima waukulu motani ndipo zoonadi tonse timakumana ndi m'dima pa nthawi ina m'moyo wathu, kaya mukumva zowawa zotani, zomwe woipayo angathe kuika pa inu, mulungu amamva nanu kuwawa pamodzi ndipo amakufunirani chithonhozo. Mungadziwe bwanji zimenezi? Zingofunikira kuti inu mulingalire zoti munapangidwa modabwitsa basi. Inu simukuyenera kubanika za momwe mungafananire ndi ena chifukwa mulungu anakupangani inu momwe mulilimo popeza ali nanu cholinga-cholinga chomwe inu nokha basi mungathe kuchikwaniritsa. Mulungu sanangokuumbani inu mwachiumbe-umbe ai, thupi lanu komanso malingaliro anu ndzapadera-dera kwa inu ndipo munakonzedwa mwa njira yomwe muliliyo kuti mukagwiritse ntchito mphatso zomwe iye wakupatsani inu kwa ena.

Simunapangidwe mwachipange pange ayi

Nthawi zina zimavuta kumvetsa chifukwa chomwe tinapangidwa mosiyana ndi anthu ena. Pamene tinali ana izi zinaki zovuta kumvetsa zedi ndiponso kuzilandira. Ife tinkafunitsitsa titakhala ofanana ndi wina wake kukhala wosasiyana ndi wina aliyense. Tinkafunitsitsa kuvala zovala zofanana ndi ena onse. Tinkafuna kukhala nawo limodzi. Tinkafunitsitsa kuchitira zinthu limodzi. Ndipo tinkafunanso makamaka kukhala wokondedwa ndi wina aliyense (ayi apatu sitikukamba zokhuza kukondedwa kwa pa facebook (fesibuku) ayi). Ngati tiganiziridwa mosiyana ndi anthu ena, ay, ichi chinali choipa kwa ife. Sitikanatha kulandilidwa ayi. Ndipo pausinkhu wa zaka zochepa umenewu zonse zinkafunikira kwa ife kuti zikhale zovomerezedwa basi. Tikangoona kuti sitikuvomerezedwa kapena kulandilidwa, ichi chinali tsoka kwa ife. Koma zinthu za maganizo oterewa, ngati ninudi munakumana nazo ndiye kuti zinazalidwa mwa inu ndi wonyenga wamkulu uja (satana), osati m'lengi wanu ai. Satana anagwira ntchito nthawi zonse utsiku ndi usana kufunafuna potionongera ife kudzera mzomo aimva za mkati mwathu ndipo iye amadziwa kwa thunthu ndithu Madera omwe ife tiri ofooka kwambiri.

Chimodzi mwazifukwa cha mapangidwe athu apadera-dera ndichoti mulungu wathu ndi waluso m'kalengedwe ka zinthu. Pamene ife tikukhala ndikukhwima mu usinkhu tidzasowekera kuphunzira kulemekeza kusiyana kwathu koposa kufanana kwathu. Tidzasowekera kumvetsetsa kuti kukhala wapadera-dera ndi mosiyana ndi ena ndi m; dalitso, osati tembelero ayi. Mulungu anakupangani momwe inu mulilimo chifukwa iye ali nanu cholinga chomwe ndi inuyo nokha amene mungathe kuchikwaniritsa. Buku lino lapangidwa kuti likuthandizeni inu kumvetsetsa cholinga chanu, cholinga chomwe mulungu chomwe mulungu wachisungira inu nokha basi.

Kanthu kabwino ndithu

Takhalani chete kwakamphindi-muziyerekeze nokha ngati m'modzi wagulu loyimba (band) lalikulu ndipo munaphunzitsidwa mwakupatulika kwanu kuti muziimba ng'oma ya besi kuimba besiko ndikomwe kukupangani inu kukhala inuyo-inu. Mulungunso anakukonzani inu ndinkamvekedwe kabwino kwambiri mkati mwanu kotero kuti mukathe kuimba besi mwabwino kuposa wina aliyense, koma kupatulika, kumeneku kumakupangani inu kukhala osiyana ndi ena-osati kufanana ayi-monga wina aliyense. Aa, zimenezo zingakhale zabwino bwanji? Ndiye tsopano tiyerekeze kuti munthu winanso wabwera pagulu la bandi yanuyo yemwe anaimba bwino chitoliro ndipo inu ndikuganiza mwainu nokha, bola ine ndikanakhala ngati ameneyu. Bwenzi ndili wokondwa koposa" koma podziwa kuti inu simunabadwe ndi milomo yopyapala yomwe inasowekera kuimba chitoliro, inu simukanatha kukhala woimba chitoliro, inu simukanakhala woimba chitoliro wamphamvu ayi. Iyi simphatso yomwe inu munapatsidwa ayi. Inu munakonzedwa ndi mulungu kuti mukhale woimba bwino ng'oma (drum) ya besi. Iye anakupatsani inu kupatulika kotero kuti inuyo nokha muthe kuyimba ng'oma ya besi. Kunena mwatchutchuchu, mphatso yomwe inu mwapatsidwa ndi yomwe inu imakupangani kukhala othekera kuimba besi mwamphamvu zedi. Simukusowekeranso kuyetsetsa kuti muziimba chitoliro chifukwa mulu kale ndi mphatso imeneyi. Palibenso wina angathe kuchita zomwe mumachita inuzi.

Ndiye sopano tayerekezani kuti munthu wina wabweranso wodziwa kuimba bwino banjo (bangwe) ndipo inu mukuganzanso mutakhala inu, bola ndikanakhala ine. Ndikanakhala wokondwa kwambiri" koma popeza inu simunabadwe ndi dzala zazitali zokhoza kufikira bwino zingwe zonse za banjo yanu komanso kuthekera koyendetsa zala zanu mofulumira.

Simukanakhoza kukhala kadaulo (katswiri) wa banjo. Simphatso yomwe inu munapatsidwa ayi. Inu munapangidwa ndi mulungu kuti muziimba ng'oma ya besi. Iye anakupatsani inu kupatulika kuti inu nokha mukathe kuimba bwino ng'oma ya besi basi. Kukhala woimba besi ndicho chomwe inu munaikizidwa m'chibadwidwe chanu.

Mulungu anakulangani inu mewa njira imeneyi-pa chifukwa

Tikaika mtima wathu pa mphatso zomwe tapatsidwa m'malo moika pazomwe anthu ena apatsidwa, tingathe kukhala m'miyoyo yathu kopanda kulimbana. Sitidzataya mphamvu zathu kuyesera kukhala monga ena. Tizakhala othekera kuimba mawu okoma kwambiri chifukwa tizagwiritsa ntchiti zida choimbira chomwe ife tapatsidwa. Idzakhala nyimbo yokoma chifukwa ndi nyimbo yomwe ambuye anikiza mwa iye-mkati mwa miyoyo yathu, ndiponso mkati mwamizimu yathu. Siizakhala yofanana ndi ya wina aliyense. Mudzimva kukhala wodalitsika pokhala wosiyana ndi wina aliyense; kupatulika kwanu ndi m'dalitso wodabwitsa

kwambiri. Kupatulika kwanu mudzathandizira utumiki (ntchito/cholinga) womwe ambuye anakusungirani inu-umene mudzauphunzire mtsogolo m'buku lino.

Satana ntchito yake ndikufuna kuti ife tiziona kuti ndife woipa chifukwa ndife wosiyana ndi ena wonse. Iye nthawi ndi nthawi akuyetsetsa kutinyenga kuti tiziganiza kuti tikanakhala wokondwa kwambiri ngati tikanakhala ofanana ndi ena. Ndipo chifukwa choti timamvetsera ku bodza lakeli, iyeyo amapambana. Satana amadziwa bwino lomwe kuti kodi ndi zingwe ziti zomwe angathe kutikokera nazo m'mbuyo [osati zingwe za banjo ai] kuti akupangeni inu kumakhala okhumbira zomwe anthu ena ali nazo. Iye mophweka tikungoyenera kuika mtima wathu pachomwe tapatsidwa. Nthawi zinse kumbukirani, mulungu wakupatsani chilichonse chomwe inu mukusowa kuti mukhale wokhutitsidwa chirichonse ndithu. Chinthu chimenechi ndiye iyeyo. Mulungu ndiye inu chomwe mukusowa basi. Ikani mtima wanu pa mulungu ndipo iye adzakupatsani iye zokhumba za mtima wanu.¹³³

Iye ali ndi cholinga ndi inu

Tingathe kukhala wokhutisidwa

Mukayamba kumvetsetsa kuti mulungu anakupngani inu pacholinga chapadera-dera ndipo kuti chifuniro chake ndi changwiro, pameneponso mudzayamba kumvetsetsa kuti mphatso zapadera zome anakupatsani inu-zapangidwa kuti zikudalitseni inu. Ndipo pamen inu mukondwera mu mphatso zapadera zomwe anakupatsani inu, iye adzakwaniritsa zokhumba za mtima wanu¹³⁴ ndipo pamene inu mukhala ndi zokhumba zoyenera, iye adzakwaniritsa zokhumba zimenezo¹³⁵ izi ndi zowinawina kale ngati ife tiika mtima wathu pa mphatso zomwe munatipatsa tingathe kukhala wokhutisidwa ndipo sitizakhumbiranso zomwe anthu ena alinazo. Sitizasowa kanthu konse-kupatula mulungu yekha basi. Ichi ndicho chikonzero cha mulungu pa wina aliynense pa ife. Choncho khalani wosangalala pa kukhala wapadera-dera. Kunena zoona, khalani wonyadira ndi kupatulika kwanu. Musayesere kukhala wofanana ndi ena ayi. Likanakhala dziko lotopetsa ndiponso lovuta kukhala kwambiri ngati mulungu akadatipanga tonse wofana.

Palibe chosatheka

Kodi mukudziwa kuti mulungu anakhazikitsa mwa inu chikonzero (plan) ngakhaledziko lapansi lisanalengedwe?^{136 137 138} ndipo iye amakonzeratu zaka zosayamba moyo womwe inu muli kukhalamo lero lino.¹³⁹

Chikonzero chakecho mkutheka mwina angathe kukutengerani pa mseu wa maenje pa basi yomwe iye akukuyendetsamoni koma dzenje lina lililonse lomwe likupezeka mu mseu m'menemo liri ndi cholinga. Mayenje amenewa

anakonzedwa ndicholinga chofuna kukuthandizani kukula mu uzimu. Mwinatu inu mukuyenda m'mayenje amenewa sopano lino.

Kuyenda mu mseu wa maenje chingathe kukhala chikonzero cha mulungu kuti inuyo mudutsemo. Iye nkutheka akufuna kuti inuyo muone chinachake, kapena mumve china chake, kapenanso kuti mukumane ndi china chake. Maenjewa angathe kuphatikizidwa kukumana ndi zowawa. Zingathenso kukhala kukumana ndi zophweteka, komanso kutaika kwa china chake pamoyo wanu. Zingathenso mwina kukhala nchisomo chachikulu kuthekanso kukhala chozizwa. Komanso zonsezi zimakhala ndi cholinga ndithu. Mulungu anabwera kuzakhala nafe pakati pathu kotero kuti tikathe kumkhulupilira mwa iye, ndi moyo wathu komanso tsogolo lathu. Kumtsata kumtsata iye kumasowekera chikhulupiliro, ndipo chikhulupiliro ngakhale chochepe iye amalonjeza kuti palibe chomwe sichizatheka kwa ife.¹⁴⁰

Kukhala pa ubale ndi iye yemwe anakulengani inu kudzakupatsani inu lingaliro latsopano kwathunthu pachifukwa chomwe inu munabadwira. Mulungu amakondwera pamene ife tikhala oyamika pa chomwe iye anatipatsa (chomwe tiri nao). Kukhala woyamika kumatithandizira ife kukhala wosandulika, kukhala chomwe iye angathe kuchigwiritsa ntchito. Kukhala woyamika pa zomwe tiri nazo kumatimasulanso ku chosowa chowasuntha anthu ena. Tganizilani kufunikira kwa chimenechi-pamene mukhala woyamika pa zomwe muli nacho ndiye kuti simuzasowekeranso kukhala wosunthika ndi anthu ena. Kodi ndi mtendere wotani umenewu. Sangalalani, ndipo kondwerani, ndiponso khalani wodalitsika pokhala ndi chikhalidwe chakuyamikira zomwe inu muli nawo. Chonse chomwe inu mukusowa-ndi iyeyo basi.

Komanso kumbukirani kuti china chilichonse chomwe mukukumana nacho, kaya ndi mazunzo kapena chokhumudwitsa, mulungu angathe kuchigwiritsa ntchito ku ubwino wa inuyo¹⁴² kukhala woyamika pa chinachilichonse chomwe inuyo mukukumana nawo kungathe kutembenuza maganizo anu wolakwika (mwachitsanzo, chifukwa chani izi zachitika kwa ine?). ndikukhala maganizo abwino (mwachitsanzo, zikomo ambuye pokhala nane nthawi zonse). Kukhala woyamika kumaumiliza chidwi chanu kuyang'ana kunja-kwa mulungu, ndiponso kwa ena, m'malo mongoyang'ana mkati mwa inu nokha. Kukondwera ndi kuyamika zidzakutontholetsani inu. Mudzadera nkhawa mochepa kwambiri. Muzakopa anthu ena chifukwa cha kutonthola kwanu, zomwe zidzapangitsa moyo wanu kukhala wolumikizika kwambiri komanso kukhala wa cholinga. Apa ndipamene mulungu angathe kukugwiritsani ntchito inu komanso kukudalitsani chifukwa chokhala ndi chikhulupiliro mwa iye.

Iwo amene ali wosiyana

Anthu ena anabadwa wosiyana ndi anzawo, koma mulungu akuti ali ndi cholinga pa chilichonse chomwe iye amalenga. Tamvetserani ndime iyi kuchokera pa yohane yokhuza munthu wina yemwe anabadwa osawona:

Yohane 9: 1 “ndipo popita, anaona munthu wosaona chibadwire. 2 ophunzira ake ananfusa iye, nanena, Rabi, anachimwa ndani, ameneyo, kapena atate wake ndi amache, kuti anabadwa wosaona” 3 yesu anayankha, sanachimwa ameneyo kapena atate wake ndi amake, koma kuti ntchito za mulungu zikaonetsedwe pa iye.”

Mulungu akutiphunzitsa ife kuti munthu ameneyu anabadwa chonchi kotero kuti moyo wake uthe kulemekeza bmulungu. Choncho ngati inu muli ndi maganizo wolakwika pa momwe munthu wina anabadwira, kumbukirani nthawi zonse kuti mulungu ali ndi choliga pomulenga iye mwa njira imeneyi. Cholinga cha mulungu ndichoti munthu ameneyi amulumekeze iye.

Nthawi zambiri timaganiza kuti munthu wina yemwe wabadwa mwa njira ina yake ndiye kuti ndi chilema, kapena ndi osafunikira, mulungu sauna mwa ngira imeneyo ayi. Mulungu analenga aliyense mwa njira ya padera-dera kotero kuti akathe kumgwiritsa ntchito kutumikira anthu ena. Mulungu samafuna kuti tizikangana naye ayi. Kapena kumumvera chisoni pamene munthu wina walengedwera, chifukwa iye wamulenga aliyense mwa njira ina yake pachifukwa (cholinga).¹⁴³

Tonsefe ndi chuma cha mtengo wapatali cha mulungu

Pa maso pa mulungu tonse talengedwa mwa njira yomwe iye mulungu anifuna pa ife. Tonsefe tapangidwa modabwitsa ndipo ndife chuma chake cha mtengo wapatali.¹⁴⁶ Izi zitanthauza kuti pali ntchito yapadera-dera yomwe mulungu ali nayo yokonzedwera pa inu yomwe inu nokha ndi amene angaichite, munjira imene inuyo mungathe kuchitira palibe chinthu china chake mwa inu chomwe chidzataidwe kapena kuonongeka. Mulungu amagwiritsa ntchito kale lanu, tsopano lanu, komanso nyengo zanu zonse zowawa ndi zovuta zomwe inu mwadutsamo kuti akukonzekeretseni za tsogolo lanu. Mphempheni mulungu nzeru kuti akuthandizeni kumvetsetsa chifukwa chomwe iye amakupangani inu momwe mululimo komanso chifukwa chomwe iye anakuikirani pansi pano. Iye ali ndi cholinga chabwino kwambiri pa inu. Inu munalengedwa chifukwa cha iye kuti mukachite ntchito zabwino.

MUTU 3

NDINAPANGIDWA KUTI NDIKHALE KUDZERA MZOVUTA ZAMBIRI

CHIKHALIDWE CHA UCHIMO

NDINABADWA WOCHIMWA

Mulungu sanalenge munthu kuti azichimwa. Mulungu anam'lenga munthu wopanda cholakwa¹⁴⁷ koma mulungu anatipatsa ife ufulu, wochita chifuniro komwe kuli kuthekera kopanga ziganizo za ife eni. Izi zikutanthauza kuti tingathe kupanga ziganizo zolungama ndi dongosolo la mulungu, kapenanso kupanga ziganizo zosalungama ndi dongosolo la mulungu, omwe umatchedwa uchimo. Ndiponso iye watipatsa ife kuthekera kosankha (kuchita chisankho chomwe tifuna eni). Ife zikutanthauza kuti mulungu watipatsanso kuthekera komkana iye, kapena kusamalira za iye. koma chinthu chofunikira ndichoti zonse ndi malinga ndi chisankho chomwe ife tingachite. Ndindani amene safuna kukhala 100% uyang'ani wa pa ziganizo za ife eni? Uku kuli ngati kumusiya mwana mnyumba ya m'bulu wa shuga ndikuchokapo. Zoonadi, umu ndimomwe mulungu watipatsira yemwe wa ife-kutheka kopanga ziganizo za ife eni ndinso kupanga zomwe tifuna eni. Choipa choposa, iye wasiya mwini wake wa m'bulu wa shugawu, yemwe ndi satana, mkati mwa nyumba imeneyi kuti akope ana onse omwe angalowemo (tonse a ife) kuti tidye mulingo wa shugayi monga momwe tingafunire. Ndipo pokhala ndife osadziwa monga tirilimu, ndipo ngatinso tikhala osamvetsa ku machenjezo atate wathu, tizamumveradi mwini nyumba ya shuga

uja. Mwini shugayo adzapitilirabe kutiyesa ife (kutiika m'mayesero). shugayi ndiwa bwino ndithu nanga angathe bwanji kukuvulazani inu? Ndipo, ndipo kumudya mulimonse monga momwe mungadyere, ndi zabwino kwa inuyo!" ndipo palibe munthu yemwe angaziwe kuti munadya wochuluka bwanji choncho idyani wochuluka ndithu!" ndipo popeza timasankha kunyalanyaza malangizo atate wathu, timayamba kudwala. Ndipo pambuyo pake timadzadzuka mkati mwa utsiku ndikunena, "oo, mamba yanga ikundiwawa. Inetu ndimangochita zomwe mwina wake wa shuga uja anena, komanso kulonjeza nanga n'chifukwa chiyani ndinadwala".

Pamene mulungu anatilenga ife iye amadziwa kuti njira yokhayo yomwe iye akadatha kudzakhalala nafe pa ubale inali yotipatsa ife mpata womvetsera kwa iye, apo ayi sadakhala ndi ubalenso ai. Chikondi sichingakhale chikondi ngati sichiri mwa njira ina iliyonse chokhudzidwa. Ndiye mulungu analola tonse a ife, kuti tipange ziganizo za ife eni angakhale olo zitanthauza kuti ifeyo tasankha kusamumvera iye. mulungu waika pansi zotichenjeza moyang'anana ndi maenje pa mseu patsogolo pa ife-ndipo kenako anatipatsa ife makiyi a galimoto. Tingathe kusamalira machenjezo ake, kapenanso tingathe kunyalanyaza machenjezo akewo. Pambuyo pake iye adzatilola kuyendetsa galimoto kupita kwina kulikonse komwe ife tingafune.

Uchimo umalowa m'dziko lapansi kudzera mwa munthu m'modzi, amene anali Adamu, ndipo wakhala ukugwira anthi mibadwo yonse kwa wina aliye nse wa ife.¹⁴⁸ Chikhalidwe cha uchimo chimenechi ndiye gwero lake la maganizo athu auchimo komanso zidzolowezi zathu zoipa. Tchimo lili ndi mizu yake m'mitima mwathu yomwe imatakatsa maganizo athu, amenenso pamapeto pake amakawonetsera kupyolera m'matupi athu ngati ife tasatila ndi kulondola pamodzi ndi zikhumbokhumbo zathu zolakwika.^{151 152} Nthawi iliyonse imene ife tichimwa timaperewera pa mlingo wa mulungu pa moyo wathu.

Ndi chisankho chathu

Podziwa kuti tonse tapasidwa ufulu wochita chifuniro chathu tingathenso kusankha kukhala molingana ndi ndondomeko za mulungu, kapenanso tingathe kusankha kukhala ndi ndondomeko za ife eni. Tchimo mwachidule limatanthauzilidwa ngiti kupunthwa (kutsutsana). Ndi mfundo kapena chikhalidwe cha mulungu. Choncho, izi zitanthauza kuti pamene tichimwa ndiye kuti talephera kufikira kundondomeko/chilungamo zomwe mulungu anazikhazikitsa pa ife.

Funso lifunikira kwambiri limene tiyenera kuzifunsa tokha: kodi tonse tinabadwa ochimwa, komwe kuli kulephera kutsatira chilungamo chomwe mulungu watikhazikitsira ife?

Yankho ndi inde, komanso ai.

Inde, tonse tinabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo. Komanso ai sitinatuluke m'mimba ya amathu ochimwa. Kuchimwa kwathu kunabwera mtsogolo mwake-pamene tinali achikulire kuti tingathe kumvetsetsa (kudzindikira). Kusi yana pakati pa choipa ndi chabwino ndipo tinayamba kupanga ziganizo motsatira zidziwitso (chikumbu mtima) zomwe tinkadziwa kuti zinali makhalidwe otsutsana ndi mulungu.

Tonse tinatenga chikhalidwe cha uchimo

Ndizosavuta kusimikizira kuti tonse tinabadwa ndikutengera chikhalidwe cha uchimo.¹⁵⁴ Tangokhalani ndi mpata woyang'ana kamwana kakang'ono. Mwana mwachikhalidwe ndi wozikonda ndipo palibenso wina aliyense amene anamphunzitsa iye kuti akhale wozikonda. Kukhala wozikonda ndimo tonse tinayambira chikhalidwe chathu. Zimakhala zongobadwa nazo basi.¹⁵⁵ Kukhala ndi chikhalidwe cha uchimo ndi n'chitidwe womwe tonse tinachita kubadwa nao.

Pamene mwanayo ayamba kukula m'sinkhu amayamba kuphunzira chabwino kuchokera ku choipa ndi kuzikonda kumeneku sikukhalanso njira yaikulu yokhalira ai. Mwanayo amaphunzira nthawi zina m'njira yovuta kwambiri, kuti angathe kusamakondwa ngati iyeyo atapitiliza njira zake zozikondazo. Iye amaphunzira kuti kudzikonda kwakeko kukumupatsa mavuto. Pang'ono ndi pang'ono, iye amaphunzira kulamulira zikhumbitso zake zozikonda zija ndipo kuti kukambirana ndi kugawana zinthu pa moyo ndiyo njira yabwino. Apatu ndipamene khalidwe lake liyamba kusintha. Amayamba kupanga ziganizo zolingalira bwino zokhuza momwe iye afunira kuti akhale-kugawana ndi amzake kapena kusagawana nawo.

Pamene iye apitilira kuchitachita ndi anzake komanso kukula usinkhu, amakumana ndi zisankho zochulukirachulukira-kuchita zinthu zomwe zili zokhoza, kapena zolakwika, ndi mtima wachifundo kapena woipa, ndipo apa ndi pomwe uchimo umalowa nmdikuyamba kuonekera. Tsopano iye ali ndi kuthekera kopanga ziganizo, zomwe zili zolingana ndi chifuniro cha mulungu, kumene kuli kuchimwa.

Pamene tikukula mu usinkhu wathu timaphunziranso zokhuza udindo komanso kuwerengera za umunthu wathu pa kupanga ziganizo. Timaphunzira nthawi zina movuta kwambiri, kuti ziganizo zathu zigathe kukhala ndi kulipira mtengo kwakukulu zedi, monga kutenga matenda, kupita kundende, kuledzera ndikuchita ngozi ya galimoto ndiponso nthawi zina ngakhale kumwalira kumene. Pamene tikukula kufikira ku ukulu timayamba kuphunzira kuti ziganizo zathu zingathe kukhala ndi zotsatira zake zoipa kwambiri.

Motero, tingathe kulora kuti chikhalidwe chathu cha tchimo chilamulire moyo wathu, kapena kuti ifeyo tilamuliere (tigonjetse) chikhalidwe chathu chauchimo popanga ziganizo zathu zomwe ndizolingana ndi ndondomeko za mulungu

ndinso ku m'dalira iye, m'zosowa zathu komanso chikonzero chake pa moyo wathu. Pamene tisatira komanso kudalira mwa mulungu chikhalidwe chathu choyenera chimakhala ndipo timayamba kusamira ku ndondomeko zoyenera za mulungu anatikirira ife" kodi mdadziwapo kuti limeneli ndiye tanthauzo la uchimo-kutembenuzidwa kulowa pansu (kuima dodolido)?

Tidzawerengeredwa m'landu

Monga anthu achikulire nthawi zonse tiyenera kukhala wokhuzika ndi zisankho zomwe timachita. Nkhani yabwino ndiyoti-tonse tingathe kugonjetsa chikhalidwe chobadwa nacho cha uchimo. Tonse tingathe kusankha kulinganiza maganizo athu komanso zochita zathu ndi ndondomeko za mulungu pamodzi ndi mfundo nzake.

Choncho, kodi muzamva kuwawa ngati simukhala molingana ndi mfundo za mulungu? Mungathe kumaona ngati simukuvutika kwenikweni, kapenanso simukuvutika kumene, pa ziganizo zomwe mumapanga. Yakho ndiloti-mwina mwake inde, koma zotsatira zake zingathe osakhala nthawi yomweyo, ndiponso za zosatira zomwe mwapangazo mwina sizingakhalenso chinachake chomwe mukukumana nacho monga munthu. Mwachitsanzo chomwe chikuwonetsera zonse ziwiri. Mwaphuzira kale m'moyo mwanu kuti chiganizo chomwe munachita mulu khola lochepa usinkhu chapangitsa kuzunzika kwa bongo (maganizo) pa m'modzi wa ana anu-zomwe mwanayo sanakuuzeni ndi kale lonse. Ndipo kuzunzika bongo kwa mwana kumeneko kumasinthira chikhalidwe chonse cha moyo wa mwanayo-koma osati kusintha kwa bwino ai. Izi zidzatanthauza kuti tizimva chithonhozo mumtima mwathu pamene sitikulandira zotsatira zake za zolakwa zomwe tinachitan ai. Mulungu anatilingejeza kuti tidzatuta chomwe tinafesa.¹⁵⁷ angakhale ngati sitinalangike chifukwa cha machitidwe ochimwa, koma tidzakhalabe owerengera m'landu chifukwa chamazunzo omwe tinapangitsa anthu ena kuti aone.

Chokhacho choti sitinathe kukumana ndi zowawa komanso kuzunzika chifukwa cha zolakwa zathu zikutanthauza kuti chinachake chosmphana ndithu chidzayenera kukhala choona: kuti machitidwe a anthu ena pamodzi ndi ziganizo zawo zingathenso kupangitsa kumva kwawa komanso kuzunzika pa ife. Zikuyenera kuchitika mwa njira imeneyi ndithu, apo ai, ndiye kuti ufulu wa chifuniro uja ndiye kuti sungakhalenso ufulu wa chifuniro ai. Pamene ife tisankha kuti tichimwe ndiye kuti tikusankhanso ndondomeko zosalingana ndi mulungu-zomwe zingabweretse mavuto komanso kuzunzika m'moyo wa ife eni¹⁵⁸ - komanso m'moyo wa anthu ena.¹⁵⁹

Mulungu angathe kutembenuza athu kukhala china chake chabwino kwambiri

Inde, mulungu akadakhoza kupwetsa zowawa zanu ndi mazunzo anu. Iyetu ndi mulungu mukukumbukira? Koma mulungu amalola zowawa ndi masautso chifukwa iye amafuna kuti inuyo muphunzire pa iye. tonse timalimbikitsidwa mitima kuitanira pa mulungu pamene tamva kuwawa, chisoni, kapena nkhwawa. Ngati inu muyandapo mdu ndege m'lengalenga mokhala mabampu ndiye kuti mukumvetsetsa bwino momwe izi zimamvekera. Umagwilitsitsa mpando kapena munthu amene wayandikana naye, ndipo umapemphera mwa mphamvu. Mumapempherera chipulumutso. Mumapemphera kuti muthe kutonthozedwa ku zowawa (zisoni) zanu. Mulungu angathedi mwamphamvu zake zopanda malire kukupulumutsani. Iye amadziwa kuti mayendedwe wopsa oterewo angathe kukusunthirani chifupi ndi iye. ndipo tonse tidziwira, zowawa ndi mazunzo zimachitika nthawi zonse. Iye angathe kutembenuza zoopsa, mavuto ndi zowawa kukhala china chake chabwino kwambiri.¹⁶⁰ Ndi kuchokera m'zowawa ndi m'zopweteka zathu momwe timapedza iye. Kuchokera m'kupsinjika kwathu ndi kusweka mtima kwathu timachilitsidwa.

Kuchimwa sichinthu chomwe tinachita kubadwa nacho ai; chikhalidwe chathu cha uchimo ndicho tinabadwa nacho. Kuchimwa ndi chisankho cha munthu mwini. Mulungu amadana ndi tchimo¹⁶¹ ndipo tchimo lathu limatilekanitsa iye ndi chitetezo cha chikondi ch mulungu.¹⁶² nthawi zina kuzunzika kwathu chifukwa cha kuchimwa kwathu kungathe kukhala kowawa kwambiri. Koma kaya ndikuwawa kotani komwe takumana nako, kapena mazunzo otani omwe takumana nawo, mulungunso naye amamva kuwawa komweku-ndinso mazunzo onsewa. Mulungu amamva kuwawa ndi machismo pamene anabwera pansi pano kudzakhala pakati pathu. Kunzuzika kwake kunali kwa kukulu zedi, kotero kuti iye anafa nako-pa cholinga cha iye mwini, pa mtanda paja, atatha kumenyedwa kwambiri, ndi mikwapulo pamodzi ndi zolatsa ndi minga zolowa m'thupi mwake ndikukakamizidwa m'mutu mwake, zoonadi iye anapachikidwa pa mtengo, pamwamba pa phiri, okhomedwa ndi misomam'manja mwake ndi m'mapazi ake, zonsezi zolenga iye mwini. Anamva zowawa zonsezi pa zolinga za iye yekha.

Iye akadakhoza kuleka kudutsa muzowawa zonsezi. Komanso imfa yakeyo, koma sanatero ayi. Iye anayenera kufera inu ndi inelchi chonsechi chinali mbali imodzi ya mapulani ake-omwe iye ananenerati m'chipangano chatsopano.¹⁶² Ichi chinali chifukwa chomwe iye anabwelera. Chinali chikonzero chake kuyambira pachiyambi pomwe. Iye anadziwiratu kuti uchimo adzalamulira dziko lapansi ndiponso kunalibe njira ina iliyonse yotipulumutsa ife ku machismo athu. Iwe amadziwa kuti adzasowekera kuti abwere m'dziko lapansi, ndikudzafa chifukwa cha ife. Ngati Mulungu sankadziwa kuti Adamu adzachimwa, ndipo kuti m'modzi mwa angelo ake a akulu lusifala (satana) anzapandukira, ndiye kuti adalakwitsa. Iye anadziwa bwino lomwe chomwe chidzachitike pamene anatipatsa ife ufulu wa chifuniro-kuti tidzasochera ndi kuchimwa. Iye anadziwa kuti ife tizachita

monga mwana wa mng'ono m'nyumba ya shugayo adzatinnyenga mosavuta m'kuganiza kuti shuga wochuluka adzakhala wabwino kwa ife.

Choncho mulungu angathe kumvetsetsa kwambiri za mazunzo anu. Iye amazunzika¹⁶⁵ ndipo anafa chifukwa cha inu kotero kuti inu, ngati mudzakhulupilira mwa iye mungathe kukhala pamodzi ndi iye kosatha (kwa muyaya).¹⁶⁶ Ngati inu simukhulupilira iye-chabwino, mathero anu amuyaya adzakhala woipa kwambiri.

Inde, iye anali pomwepo

Ndiye mwina mungathe kumazifunsa nokha mafunso: kodi mulungu anali kuti pomwe chinthu choipachi” chin'kachitika m'moyo mwanga? Yankho ndiloti, iye anali pomwepo. Anamva ululu wonse omwe inu munaumva, ndipo iye anadana nawo chomwe chinachikacho. Koma analola kuti chichitike kuti akathe kukwaniritsa chinachake chchikulu. China chake chachikulu chimenechi ndiyo mphatso yake ya kwa ife tonse, yomwe ili mphoto yathu yosatha pa kudalira kwathu pa iye komanso komanso kukhala ndi chikhulupiliro mwa iye. tsiku lina iye adzabwezeretsa zinthu zonse^{168 169} ndipo sikudzakhalanso mazunzo ai. Monga momwe khola la chikondi lingathe kulora kuti mwana amve zowawa kutsatira chisankho chomwe wachita, motero mulungunso amalola kuti timve zowawa potsatira zisankho zolakwika zonse zomwe tinachita. Mwatsoka lake izi zithanso kuphatikizapo zowawa zotsatira zomwe anthu ena anchita. Tingathe kukhala osamvetsetsa za maphunziro omwe mulungu akutiphunzitsa mynthawiyo, koma ululu wa zotsatira zimenezi omwe timaumva ungate kuthera mu kusinthika kwa moyo. Ndipo monga mwa dongosola la mulungu, kusintha kwa moyo ndi kwabwino, maka uko kumene kwakonzedwa kuti kumvetse kuwawa. Mulungu amakhumba kuti ife tisinthe kotero kuti iye akathe kutigwiritsa ife ntchito. Iye amatifunira ife kusinthika mwa kukonzanso mwa malingaliro athu.¹⁷⁰ izi zikutanthauza kuti mulungu anlola kuti ife tikumane ndi mavuto komanso zitsautso m'moyo mwathu,^{171 172} ndicholinga choti ife tithe kuwandikira kwa iye. iye amafuna kuti ife tithe kusandulika ndikulowa njira zake za kaganizidwe kotero kuti akathe kugwiritsa ife ntchito, ndikudalitsa. pamene tiyamba kumvetsetsa chifuniro chake pa miyoyo yathu apa ndi pamene tingathe kuyamba kuazindikira chifukwa chomwe tinabadwira, komanso za momwe zolinga zathu ziri.

Mwina tingathe kumakumana ndi zovuta chifukwa choti ndanamizidwa

M'munda muja

Zolengedwa za ngwiro, Adamu ndi Hava, anakhala wochimwa pamene iwo anasakha kusamvera malamulo a mulungu m'munda mwa Edeni. Iwo anasankha kudya chipatso chamu mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa angakhale mulungu anawauza kuti asadye. Inde, ndi zoonza kuti Adamu Hava sanapezeke m'nunda muja okha ai, wonyenga wamkulu uja (satana) analinso momwemo. Cholinga choyambilira cha satana ndi kutisokoneza ife, kutipanga ife kuonongeka, kuononga miyoyo yathu, ndikuiikitsa ife pokana mulungu. Iye amafunitsitsa kuiika chionongeko chchikulu pa ife chifukwa iye amadana ndi china chilichonse chopangidwa m'chifanizo cha mulungu.

Chinyengo komanso mabodza ndizo zida zomwe iye amagwiritsa ntchito. Winw aliyense anayamba wanyengedwapo akudziwa bwino kuphweka kwake kwa momwe zimachitikira-angakhale tiri chipenyere. Ndipo pamene tavulazidwa, zonse zomwe tinganene ndi kungoti, ha, ndachimwanso...eti!"

Satana ndi wabwino pachinyengo chake moti mabodza ake amatha kuoneka ngati choonadi. Motero timatha kumumvetsera iye, ndipo timakhulupilira iye, angakhale timanka ndi kuvulalira-vulalirabe. Timaoneka kuti sitifika posiyanyitsa pakati pa ziganizo zathu zoipa ndi mavuto omwe amatsatirapo. Satana ndiye m'konzi wa m'chitidwe wa uchimo uwu m'munda mwa Edeni, ndipo akunkera-kerabe kukhala m'konzi wa mabodza ndi chinyengo lanthu lero lino. M'munda muja satana anmunyenga Adamu ndi Hava kuti sadzafa ai ndithu" ngati adzadya zakumtengo uja wodziwitsa zabwino ndi zoipa. Ndipo pamene Adamu ndi Hava anakana choonadi cha mulungu pakudya zochokera ku mtengo uwu, pamenponso ndi pomwe kusalakwa kwao pamodzi ndi kwa ifenso kunataika, ndipo pamenponso ndi pomwe dziko la masautso linayambira.^{173 174} Munthu anasankha kusamumvera mulungu tsiku kimene lija-ndipo ochuluka athu lero lino akupitilirabe kusamumvera mulungu lero lino. Mulungu akankhoza kukonza mazunzo onse am'dziko m'kamphindi-koma iye anatipatsa chisankho. Anatipatsa ife ufulu wachifuniro. Ngati mulungu akanakhoza kuthana ndi mavuto onse a dziko lapansi, amene ndi ifeyi tidawapanga, ndiye kuti ufulu wachifuniro womwe anatipatsa ife ukanakhala wopanda tanthauzo ndiponso tikanakhala opanda chiwerengero cha chisankho chatu cholakwikachi.

Choncho pamene inu muli kufunafuna komanso cholinga m'moyo-woipayo adzapitilirabe kunong'ona m'makutu mwanu (kwinanso panthawi ino ali mkati mokunong'onezani) kunena kuti ndinu wopanda pake ndiponso kuti ndinu wopanda chiyembekezo. Koma kumbukirani kuti ali ndi bodza. chimenechi sicholinga cha mulungu pa moyo wanu ayi. Tonse tiyenera kuzindikira kuphunzira liwu la mulungu monga momwe nkhoa imamvera liwu la m'busa

wake. Iye tikungofunika kukhala anzeru monga ana ankhosa. Ngati siriri liwu la mulungu lomwe tikumvalo, tidzasowekera kukhala wochenjera ndithu kutembenukira mbali ina ndikuyamba kuyenda.

Mphamvu yokhayo ya satana

Satana alibe mphamvu iliyonse pa ife kupatila kutinyenga ife-koma m'gawo lachinyengochi iye ndiwochenjera kwambiri. Iye sangativulaze mwathupi maso ndi maso ai, koma iye angathe kutinong'oneza m'makutu mwathu, iye ndi kadaulo kwambiri kotero kuti ife sitingathe mpang'ono pomwe kudzindikira machenjeleru akewo anasamira pa zofooka za umunthu wathu komanso zokhumba za umunthu wathuwo. iye amadziwa bwino lomwe dera lomwe tiri ofooka kwambiri. Choncho ife timamvetsera kwa iye, ndipo timakodwa mu m'sampha wake ("aa komatu chitnhuchi chinali chooneka bwino kwa ine"), ndipo pambuyo pake tidzazindikira kuti tinanyengedwanso. Ngati ife tipitiliza kulola zikhumbitso zathu kuti ziziyenda mosaunikilidwa ndiye kuti tizapitilira kutengera zotsatira zobvuta, zowawa, kupweteka, mazunzo, maubale opasuka (oonongeka) ndi zina zambiri. Tangotengani ka mphindi kulingalira ka nkhanika. Ambiri mwa mavuto omwe lero tikudusamo ndi zotsatira zosamvetsera liwu la mulungu komanso ziphunzitso zake. Anthu siangwiro ai, koma anthu ali ndi kuthekera kokhala ndi ubwino wa iwo eni.

Tikumayang'ana munthu ndiye ndikumayembekezera ungwiro pa iye tidziwe kuti tidzakhumudwa kwambiri. Koma inu yang'anani zofunikira za iye zokhala mkati mwake mwa munthu aliyense ndikumuthamangira iyeyo kuti athe kufikira ukoma ndi kuthekera kwake, mwachitsanzo kusanyalanyaza machenjezero a mulungu zomwe zimathangatira kuti ife tisapunthwe ndi maenje omwe satana watikira mtsogolo mwathu. Ndiponso nthawi zina maenje amenewa amakhala okuya kwambiri, ndiponso amavulaza kwakukulu.

Koma tiyeni tsaiwale kuti ife ndiye anthu ndithu, ndipo nthawi zonse tidzakhala tikudabwitsa. Ngakhale kaya titakhala wochenjera motani pa zokhuza machenjezero ochulukira a satana-komabe tizakhala okumana nazo zowawa, Kutaika, kusalidwa, kuthodwa, chisoni komanso zovuta zina zambiri pokhala ife ndi moyo. Nkhani yabwino komabe ndi yakuti, Mulungu amatiuza ife kuti iye angathe kugwiritsa ntchito zoipa zomwe zikuchitikira ndipo angathe kulenga chinachake chabwino kuchokera m'menemo.^{175 176} Ngati ife titamtsata iye. Izi ziyenera kukupatsani chiyembekezo chachikulu pa china chilichonse chomwe inu mukudutsamo. Mfundo imeneyi ndi yofunikira kwambiri kotero kuti tiyenera kuibwerezanso; Mulungu angathe kugwiritsa ntchito zoipa zomwe satana wazikonza m'moyo mwanu

Ndipo iye angathe kuzitembenuza izo ndikukhala chinthu chinachake chabwino ngati inu mutamtsata iye. kodi ndi lonjezo labwino lotani ili!

MASAUTSO ATHU NDIZO NJIRA ZOMWE CHIKHULUPIIRO CHATHU CHIMATSIMIKIZIDWA

Izi zikutanthauza kuti muli chozizwa m'mazunzo athu. Ukulu wake wa Mulungu pamodzi ndi chikonzero chake pa ife zizagwiritsa ntchito mabvuto athu kuthandizira kulimbitsa chikhulupiliro chathu mwa iye. mayesero athu pamodzi ndi mabvuto athu ndizo njira zomwe chikhulupiliro chathu chimatsimikizidwa. Choncho mwamvemvemve, mabvuto athu pamodzi ndi mazunzo athu ndizo njira zomwe Mulungu amatilungamitsira, kutilimbikitsira komanso kutumba ife kukhala cholengedwa chomwe iye angathe kuchigwiritsa ntchito zomwe¹⁸⁰ zizatipange ife kukhala okhazikika okhonza kuimanji kutsutsana ndi machenjezero ochulukira a satana. Mayesero omwewo omwe satana amaika inuyo kuti muonongeke nawo, munthu azawagwiritsa ntchito kuchiombola chanu komanso kukhala kwanu kwauzimu.¹⁸¹

ZOPEMPHA ZINA ZA SATANA ZIDZATHA KUYAMBA ZADZERA KAYE KWA YESU POYAMBIIRA

Kodi munayamba mwadziwapo kuti mulungu amalora satana ndi ziwanda (amithenga) zake kuti akuyeseni inu? Mulungu akanakhoza kumletsa satana kuti asakuyeseni inu ngati akadafuna kutero (kumbukirani kuti iye paja ndi Mulungu), koma kumlola satana kuti akuyeseni inu, ndi gawo limodzi la chikonzero chapadera cha mulunguyo kuti akuumbeni inu mchikhulupiliro chanu mwa iye. Mulungu adzakuikani inu m'mayeso¹⁸² koma osati kukuyesani ayi.¹⁸³ Iye timayesedwa pamene tatengedwa ndi zikhumbitso zoipa za ife eni.¹⁸⁴ Yesu akutiphunzitsa kuti uchimo umayamba ndi ndi iyeyo¹⁸⁵ tiyenera tisaiwale kuti Mulungu ali ndi uyang'aniro wa mphamvu pa Satana.^{186 187}

Baibulo likutiphunzitsa ife kuti pafupifupi ena, ndiponso mwina onse amapempe (zopempha) a Satana oti akuyeseni inu angathe ndithu kudutsira mwa Yesu poyamba-ndipo Yesu ayenera kunena "Inde" (eya) kuzopempha za Satanazo. Koma ngakhale kuti Yesu atanena eya, iye akutilonjeza kuti sadzalola kuti Satana akuyeseni inu mopitilira kuthekera kwanu.¹⁸⁸ munthawi ya m'gonero otsiriza pamene yesu anawauza ophunzira ake pomwe anali kupita (mwachitsanzo kukapachikidwa), Yesu anauza Petro kuti Satana amufunsa kuti ampete Petro ngati tirigu¹⁸⁹ izi zikutanthauza kuti ena ndiponso mwina onse amapempe asatana kuti akuyeseni inu angathe ndithu kudzera (kudutsira) mwa yesu poyamba. Kodi izi sizokoma kwambiri? Chifukwa chomwe Yesu analolera mayesero kuti atsimikize chikhulupiliro chanu mwa iye.

Pamene izi zikuchitika - Yesu nthawi zonse azakhala akupemphera kuti chikhulupiliro chanu chisadzime, monganso muja momwe anamuzira Petro Kunene kuti anamupemphelera iye kuti chikhulupiliro chake chisadzime. Choncho angakhale ife tikhale osasimikizika kaya satana akufuna Yesu kuti atiyeseb ife kapena ayi, tiyenerabe kudziwa kuti Satana amafunitsitsa kuti alimbane naye ndikutipeta ngati tirigu. Izi zitathauza kuti tiyenera kuyesedwa ndi mayesero ambiri kuti aone ngati chikhulupiliro chathu chiri chenicheni kapena ayi.

TIDZICHIYESA CHIMWEMWE CHOPOSA PAMENE TIKUMANA NDI MAYESERO

Tonse aife timapeza kukhala chithu chovuta pamene tiri mkupetedwa. Mulungu akutiiza ife kuti tidzichiyesa chimwemwe choposa paliponse pamene tikumana ndi mayesero,¹⁹¹ poziwa kuti mayesero amabwera kuti ayese chikhukupiliro chathu, ndipo chiyesedwe cha chikhulupiliro chathu chizachita chipiliro ndipo chipiliro chiyenera kutsiriza ntchito yake kotero kuti iye tikathe kukhala angwiro komanso amphumphu (okwanira) osasowa kanthu monsemo.¹⁹²

Koma khalani ochenjera-ndi pokhapokha pomwe inu muika chikhulupiliro chanu mwa yesu pamenenso inu mudzayesedwa ndinso kukumana ndi mayesero, choncho muyenera kukhala okonzeka. Inuyo mukuganiza kuti satana amafunafuna kuwayesa ndani? Kodi mukuganiza kuti satana amafunafuna kuwapeta iwo amene sakhulupilira mwa mulungu ndipo sanaika chikhulupiliro chawo mwa yesu? Ayi ndithu, iye athu oterewa alinawo kale satana amafunitsitsa kuwayesa komanso kulimbana nawo iwo amene adakali mkati mophunzira kuika chikhulupiliro chawo mwa yesu. Satana alinako kuthekera koyikira tsopano lino kuwagonjetsera anthu amenewa ndikuwakokera kuzilakolako za munthu wawo kotero kuti angathe kuwaononga iwo.

ZOFUNIKIRA KUZITENGA

Pano pali mphindi zomphunzira yofunikira kwambiri choncho ndikudandaulirani kuti masamale (mutchere khutu). Tikuyenera kuchiyesa chimwemwe choposa pamene ife tiri mkuyesedwa. yesu angathe kulola kuti satana akupeteni ndicholinga choti ayese chikhulupiliro chanu. Koma nthawi ino,¹⁹³ popeza tsopano mwazindikira momwe zithu zimzchitikira, mudzapambana munkhondoyi. Mwaphunzira kuti ngati muyesa uthengawu muzapeza kuti chinyumba cha katundu nthawi zonse sichabwino kwa inu ndipo kukhala ndi zonse zokhumba za moyo wanu mwinamwake zingathe kubweresa zowawa zochuluka kwambiri pamoyo. Mwazindikiranso kuti mwini wachinyumba chachikulu cha katundu pamodzi ndi malonjezano ake-kaya ndi okoma motanizidzakusocheretsani inu kulowa m'njira yolakwika. Mwaonetsa chikhulupiliro m'ziganizo zanu, ndipo chifukwa cha chikhulupiliro chanucho mulungu adzaika chidaliro chachikulu mwa inu.

Komatu konzekani. Ngati satana amafunsa yesu kuti akupeteni, ndipo ngati yesu amayankha kuti “inde” kenako ndikupemperera chikhulupiliro chanu, apa ndipamene mayesero anu akubwera kukhala okhwima kwambiri. Kakamiranibe molimba monga ngati muja zikhalira munthu akamapalatsa njinga munseu okumbika-wokhala ndi zitunda. Koma pamene inu muphunzira kuika chikhulupiliro chanu mwa mulungu, ndipo pamene satana awona chikhulupiliro chanu choumbika mwatsopano mwa yesu, satana azaphunziranso kuti inu simuli m'modzi mwa anthu omwe mungathe kunyendedwa mosavuta kotero iye sadzakhalala ndi nthawi yochuluka yoitaya pa inu, moyo udzakahala wophweka kanizani m'dierekezi ndipo iye adzakuthawani

Satana kwenikweni amakonda kupeta atsogoleri. Iye adzawalonda atsogoleri m'banja mwanu, atsogoleri pakati pa abwenzi anu, atsogoleri komwe inu m'magwira ntchito, ndiponso ngakhale atsogoleri ampingo wanu. Satana

amadziwa kuti ngati angathe kunyenga abusa ankhosa ndiye kuti nkhusa zidzakhala zosatetezeka, ndipo pamenepo ndipomwe mimbulu ingathe kulowerera ndikuononga zotsalazo.¹⁹⁵ Choncho ndikofunikira kwambiri inu anthu muzipempherera atsogoleri anu.

CHINYENGO CHENICHENI CHA SATANA-KUNYADA

Muyeneranso kukhala pakuchenjera kwambiri pamene zinthu zikukuyenderani bwino. Pamene zinthu zikuyenda bwino-satana adzayesera kukupatsani maganizo oneka kuti simukusoweke anso mulungu ayi. Inu mukhonza mwina kumathamanga ndi moyo wachipambano pamodzi ndi banja lanu, ntchito yanu, chuma chanu, abwenzi anu, ndipo mu nthawi zonga izi satana azachita chotheka chirichonse kuti inu mukwezeke ndikuyamba kunyada. Iye adzakunyengani inu kuyamba kuganiza kuti simukusoweke anso mulungu ayi.

Pamene zinthu sizikuyenda bwino-satana adzachitanso mwanjira ina. Uthenga wake mu nthawi ya mavuto ndiwakuti mulungu wakusiyani inu. Iye adzayesesa kukunyengani kuti mulungu sangakusamalani konse chifukwa anthu a mulungu sayenera kumavutika ayi. Satana ndi kadaulo posewera ndi bongo wathu (maganizo athu) ndikutipotoza mkuyamba kuganiza molakwika. Iye amadziwa momwe angamugwilisire ntchito zochitika m'malingaliro athu kuti alimbane naye satana adzagwiritsa ntchito mazunzo ena alionse komanso kukaika kuti atipotoze ife kuchoka kwa mulungu, koma zonsezi ndi mabodza ndi chinyengo chabe basi. Iye tikuyenera kupitilira kuyesa maganizo athu komanso mizimu yathu¹⁹⁶ tiyenera kukhala anzeru ku machenjerero ochuluka a satana.

ZILAKOLAKO NDI KUSILIRA ZOMWE ENA ALI NAZO

Chimodzimodzi mwa zofooka zathu zikuluzikulu, ndiponso chimodzi mwa zipambano zake za satana, ndi pamene satana watinyenga ife kuti tikuyenera kukhala ndi zinthu zochuluka-kuti tikhale osangalala. Iye adzayetsesa kunong'ona m'makutu mwathu kunena kuti ena alinazo zambiri (zokwanira), ndipo ifeyo tiri ndi zochepa. Satana adzayetsesa kutipanga mosalekeza ife kukhala osakondwa ndi zomwe tiri nazo. Ndipo chifukwa cha kufooka kwathu kwa umunthu, ngati timumvetsera iye tizatha ndithu kukhulupilira bodza lakeli. Koma inu chonde musanyengedwe. Kukhala ndi zinthu zambiri sikuzatha kukupangani inu kukhala osangalala. Mungowafunsa anthu ambiri omwe amalandilapo mphoto-ambiri aiwo anataya chimwemwe chawo. Kunena zoona, ochuluka a iwo anakhala achisoni. Tikachimwa timakonda kudadza mitima yathu ndi zithu zochuluka, koma zithu zochukuka sizomwe ife tikusowa ayi. Chomwe ife tisoweke kuchita ndiko kudzazitsa mitima yathu ndi mulungu, pakuti tikatero iye adzadzitsa mitima yathu ndi chimwemwe.¹⁹⁷

Mphatso ya mulungu, ikulindira inu, chomwe inu mukusoweke kuchita ndicho kuilandira (kuivomereza). Iye akugogoda pa khomo la mitima yanu. Inu mungosegula mitima wanu ndikumulora kuti iye alowe basi. Inu mukatero iye adzayamba kukubvumbulutsirani chikonzero chake cha pamwamba kwambiri chomwe alinacho pa inu.

KUKONZANSO MTIMA WANU

Mulungu akuienza ife kuti iye adzathandizana naye kutikonza ife zomwe zidzatithadiza ife kudzindikira (kumvetsetsa) chifuniro chake pamoyo wathu. Kukonzanso mtima wathu ndicho,¹⁹⁸ chikonzero chomwe iye alinacho pa ife. Iye tikasankha kukonzidwa kumeneku tidzatsimikizira maitanidwe athu komanso m'banja lake-m'mene sitizapunthwa (kukhumudwitsidwa) konse.¹⁹⁹ Tizaphunzira nthawi zina titatha kuyenda m'miseu yokumbika, kuti kukondwa kwenikweni kungapezeke mwa mulungu yekha basi. Iye adzakudalitsani inu chifukwa chakum'londa iye.

NDITHA KUMAKUMAN NDI ZOVUTA CHIFUKWA CHOTI NDIKUKHALA M'DZIKO LAKUGWA (LOCHIMWA)

SIZINAPANGIDWE KUTI ZIKHALE MOTERE

Dziko lomwe tikukhalamoli ndi lowonongeka momvetsa chisoni; koma sizinakonzedwe kuti zikhale motere ayi. Dziko lathuli ndi lodzaza ndi chisalungamo, kuvulala, nthenda, kuwawitsa bongo, kudwala, chisoni, ziwawa, imfa, kuzunzika, kusweka kwa maubale komanso mauthenga opanda pake oti kulibe mulungu, zoti zichitikire inu komanso mwa kanthawi. Tangoyang'ana kuzungulira kwa dzikoli. Uthenga woti muzidalire nokha uliponseponse: m'manyuzipepala, m'zofalitsira mauthenga, m'ma tv, pa intaneti komanso m'malo ena ambiri. Mauthenga omwe tikusautsika nawo ndikuphatikizapo: ukusowa ichi, udzakhala wosangalala, anthu azakukonda kuposa ena, wina aliyense alinazo komanso ndi ena ambiri.

Kuzera m'kusakhulupika kwa Adam ndi Hava m'dima unayamba kulowerera mtunda wa anthu uchimo womwe tonse tinatengerako m'dima umenewu ukunyekepera-nyekeperabe m'moyo mwathu ndikukhuza maubale athu. M'dima umenewu, womwe umayambika m'munda wa Eden ukuyetsesa kutikokera ife m'moyo wachisoni komanso wopanda cholinga. M'dima umenewu, nthenda imeneyi, njoka imeneyi, ntchimo ili, cholinga chake ndikuononga mtundu wa anthu.

Tikukhala m'dziko lomwe likukhudza kuti, ndizikwaniritse ndekha, ndizikondweretse ndekha komanso ubwino wonse ukhale wanga. Kodi mukukumbukira ulamuliro wa maslow wa zosowa womwe ukuphunzitsidwabe m'masukulu mpaka lero lino? Pa chi inde-inde pa ulamuliro umenewu pamatchedwa kuti "utchenicheni" ndipo umakhuza kuti zonse ndi zanga basi (ine) mukasanthula za uchenicheni umenewu kodi mumaonamo mulungu ngakhale pang'ono kapena cholinga chenicheni? Ai. Zonse zimangokhuza ndi kukhutitsa mimba yako basi. Kudzikhutitsa iwe mwini zikusemphana ndi chikonzero cha mulungu pa moyo wanu. Ichi ndiye chifukwa chake chomwe dziko lathu lero lino lilir lowonongeka. Dziko lathu ndilo onongeka koposa koto kuti anthu ambiri akufunafuna tsiku pamene lizamasulidwe ku ukapolo ndi chivundi zomwe zikutisendereza lero lino ku ukapolo ofuna kuti zonse zikhale zako basi. Nkhani si ine kapena inu ayi, nkhanu ndi mulungu. Iye analenga china chilichonse. Iye akuyetsesa kuulula ndikugawana naye zabwino zake, koma inuyo mukuyenera kuvomereza (kulandira) mphatso yake.

CHIFUKWA CHANI MULUNGU AMALOLA ZOWAWA KOMANSO MAZUNZO M'DZIKO?

Anthu omwe sankhulupilira kuti kuli mulungu-chabwino, ayeneranso kukhulupilira kuti satana kulibe. Sangakhale ndi m'modzi osakhala ndi wina. Kukhulupilira mwa m'modzi ndiku sakhulupilira mwa winayo ndichimodzimodzi kukhulupilira kuti kuli choona kapena cholakwika; kuli kutentha koma kulibe kudzidzira, kungakhale kuunika kapena m'dima. Taonani zoipa mdziko lathuli, ziri ponseponse. kodi mukuganiza kuti zoipa zimenezi zikuchokera kuti? Inu mukungofunikira kuti kutsegule maso anu kuti muone kuti ndindani amene akulamulira dziko lathuli.²⁰⁶ Nanga ndindani amene akupangisa zowawa zonsezi ndi mavuto onsewa m'dziko lathuli. Koma zimenezi zimazesa funso lovuta kwambiri, ndipo funso lake ndi ili: chifukwa chain mulungu akulora zowawa zimenezi ndi mazunzo awa ngati iye alidi wamphamvu pa satana? Kodi kapena mulungu ngopanda mphamvu pa zonse zoipa ndi zowonga za satanazi?

Yankho lake ndilophweka zedi-koma ndi yankho lovutitsitsa kwambiri kulimva. Yankholi ndi ili: ndikupyorera am'masautso amenewa m'dziko lathu lauchimo ndi lakugwali momwe ulemelero wa mulungu ungathe kuwonekera momveka mve mve mvee. Kudzera m'zolephera zathu zochulukaz komanso m'zovuta zathu zankhaninkhanizi pamodzi mkulephera kwathu kosova mavuto athu onsewa m'dziko lapansi, zomwe zimaonetsa poyera kuti mulungu, ndiponso kuti anthufe timasowekera mulungu. Mulungu amadziwa zonsezi ndipo akudikilira. Iye akudikilira kufikira munthu wina aliyense atamva nkhanu yake komanso kufikira uthenga wake wabwino. Iye watuiza ife kuti uthenga wake wabwino uyenera kulalikiridwa kufikira mbali zonse za dziko iye asanathane naye satana.²⁰⁷ Koma pamene tiri mkudikilirabe sitienera kukhala okhumudwitsidwa kapena kumwa kulemedwa,²⁰⁸ pa utsiku yesu anali asanamwalire iye anauza ophunzira ake kuti, m'dziko lapansi mudzakhala nacho chibvuto, koma limbikani mtima ndalilaka dziko lapansi ine.²⁰⁹

Choncho ife tikudikilira...

KUONA MAZUNZO MOSIYANA

Pamene muli kudikilira ndipo chifukwa cha zomwe mulungu amatiuza ife m'baibulo. Komanso zomwe mwazimva ndikuziphunzira m'bukhuli, tsopano inu mulinako kuthekera komvetsetsa mazunzo anu mosiyana ndi mmene inu munali kuwamvetsetsera poyamba:

Mazunzo ndi masautso;

- Adzakunyangani monga golide ndipo adzakupangani inu kukhala amphamvu²¹⁰
- Adzakukonzekeretsani inu kuti mukathe kutonthoza ena.²¹¹ Iwo amene azunzidwa ndi kuona masautso ochulukana ndi omwense amasanduka atonthozi abwino.
- Adzakuthandizeni kuti muyende m'chifupi cha mulungu mwakuya (modzama).²¹²
- Matsautso anu angathe kugwiritsidwa ntchito kuti akhwimitse chikhulupilira chanu.²¹³

MWINA NDIINGATHE KUMAKUMANA NDI CHIFUKWA CHOTI MULUNGU AKUNDILANGA (KUNDIKANZA) INEYO

TIKAMVA MAWU OTI KULANGA, CHITHU CHOYAMBILIRA CHOMWE ANTHU AMBIRI AMAGANIZIRA NDICHOTI mulungu akundikantha komatu pali kusiyana kwakukulu pakati pa kulangidwa (kukonzedwa) ndi kukanthidwa. Taonani m'mene buku latanthauzira mawu (dikishonale ya Webster ikutathauzira mawu awiriwa:

CHILANGO (KUKANTHIDWA)

1. mphoto/malipiro pa mlandu kapena cholakwa chirichonse chomwe munthu wachita
2. m'chitidwe wa kulangidwa kapena kukanthidwa.
3. kuchitidwa choipa pobwezera cholakwa.
4. kuchitiridwa mwakhanza ngati njira imodzi yophunzitsa munthu.

KUKONZEDWA (DISIPULINI)

1. maphunziro kapena zochitika zoikidwa pa munthu ndicholinga choti munthuyo asinthe kuchokera koipa kupita kwabwino pa thupi lake kapena kudziletsa kwa mumtima.
2. maphunziro oyenera pomvera malamulo komanso ulamuliro.
3. makhalidwe a kusinthika kwa chikhalidwe, ndi zina zotero. zochokera m'maphunzitsa amenewa kapena m'zochitikazi.
4. ndondomeko ya malamulo apa chikhalidwe, njira ya machitachita oyenera.
5. nthambi (gawo limodzi) ya maphunziro kapen malangizo.

Nanga kodi kholo labwino lidzasankha chain-kukantha (kulanga) kapena kukonza (disipulini)? Kholo lachikondi nthawi zonse lidzasankha kukonza (kupseka disipulini) m'malo mwa chilango (kukantha), chifukwa disipulini ili ndi maphunziro mkati mawake. Kodi ngati tikunkonda munthu, kodi tyidzalekeranji kumukonza iye? inde, sitikanatha kutero ayi timamukonza munthu chifukwa tikufuna kumusamalira iye. Timawakonza ana athu ndicholinga choti adzakhalenso ana abwino, komanso asalimira athu ena. Timafuna kuti iwo aphunzire m'mene iwo angakhalire odziimira paokha pamenenso ali kugonjera ku ulamuliro. Timafunanso iwo kuti adziwe kuti tikuwalanga iwo chifukwa choti timawakonda. Kodi iwo mukuganiza kuti angazimvetse zimenezi? Ayi ndithu. Chifukwa chain mukuganiza kuti zingatero?

Mwatsoka lake, pamene ana athu ali kukula mopandukira kumalowa. Kupanduka kuli ndi njira yake yodzikuza, ndipo kudzikuza kulinso ndi njira yake kusamvera kwa akulu (ulamuliro)-womwe uli uchimo. Choncho pamene ana athu satimera ife kumeneko ndiye kuchimwako.

Zimenezitu sizosiyana pamene ife sitikumvera mulungu. Pamene ife sitimvera kwa mulungu ndiye kuti pamenepo sitikukhala makhalidwe oyenera molingana ndi mulungu sikumamvetsetseka bwinobwino ayi. Nthawi zambiri sitimakhala odziwa chifukwa chomwe tikudutsira m'nyengo zovuta ngati zimenezi

kapenanso ngati kulangako kuli kochokera kwa mulungu kapena ayi. Zitha kukhala kuti ndi chithu china chomwe chikuchitika chosaululika bwinobwino pachifukwa choti tiri m'dziko iri la chionongoke. Choncho musamatanthauzire chirichonse chomwe chikukuchitikirani inu monga kulanga kochokera kwa mulungu ayi. Mwina samakhalanso mulungu mkomwe. Atha kukhala satana kufuna kukusokonezani inu basi.

MUSAMAWATENGE MAVUTO ANU KUKHALA MONGA GORI AYI-KOMA NGATI CHOKULIMBITSANI CHAUZIMU

Musakhale okhumudwa pamene mulungu akukulangani²³⁰ - koma muzikhala ndi chiyembekezo mwa ambuye ndipo iye adzalimbikisanso mphamvu zanu.²³¹ musamabwerere m'mbuyo m'mayendedwe ake ndi iye chilango cha mulungu nthawi zonse ndi changwiro. Chilango chake sichizaposera muyeso. Sichizakhala cha nkhanza kwambiri komanso chopepuka kwambiri. Chilango chake sichimabwera kuti chikhale gori ayi, koma kuti chipereke phunziro. Chimakonzedwa kuti inu chikulimbikitseni ndipo chidzakupangani inu kukhala othejera kuimanji kutsutsana ndi mayesero ambiri otumizidwa kwa in u ndi oipayo.

Kuti muthe kuthana ndi masautso ndi chimwemwe chamu mtima muyenera kupitirira kufunafuna kumvetsetsa cholinga cha mulungu m'kusautsidwa kwanuko. Inutu munalengedwa ndi cholinga ndipo uwu umakhala m'dalitso wanu-inde, m'dalitso-kuti mupeze chomwe chiri. Musawatenge mavuto anu monga gori ayi, koma monga ngati cholimbikitsa chauzimu kutakatsa chikhulupiliro chanu ndicholinga choti mukule kusunthira chifupi ndi mulungu. Pamene inu mulimbikitsa chikhulupiliro chanu mudzayambanso kuumba machiri auzimu, ndipo pamene machiri auzimu anu adzachelukirachulukira kukhala olimba, pameneponso mudzakhala othejera kuyamikira ndiponso kuthokoza chomwe mulungu akukuchitirani m'moyo wanu-angakhale mukumva kuwawa chifukwa chilango chakecho.

MULINGO/MUYESO WA MULUNGU NGOTANI?

Musalore kuti maganizo a anzanu asokoneze chiganizo chanu

Pamene muli munkhawa ndi kukaika nthawi zonse tsatirani bukhu la malangizo lotchedwa kuti baibulo. Pakuti m' buku lake la malangizo limeneli, mulungu akutiiza kuti, chifukwa chipata chiri chachikulu, ndi njira ya kumuka nayo kukuonongeka iri yotakata, ndipo ali ambiri amene alowa pa icho. Pakuti chipata chili chopapatiza, ndi ichepetsa njirayo yakumuka nayo, kumoyo, ndimo akuchipeza chimenecho ali owerengeka.”²³²

Ndiye apa pali funso lofunikira kwambiri: kodi ndi chipata chiti chomwe inu mukufuna kulowerapo? Yankho lanu ku kufunso lofunikira bkoposali liliri ndi zotszira zake zonka muyaya ngati mungalakwitse pama lankhulidwe a funso limeneri mungathe kuzanzuzika moyo wanu wonse-choncho kungakhale koyenera kuti mutenge maola angapo a nthawi yanu kusanthula chiganizo chomwe mungathe kupanga. Ndipo musaganizire kuti mukapanda kupanga chiganizo ndiye kuti mukuchita chisankho cha nzeru ayi. Sinzeru. Kusapanga chiganizo-ndiye kupanga chiganizoko onetsetsani kuti mwawerenga zomwe ichi

chikutanthauza. Pamene muli kuganiza chiganizo chanucho ndikofunikira kuti musalore malangizo a abwenzi anu kuti achotse chiganizo chanucho. Tingathe kunena kuti pafupifupi zonse zomwe mwakhala mukumva kuchokera kwa abwenzi anu sizokhala pa choonadi cha mulungu ayi (pokhapokha ngati bwenzi lanulo amalidziwa baibulo bwinobwino). Chomwe muyenera kuchimvetsetsa ndichakuti satana samafuna kuti inu mukhulupilire kunena kuti palidi dongosolo muyeso la mulungu lomwe inu mukuyenera kukhalira moyo wanu-chifukwa cholinga cha satana ndichokupangani inu kukhala mbuli ndicho cholinga chake. Pali liwu limeneli loti “mbuli kachiwirinso. Ngati munaiwala kuti kodi kukhala mbuli (kapena umbuli) ndi chani bweleraninso ku mutu 1 ndikuwerenga tanthauzo lake lachiwiri. Tathaunzo lake ndila chionongoke chachikulu, tanthauzo lake limatitsutsa ife kwambiri ndife mbuli ngati tikhale osowa chidziwitso ndi maphunziro a baibulo, kapenanso ngati tikhala osadziwisidwa kapena osadziwa za chomwe baibulo limakamba. Ili ndi dera limodzi lomwe inu simusowekera kuti mukhale osadziwa. Mwina mutha kusankha kukhala osadziwa kusoka zovala kapena kuyendetse njinga kapena momwe mungazalire maluwa kapena kuphika koma simufunika kukhala mu umbuli inu, baibulo ndilo mawu ake. Kumbukirani-satana anakondwera kwambiri pamene ife tikhala mu umbulu pa za mulungu, pamodzi ndi mphamvu zake. Satana akugwira ntchito mosalekeza pa wina aliyense kuphatikizapo abwenzi anu. Choncho musamawam, vere abwenzi anu amene amakonda kukupatsana inu malangizo pa nkhani zina ndi zina pokhapokha ngati maganizo awo ali molingana ndi malemba. Malemba ndiwo choonadi. Maganizo mochulukira Sali choonadi ayi. Makhaliidwe a mulungu cholinga chake ndi kupulumutsa. Makhaliidwe a satana nthawi zonse cholinga chake ndikukuchotsani inu pa choonadi cha mulungu. Ngati satana angathe kukudzadzani inu ndi maganizo a bwenzi anu-ndithu iye adzagwiritsadi ntchito mwayi umenewo.

Satana adzadzazanso maganizo anu ndikukaika zomwenso mwina mwake ndizomwe ndikukuchitirani sopano lino monga ngati, “n’chifukwa chani ndikusowekera nkupanga chiganizo sopano lino? Ndingathe kudikira kaye. Mwina mawa ndingathe kuganiza mosiyana” icho ndiye chimodzi mwa zinyengo zikuluzikulu za satana-kutiunjikira iye kukaika. Musalole kuti satana apambane. Palibe chikaiko china chilichonse kuti inu ndinu cholengedwa cha mtengo wapatali, cholengedwa ndi mulungu wapa mwamba kwambiri, ndiponso kuti mulunguyo alindi chikonzero (pulani) chachikulu pa inu. Koma muyenera kutsegula mtima wanu ndikumulola iye kuti alowe. Mutsalore kuti kunyada kwanu kukutsekereni khomo. Musalole kuti satana apambane nkondo iyi yakukaika (chikaiko). Makhaliidwe amulungu akhazikika pa choonadi chake-omwe ndi olondola komanso oipa ndi zabwino za umunthu sizikhuzana nawo. Tikuyenera kupeza mayankho kumafunso ofunikir kwambiri a moyo wathu. Kuchokera m’buku lake la malangizo lomwe ndi baibulo. Wina aliyense yemwe azamva mawu ake ndikwagwiritsa ntchito ali ngati munthu wamzeru amene anamanga nyumba yake patanthwe.²³³

KODI INU MUKUKHALA MOYO WOTSOGOZEDWA NDI NAMLONDOLA?

Panonso pali funso lofunikira kwambiri lomwe inu mukuyenera kuzifunsa nokha-ndinso kuyankha. Kodi inu m’makhulupilira baibulo ndi mawu a mulungu? Yakho lanu ku funso ili silidzangotengera kokha momwe in u m’malionera baibulo ayi, yankho lanu lizatengeranso kuti kodi inu m’makhulupilira mu ulamuliro wa mawu

a mulungu komanso ngati kapena inu bukhu limeneli ndi namlondola wa moyo wanu.

Ngati inu m'makhulupilira kuti baibulo ndi mawu a mulungu ndiye kuti mudzafuinitsitsa kuliwerenga, kulidalira komanso kulimvera ngati musankha kukhulupilira baibulo si mawu a mulungu, apo ndiye kuti moyo wanu udzakhala osunthika-suthika ndi maganizo a watnthu komanso mabodza awo-womwe uli mtundu wachikhulupiliro umene satana amaufuna kuti inu mukhale nawo. Kukhala m'chikaiko kuti siriri mawu a mulungu komanso kuti baibulo ndichoonadi zidzapangitsa kuti woipayo akuchotseni pa m'busa wanu-komwe mimbulu idzakunongani. Zoonz zake n'zakuti inu mudzakhala moyo wanu wonse popanda chiongolero mawu a mulungu pamodzi ndi chifuniro chake chapa moyo wanu zingathe kukhala chiongolero chanu-chokusungani inu kukhala chifupi ndi m'busa wanu.

Mwana wa mulungu, yesu sananena kuti m'malemba (monga baibulo) muli mawu a mulungu ayi. Yesu ananena kuti malemba ndi mawu ake.^{234 235} ndipo mtumwi Paulo anatichenjrdza ife kuti sitiyenera kuwonjezera pachimene chalembedwa.²³⁵ Ngati inu mukhulupilira zimezezi ndiye kuti baibulo liyenera kukhala mulungo wanu momwe inu muyenera kukhalira moyo wanu ndipo simuyenera kuwonjezerako, kapena kupambanitsa ku chomwe chalembedwa. Izi zitathauza kuti ngati bwenzi ayesera kukukopani inu kunena kuti, chabwino chitani china chake powonjezera "mwina mwake" kapena "nthawi zina" kapena ngati ena akuchita izi, ndiye kuti zilibwino" kumawu ena ake a m'baibulo (mwachitsanzo ngati ntchimo lina lake), kumeneko ndiko kuwonjezera kuchimene mulungu wanena-zomwe sitiyenera kutero. Kuonjezera mawu ku baibulo ndicho chithu chomwe woipayo amayetsesa kuti atifikitsepo-kuonjezera chinthu chomwe mulungu wachitanthauzira kale m'mawu a iye mwini. Kodi ndi mawu andani omwe inu mukufuna kuti muwatsatire? Muzaona kuti mulungu sanagwiritsepo ntchito mawu oti "mwina mwake" kapena, "nthawi zina" kapena, "nkutheka" kapena, "zingatheke kutheka."

Kawirikawiri. Mulungu Sali ofuna za chisawawa ayi. Ngati inu mufuna kukhala ofuna za chisawawa ndiye kuti mwina simunali kutsatira ndondomeko za mulungu. Ndipo sopano lino mukudziwa chomwe izi zikutanthauza.

Baibulo-monga momwe lalembedwera lero l. ino-liyenera kukhala liwu lotsiriza pa zonse zokhuza zikhulupiliro zathu pa zokhuza kodi chenicheni m'chiti pa uchimo komanso momwe tinayenera kukhalira miyoyo yathu.

KUZIKA ZONSE M'MAWU AMODZI

Pali maumboni ambiri otsimikizira kuti baibulo, choonadi ndi mawu a mulungu. Umodzi mwa iwo ndikuvomerezana kwake komwe pamodzi (umodzi wake). Ngakhale kuti lapangidwa m'mabuku osiyanasiyana okwana 66 olembedwa m'nthawi yokwana zaka 1500 ndikuwonjezerapo, m'ziyankhulo zitatu zosiyana komanso komanso lolembedwa ndi alembic opitilira 40 amene anachokera m'zikhaliidwe za miyoyo zosiyanasiyana, baibulo ndi buku lokhalo lolumikizana pamodzi kuyambira pachiyambi mpaka pamathero. Koma monga buku lina lili lonse, muyenera kuika mutu woyamba ndi mutu wotsiriza komanso mutu wina uliwonse mkati mwa nkhani pamodzi nmdi unzake. Simungathe kuchotsa

kandime kamodzi kapena tsamba (peji) kuchokera m'mabuku 66 amemewa ndikulitcha kuti limenelo ndi yankho. Choonadi chisizachokera minkhani yonse ya mthunthu ya malemba amenewo pamodzi nawo china chirichonse cholembedwa m'baibulo.

Imodzi mwa njira zophweka kwambiri kuti munthu atsutsane ndi chimenechi ch baibulo, kapena kuti atsutsane ndizomwe baibulo limanena zokhuza mutu/nyundo ina yake, ndiyo kusankha vesi kapena ndime inayake. Ndikuyamba kunena, ichi chomwe baibulo likunena pa zokhuza nkhani yakati yakati....." Kuika ndime kapena vesi ya m'baibulo pozisokhanitsa zonse pamodzi ndi mawu onse a m'baibulomo ndichithu chofunikira koposa kuti munthu kumvetsetsa chomwe mulungu akufotokoza zokhuza mutu umenewo. Baibulo ndi buku ka nkhanu zophatikizana pamodzi ndiponso likathe kumveka bwino ngati muli mvetsetsa monga mfundo imodzi.

Komanso anthu ambiri amalankhula kuti pali kutsutsana pakati pa chipangano cha kale ndi chitsopano. Kunena zoonadi ndikosavuta kusegula baibulo ndikungowerengamo kandime kamodzi ndi kuyamba kunena, "zimenezozizingatheke mpang'ono pomwe" kapena, kapene ndime imeneyi ikusephana ndi zomwe zalakhulidwa m'chipangano chakale icho ndiye chifukwa chomwe ife tisowekwera kuwerenga baibulo lonse kuti tithe kumvetsetsa bwino nkhanu yonse yaziphunzitsa za mulungu. Nthawi zina ndime kuoneka ikunena zithu zopita m'chipangano chakale ingathe kumvetsetseka bwino m'chipangano chatsopano. Inu muyenera kuwerenga baibulo lonse lathunthu kuti nmthe kupeza uthenga wonse komanso tanthauzo la zomwe zaphunzidwa. Ndikofunikiranso kumvetsetsa kuti chipangano chatsopano sichipangitsa kuti chipangano chakale chikhale chenicheni ayi. Chipangano chatsopano chimakwaniritsa zomwe zafotokozedwa m'chipangano chakale. Muyenera kuwerenga chipangano chakale chonse pamodzi ndi zonse zomwe zafotokozedwa m'chipangano chakalecho, ndipo komanso muwerenge chipangano chonse chatsopano pamodzi ndi zonse zomwe zafotokozeredwa m'chipangano chatsopanocho kuti mupeze choonadi chathunthu komanso changwiro chokhuza phunziro liri lonse. Chonde, musatenge kulakwitsa kongotengera chilichonse cha ziphunzitsa za mulungu m'chipangano chakale ndikuchikhulupilira kuti ndi choonadi cha thunthu. Mwina zingathe kukhala choncho ayi. Werengani chipangano chatsopano kuti muone ngati mulungu watsiriza mfundo zake, phunziro lake, komanso choonadi chake pazokhuza mutu umene mukufunawo.

MA ULOSI OKWANILITSIDWA

Njira ina yotsimikizira uchenicheni wa baibulo ndiyo kuona ma ulosi wopezeka m'menemo-makamaka m'chipangano chakale. Muli mazana-mazana amaulosi wolankhulidwa pa zokhuzan tsogolo la mizinda, zomwe tiyenera kuyembekezera zokhuza matsoka ndi zoopsa, komanso tsogolo la mtundu wa anthu. Komanso pali mazana-mazana a maulosi a m'chipangano chakale omwe akwaniritsidwa m'chipangano chatsopano. Okhuza iye amene adzawera kuzakhala nape pakati pathu komanso iye amene adzabwera kudzakhala mpulumutsi. Ma ulosi onsewa amakwaniritsidwa monga momwe mulungu analankhulira kuti adzatero (kudzera mwa aneneri ake), ndiponso alipo ochuluka omwe alinkuza onetsetsani kuti mwawerenganso buku linzake la ili lomwe mutu wake ndi "tsopano ndi nthawi"-Now it's time). Buku lina limeneli lidzakuzindikiritsani za zomwe zili mkudza-

zimene tonse tiyenera kudziyiwa. Mukawerenga maulosi onsewa, pali maulosi oposera 300 okhuza yesu m'chipano chakale, anthu ambirir amayetsa kuti yesu wangotchulidwa m'chipangano chatsopano chokha basi, (monga kubadwira modiyera....). Koma chipangano chakale chalankhula zambiri zokhuza yesu. Chipangano chakale chinalosera za m'zinda womwe yesu adzabadwiremo. Chipangano chakale chinalosera za mbumba yomwe iye adzabadwireko. Chipangano chakale chinalosera za momwe yesu adzalowere mu m'zinda wa yerusalemu m'matsikuotsiriza a iye (monga pokwera bulu). Chipanganonso chakale chinalosera zokhuza momwe iye adzafero pogwiritsa ntchito chizunzo chomwe chinali chisanakonzedwe mpomwe pa nthawiyo (mwachitsanzo kupachikidwa).²³⁷ Ndipo chipanganochi chinalosera kuti iye adzauka kwa akufa patatha matsiku atatu. Zonsezi zinalotseredwa kwa ife mwatsatanetsatane zaka mazana ambiri zithu izi zisanachitike.

Chipangano chakale chinalankhulanso mwachimvekere kuti imfa ya yesu pamtanda idzakahala pangano lake latsopno.²³⁸ Iomwe lidzapulumutse ife ku machismo athu. Kudzera mwa aneneri ake iye anauza anthu mazana-mazana kuti iye adzabwera kudziko lapansi, kudzakahala pakati pathu, kutifera ife, ndiponso kuti adzalilaka dziko lapansi²³⁹ ndipo izi ndi zomwe zinachitikadi. Pali njira iana iliyonse yomwe mungathe kufototozera ma ulosi ambirimбири a m'chipangano chakale womwe amakwanilitsidwa n di ungwiro wodabwitsa kwambiri kuposera kunena kuti maulosi onsewa anaperekedwa mwa umulungu wa kale lomwe. Palibe buku lomwe limaphatikidza chidzalo ndi ungwiro za kulosera kwa uneneri womwe ukupezeka n'chipango chakale. Palinso umboni wathupi (wonekera) umene umanenetsa kuiti baibulo ndilo mawu a mulungu. Umboni wa anthu wochita kafukufuku watsimikizira kuti matsiku (madeti) a m'baibulo ndi enieni pomwe zolembe zinapezeka pafupi ndi Nyanja ya m'chere (pafupi ndi Qumran ku Israeli), komanso pamodzi ndi zochitika zochulukira zomwe zinachitika m'nyengo za matsiku omwewo. Zizokhazi ayi, komanso maumboni a onse ochita kafukufuku pamodzi ndi zonse zolembnera zomwe zimatsimikizira zomwe zinalembedwa m'baibulo kukhala buku lokhala ndi mabuku ena onse. Mfundo zoyenera kuti baibulo lafotokozera bwino mbiri ya zochitika ndi umboni wa ukulu wa choonadi chake.

Ungwiro wa alembic a baibulo nawonso umapereka umboni wa chenichei cha bukuli. Onse a ophunzira ake a yesu anasiya mabanja ndi ntchito zawo kutsatira iye. Wina aliyense wa iwowa antha kumenenyedwa, kumangidwa ndende, komanso ambiri a iwo ankatha kuphedwa polengeza chomwe amakhulupilira-kuti anakhulupilira kunena kuti yesu anali mulungu. Kodi ndi anthu angati omwe inu mukuwaziwa kuti akanatha kutsatira munthu wina wake kwa zaka zitatu ndipo pambuyo pake kusankha kuwafera iwo ngati iwo sanathe kukhulupilira za iyeyo? Pachifukwa choti ophunzira ake a yesu anali ofunitsitsa kufa chifukwa cha chomwe iwowo ankhulupilira zikutsimikizira kunena kuti amuna amenewa anakhuluolira kunena kuti anasogozedwa ndi mulungu.

MATANTHAUZILIDWE A MULUNGU PA UCHIMO SANASINTHE AYI

Pamene yesu anafa pamtanda iye analipira mlandu wa iwo onse amene anachimwa-omwe ndi tonse a ife. Komano izi sizitanthauza kuti onse omwe amatsatira iye ndi angwiro ndipo kuti sangathe kuchimwa ayi. Ngati inu muvomereza machismo anu ndikumufusa yesu kuti alowe m'mitima mwanu

muzapulumuka ndipo ndithu palibe ntchimo liri lonse la mtsogolo lomwe lidzatha kukubwezani inu kulowa kumwamba. Pamene yesu anakuferani chifukwa chamachimo anu, iye anafera machismo anu onse-akale, atsopano ngakhale amtsogolo mwanu. Komabe tisowekera iye kuzindikira chikhaliidwe chathu ch uchimo ndi kuvomwereza kwa mulungu kuti ndife ochimwa. Pamene timva kutsutsika mkati mwathu izi ndi chifukwa choti timamva manyazi pa zomwe tzhitira ndiponso kunena kuti tadziwa kuti tsiku lina tidzawerengedwa m'landu pa machismo athuwo.^{240 241 242} Tchimo silikhala tchimo chifukwa chongoti tayedwa ayi. Tchimo limakhala tchimo pamene ife tigonjere ku kukuyesedwako ndipo tichita monga mwakuyesedwako²⁴³ yesunso anayesedwa koma iye sanachimwe ayi.²⁴⁴ iye sanakuze zokhumba zake kuposera zokhumba za mulungu ayi. Imfa ya yesu pamtanda inaimilira nsembe yathunthu, yangwirow, komanso yokwanira pamachimo onse amene ife tinachitapo, kuphatikizapo iwo amene ife sitinathe kuwachimwa konse.^{245 246}

Kodi ife timasowekera kusiya machismo athu kuti tipulumutsidwe? Yankho ndiloti ayi, koma timasowekera kuwazindikira iwo chomwe iwo ali-ndi machismo ndithu. Machismo ndiwo kuphwanya kwa ndondomeko ya mulungu. Chenjerani kusanyalanyaza machismo anu ndikumanena kuti chomwe inu mulu kukitacho sichoipa ayi, kapena kuti popeza wina aliyense amachita zoterezo, kapenanso kuti malamulo a mulungu anatha ntchito. Malamulo (ndondomeko) a mulungu samasintha ayi. Tchimo ndi tchimo basi. Tchimo lomwe linali zaka zikwi zapitazo ndi tchimo ngakhale lero lino. Anthu ambiri amakhulupilira kuti ndondomeko ya mulungu simayenera kusintha kuti zipereke mpata wogwirizana ndi nthawi. Koma ndondomeko za makhalidwe moyenera a mulungu samasintha ayi. Ngati china chake chinali tchimo m'chipangano chakale ndiye kutinso ndi tchimo m'chipangano chatsopano. Chinali choipa zaka 2000 zapitazo ndipo chikali choipa kufikira lero lino. Motsutsana ndi opanga malamulo a lero, mulungu samasintha maganizo kapena kusintha maganizo ake.²⁴⁷ malamulo a mulungu amaima chiimire ndipo osasintha,²⁴⁸ iwo anakhazikitsidwa ndipo adzakhala chimodzimodzi kunthawi zosatha.²⁴⁹

Mwina ino ingathe kukhala nthawi yabwino yotsegula baibulo ndikuphunzira zomwe likunena, sikuti ndi buku longodzadza ndi zoti izi muzichita" ndipo izi musamachite" ayi, bukuli ndi buku lodzazandi nzeru zapamwamba zedi. Linapangidwa kuti lipange moyo wanu kukhala wosavuta. Baibulo limapereka mafototkoziedwe a moyo wa iwe munthu, banja lako pamodzi ndi dziko lonse kupereka mayankho a mavuto ons liri lonse la iwo. Werengani buku la malangizo zonse ziri m; menemo.

Kodi timakhala molingana ndi malamulo a mulungu motani?

Kuti tikhale molingana ndi ndondomeko ya mulungu tiyenera kukhala monga mwa mzimu osati monga mwa thupi ayi.^{250 251} Tiyenera kumamvesera ku uzimu wa mulungu wokhala mkati mwathu pamene tizatha kugonjetsa chikhaliidwe chathu cha uchimo, apo ayi ndiye kuti sitizatha kukhala monga mwa ndondomeko za mulungu pa ife tokha. Tidzayetsesa, koma sitizalephera. Tiyenera kumvetsa kunena kuti malamulo a mulungu amapangidwa kuti atisunthe ife komanso kutipanga ife kukhala ozindikira kuti ndife ochimwa.²⁵² tikuyenera kuvomereza choona chakuti tidzakhala nthawi zonse ndi maganizo ochimwa, kuchita zinthu zochimwa, ndipo tingathe kupuluka pokhapokha

mwakukhulupilira kuti mulungu anadza kudzko lino la pansi kudzatipulumutsab ife. Yesu akufunanso kuti ife tidziwe kuti kumvera malamulo ake m'chipangano chakale kudakali kofunikira kwakukulu chifukwa m'chipangano chatsopano akuiphunzitsa kuti "chifukwa chake yense wakmasula limodzi la malangizo amenewa ang'onoang'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwechi, adzatchulidwa wam'ng'onong'ono mu ufumu wa kumwamba; koma yense wakuchita ndikuphunzitsa awa, iyeu adzatchulidwa wamkulu mu ufumu wa kumwamba." ²⁵³

Matsiku otsiriza-ambiri sadzakhulupilira, choncho musawatsatira anthu amenewo

Mtumiki Paulo akutichenjedza ife m'buku la 2 Timoteo 4: "pakuti idzafika nthawi imene sazalola chipulumutso cholamitsa, polowa mkhutu adzaziunjikira aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzaludza dala pa choonadi, nadzapatukira kusata nthawi zachabe"

MUTU 4

Ndinapangidwa-Kuti Ndidziwe Cholinga chachikulu cha Mulungu

Kuvumbulutsa Pulani Ya satana

Pamene mulungu anaika Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni ndikuwauza iwo kuti asadye za Ku mtengo uja wakudziwitsa zabwino ndi zoipa.²⁵⁴ Ndipo pambuyo pake Satana ndikumunyenga Hawa kuti zonse zidzakhala bwino kwa iwo akadya chipatso chochokera ku mtengo umenewo, uku kunali kupambana koyamba kwa satana kunyenga mtundu wa anthu.²⁵⁵ Pamenepo ndi pomwe Mulungu amachotsa ulamuliro wolamulira dziko lapansi kuchokera kwa Adamu ndi Hawa ndikupereka kwa satana.^{256 257} Ndipo satana wakhala ali kutinyenga ife kufikira lero lino.

Komatu Mulungu ankadziwa kuti zimenezi zidzachitika.

Mulungu amamangika m'mau ake. Pamene mulungu amapeleka ulamuliro wa dziko lapansi kwa satan, zimampanga iyeyo kukhala wothekera kumusakasaka munthu. Ichi ndiye chifukwa chake kuli mazunzo m'dziko lathu lero lino. Ichi ndi chifukwa choti satana pamodzi ndi ziwanda zimzake ali ndi ulamuliro wa pa dziko lapansi lomwe ife tili kukhalamo - kutinyenga ife, kutivulaza ife, komanso kuyeserera kutiononga ife. Satana amadziwa kuti iye amagonjetsedwa chifukwa

amaona Chigonjetso cha Yesu, pa mtanda paja komabe iye adakali ndi nthawi ina yake yakuyesera kuwatengera anthu ku gahena pamodzi naye.

Mulungu amadziwa zonse zokhudza satana chifukwa mulunguyo ndiye amene amamulenga satanayo. Satana ndi m'modzi wa angelo akuruakuru a Mulungu amampatsa satana zimphamvu zodabwitsa zochuluka kotero kuti satana amafuna kukhala Mulungu, koma sizinatheke. Choncho satana anapandukira. Iye anapandukira pochita chothekera chilichonse kuti asocheretse angelo ena kumtsatira iye. Ndipo ndithu anaterodi. Iye amasocheretse pafupifupi theka la chiwerengero cha angelo ndi kumtsatira iye.²⁵⁸ Koma iye popeza satana sangathe kumuononga Mulungu, Zoonadi, wotsatila wake ndiye inuyo, ndi ine. Satana amafunitsitsa anthu chifukwa choti iyeyo tinalengedwa m'chifanizo cha Mulungu.

Choncho, pokhala ndi satana wothekera kunyenga anthu pa dziko lonse lapansi ndiponso ndikuthekera kusocheretse anthu kuwachotsa kwa m'busa wathu, komanso pokhala ndi anthu okhala ndiponso chikhaliidwe chochita chifuniro chawo ndi kulowera kulikonse komwe iwo afuna mwa zokhumba zao-nanga cholakwikanso nchiyani? O, m'nyamatawe, ungate kumva momwe mmbulu ikukhetsera dovu pa iwe.

Mtundu wina wake wakusakanikirana koipa, sichoncho? Izitu zili ngati akatswiri a mpira kusewera ndi tiana tophunzira kusewera. Simpikisano waukulu kodi?

Satananso naye ndi mzimu wamuyaya-zomwe zitanthauza kuti satana angathe kunyenga anthu kufikira muyaya ngati ataloredwa kutero.

Wo, Ichitu ndi Choipa zedi.

Anthu ndiwosavuta kunyengedwa ndipo satana ndi kadaulo wodziwa kuchita bodza, kotero kuti satana akathe kunyenga mtundu wonse wa anthu- wosatha. Kodi ndi osewera achichepere ati omwe angathe kupambana akatswiri odziwa kusewera? Siambiri ai.

Chabwino, palibe.

Sikovuta nkomwe kunyenga anthu. Kuwapanga anthu kukhala ongodzikwaniritsa okha ndi zokhumba zao zathupi ndikumawauza iwo kuti palibe choipa chomwe chidzawagwere. Kuwapanga anthu kukhulupirira kuti tingathe kuphwanya malamuro a mulungu ndipo palibe yemwe angathe kudziwa. Kuwapanga anthu kukhulupirira kuti kukhala ndi zochuluka. Chuma chambiri kudaztipanga ife kukhala okondwa kwambiri. Kuwapanga anthu kukhala kukhala okhulupilira kuti ngati chomwe uli nacho sukuchikonda, kungochitaya basi ndikuyambiranso, kuphatikizapo maukwati, ana, maubale ndi zina zambiri. Kuwapanga anthu kukhulupirira kuti bola zanga zikuyenda, zilibe kanthu kaya

zikipweteka enapalibe vuto. Ndiponso makamaka kutumiza anthu kwa ife omwe ali ndi maganizo akuya kuti ayesere kutinyenga ife kulowa n'kuganiza kuti maganizo aowo akupangitsa kuphwanya kwa malamulo a mulungu chinthu choyenera.

Kukhala mu umbuli

Mwa mve mve mve, kumpatsa satana ulamuliro waulere pa mtundu wonse wa anthu ndi kumulora iye kukhala pa malo oyenelera ndi anthu onse kuti athe kuwanyenga. Koma osawauza mkomwe anthu zokhudza chionongeko chomwe chidzakhalapo pambuyo pake pakuchimwa - mazunzo, chisoni, kusautsika, kusweka kwa maubale, ndikugwira njakata. Ndiponso kwenikweni osawauza anthu kunena kuti chitetezo cha mulungu chidzachotsedwa pamene iwo achimwa chifukwa mulungu ndi woyera ndipo sangathe kuthandiza anthu ochimwa.

Ilitu ndilo bodza lankunkhuniza la satana. Kulora satana kuwakhulupiritsa anthu kuti adziyenderere ndi kusochera, ndiponso kuti anthu adzimumvetsera iye. Anthu alowerere kupita kutali kusiyana ndi mtetezi wao ndipo iwo amavulala. Pambuyo pake satana amawauza iwo kuti Mulungu wawataya iwo. Ndipo pambuyo pakenso anthu-monga alili aumbuli ochuruka, a iwo-sangathe kuunikira chifukwa chomwe iwo ali kuvutikai sakutha kuzilumikiza nkomwe.

Iwo ali ngati nkhoa zomwe zasocheretsedwa kwa m'busa wao ndipo osatha kukhala nayo nzeru zakuzindikira kuli anali m'busa wao yemwe anali kuwatetezera iwo. Atatha kuzungulidwa ndi mimbulu, kwete-sangathe kuzindikira chomwe iwo analakwitsa.

Satana amakondwera nazo pamene anthu akhala mu umbuli wokhuza mulungu pamodzi ndi mphamvu zake. Tatiyeni tikhale chete pang'ono ndikulingalira kuti kodi umbuli ndi chani.

Liu lofotokozera za chinthu china chake kapena munthu:

1. Kusowekera kwa chidziwitso; kusaphunzira.
2. Kukhala osautsidwa: wosadziwa.
3. Chifukwa chosowa maphunziro kapena kuonetsa kusadziwa.
4. Kusowa chidziwitso kapena uphungu pa chinthu chinachake.
Monga mungathe kuona kuti, sichabwino kukhala mbuli pa za mulungu komanso mphamvu zake izi ndi zomwe satana amakondwera nazo.

Angelo omwe satana anawanyenga kuti amtsatire iye, timawatchula kuti angelo oipa, ziwanda-chifukwa cholinga chawo ndicho kuononga. Iwowo ndi ziwanda, kutanthauza kuti oipa. Satana amamuda mulungu kwambiri kotero kuti iye

adzachita chotheka chilichonse chomwe angathe kuti anyenge ndi kuononga china chirichonse komanso zonse zopangidwa m'chifanizo cha mulungu. Ife sitingathe kuona angelo oipa amwenewa chifukwa ndi mizimu, komatu mizimu imeneyi ili ponseponse. Cholinga chao ndichofuna kuti monga ifeyo. Tangoyang'anani m'manyuzi pepala kuti muone momwe iwo akupambanira. Mudzatha kuvomereza kuti zoonadi iwo akupambana kwambiri. Simungathe ngakhale kumvera nkhani zochitikazo kwa mphindi imodzi popanda kuona momwe satana pomodzi ndi ziwanda zake atangwanidwira kuononga china chake, komanso chirichonse.

Ichi ndiye chifukwa chake nthawi zonse anthu akamachita china chake chomavulaza iye, kapena anthu ena, satana amabisala pakona kumalankhula kwa iye mwini, “Ya, ndinam'nyenga wina wake!” satana amaomba lipenga pamene wanyenga munthu kuti adziphe yekha, ndipo nthawi yomweyonso kuwapha ena m'chikhaliwe chakechi. Pamene izi zichitika satana amakhutitsidwa kunena kuti zolengedwa za mulungu zikuphedwa kumbali zomwe.

Koma mulungu amadziwiratu pachiyambi pomwe kuti izi zidzachitika - Ndipo anali ndi chilinganizo (Pulani). Inde chilinganizo changwiro.

Pulani yaikulu ya mulungu

Kodi anali m'munda muja ndani?

Timadziwa kuti mulungu ndi mzimu ndipo mizimu sioneka, nanga, anali kuoneka ndikumayenda yenda komanso kulankhula ndi Adamu pamodzi ndi Hava m'munda wa Edeni pa nthawi yomwe, Adamu atangochimwa ija anli ndani?

Kumbukirani pa Genesis 1 pomwe akunena kuti, “Tiyeni tipange munthu m'chifanizo cha chathu; monga taphunzirira m'mutu woyamba, “tiyeni” ndi “chathu” m'ndime imeneyi akutanthauza.

1. Mulungu atate
2. Mulungu mwana, yemwe ali yesu, ndiponso
3. Mulungu mzimu woyera, choncho pamene mulungu anati, “Tipange munthu m'nchifanizo chathu” - iwo onsewa anali pomwepo pamene munthu anali kulengedwa.

Izi zitanthauza kuti ngati yesu analipo pamene munthu ankulengedwa zingathe kukhala kuti anali yesu yemwe anali kuyenda komanso kulankhula ndi Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni muja. Ndiye kuti mwina mwake sanali Mulungu Atate yemwe anali m'munda muja chifukwa cha zomwe ophunzira a Yesu adalankhula kwa ife.

- Timoteo akutiiza kunena kuti palibe angathe kumuona Mulungu²⁶¹ ndiponso
- Yohane anatiza ife kuti palibe munthu yemwe amaona Mulungu Atate ndi kale lonse²⁶²

Yesu wakhala ali woimilira Mulungu nthawi zonse pansi pano- kuonekera m'malo mwa iye komanso ngati iye. Ndi zachimvekere Kuchokera m'malemba kuti yesu ndi Mulungu Atate ndi amodzi.²⁶³

Izi zikutanthauza kutisizangokhala zotheka kokha, ndi zachidziwikire ndithu kuti analidi Mulungu m'nchionekedwe cha thupi - yesu - yemwe anali kuoneka ndiponso kulankhulana ndi Adamu ndi Hava, ali kuyendayenda m'munda wa Edeni muja, Adam atangochimwa. Ngati Timoteo ndi Yohane akulondola kunena kuti palibe munthu yemwe anamuonapo mulungu Atate ndi kale lonse, ndiye kuti mwina anali yesu (monga kuti Mulungu m'thupi) yemwe anali m'munda wa Edeni muja pamene adam adachimwa.

Dongosolo (chikonzero) yapamwamba kwambiri

Ngati izi ziri zoonza, kodi izi sizingakhale zomveka kuti Adamu ndiponso mwina mwake yesu anali m'munda wa Edeni pamene Adam anayamba kugwa kwa mtunda wa anthu kuzera mukuchimwa kwake, ndiponso kuti yesu anali ali pomwepo mu nthawi yomweyi kuti apulumutse mtundu wa anthu ndi dongosolo lakelo?

Zochitika ziwiri zonsezi zinayenera kuchitikira limodzi mu nthawi yofanana m'mundamo apo ai ndiye kuti mulungu analakwitsa. Mulungu anadziwiratu kale lomwe kuti satana adzanyenga Adam m'munda muja (kumbukirani, kuti izi sizovuta ai) ndiponso iye anadziwiratu kuti adzayenera kukhala ndi dongosolo m'malo mwake pa nthawi yomwe Adam anachimwa kuti atipulumutse ife ku machimo athu.

Izi zitanthauzanso kuti mwina mwake anali yesu amene anali m'munda, yemwe anadziwiratu pompo pompo kuti Adamu anachimwa kutinso iye adzayenera kutifera ife. Pa mphindi yomweyo pomwe panali uchimo, panalinso yankho lake. Pa nthawi yomweyonso yomwe Adam anachimwa, Yesu anadzipereka yekha monga mpulumutsi. Zonsezi inali mbali imodzi ya chikonzero chachikulu cha mulungu.

Mwana sakuyenera kuchita kanthu kalikonse kuti akalowe kumwamba

Chikonzero (pulani) chimenechi m'munda wa Edeni chikutanthauzanso kuti mwana aliyense wobadwa m'dziko lapans amakhala kale ali ndi mphulumutsi mwana sabadwa m'dziko lapansi atatsenza chiweruzo cha uchimo ai, koma kudzera m'chikondi cha mulungu pamodzi ndi chisomo chake komanso imfa ija Yesu pa mtanda mwana amapulumsidwa.²⁶⁴ Mwana sasowekera kuchita kanthu kena kalikonse kuti akalowe kumwamba. Ndipokhapokha pomwe mwanayo ayamba kudziwa kuchita uchimo, pamene adzasowekera kufunsa chikhululukiyo cha mulungu- kupyolera m'chikhulupiriro chake mwa yesu - kuti apulumutsidwe.^{265 266 267}

Yesu sakadatha kugonjetsa satana komanso tchimo mpaka atafa pa mtanda, koma nkhanu yonse inali idakali yosungika. Dongosolo (pulani) lake la chiombolo linali litakhazikitsidwa.²⁶⁸ Yesu anadziwiratu kuti sakadatha kubwera ku dziko lapansi kudzakhala nsembe ya zochima zathu mu nthawi ina iliyonse cha posachedwa chifukwa choti iye amasowekerabe kutipatsa ife malamulo ake khumi aja.

Kutipatsa ife malamulo ake khumi zaka mazana ochuluka mtsogolo mwake kunali ndi chifukwa kotero kuti tikathe kuphunzira kuti sitikadakhonza kuwapsira mosavuta malamulo amasowekera kutisutsa ife²⁶⁹ komanso kutipanga ife kukhala wolakwa.

Tinasowekera kuphunzira - kunena kuti tinasowekera mpulumutsi.

Chionongo chachikulu chisinthika (chibwezedwa)

Chikonzero cha Mulungu m'munda wa Edeni chikutanthauzanso kuti Adam komanso wina aliyense yemwe adzakhalepo pambuyo pa Adamuyo sanasiidwa angakhale mphindi imodzi pansu pa chilango cha uchimo komanso chitsutso. Pa mphindi yomweyo yomwe Adamu anangochimwa, yesu anali pomwepo kutipulumutsa ife ku zochimwa zathu.²⁷⁰ Pali mulingo umodzi wokha basi-tikusowekera kuphulupilira mwa iye. Tikusowekera kukhulupilira kuti Yesu anabwera ku dziko lapansi kudzapulumutsa ife ku machismo athu. Ichi ndi chikonzero cha ngwiro, chokonzedwa mwa ungwiro, ndipo chochitidwa mwa ungwiro ndi Yesu. Iye tikungosowekera kukhulupilira basi.

Chikonzero changwirochi chinakonza vuto la mtundu wa anthu wokhala pansu pa chiweruzo komanso m'chiopsezo chachikulu cha chionongo. Pulani ya yesu m'munda muja kothelatu inasinthia chionongo chomwe Adamu, kuzera mu uchimo wake, chinapekedwa kwa wina aliyense wa ife.

Choncho Mulungu anadziwiratu kuti satana adzapanduka, ndiponso anadziwiratu kuti Adam adzachimwa. Koma ngakhale anadziwiratu zonsezi iye

anawalengabe iwowa-chifukwa kuchimwa kwa mtundu Wa anthu komanso kupandukira kwa satana zonsezi chinali chikonzero chachikuru cha mulungu kuti akathe kuonetsera ulemelero wake. Izi zikutanthauza kuti ufulu wathu wakuchita chifuniro komanso kuchimwa kwa anthu ndiyo njira yomwe mulungu amaonetsera ulemelero wake komanso chifuniro chake chimachitika. Ndipo chikonzero cha yesu kudzafa pamtanda ndicho chinthu china chomwe ndi mbali imodzi ya chikonzero chachikuru cha Mulunguyo.^{271 272}

Yesu sanabadwe chifukwa choti kuchimwa kwa Adamu kunapangitsa vuto losaoneka ai

Ubale uwu wa pakati pa mulungu ndi anthu- kudzera mwa Yesu-sinani pulani B ya Mulungu ai. Yesu sanabadwe pa chifukwa choti kuchimwa kwa Adam kunapangitsa vuto losaoneka ai, lomwe linayenera kuti likonzedwe. Monga zananedwera m'buku la Aefeso, Mulungu nthawi zonse kuyambira zokhala m'nthupi:

Aefeso 1: 4 Monga anatisankha ife mwa iye, lisanakhazikike dziko lapansi, tikhale ife oyera mtima, ndi opanda chirema pamaso pake m'chikondi. 5 Anatikonzeratu tilandilidwe ngati ana a iye yekha mwa Yesu khristu, monga umo kunakomera chifuniro chake, 6 Kuti uyamikidwe ulemelero wa chisomo chake chimene anatichitira ife kwaufulu mwa wokondedwayo.

Kodi wina angathe kusankhiratu bwanji mtundu wa anthu kuti akhale ana ake kuzera mwa yesu ngati yesuyo sanali woti adzakhale munthu pokhapokha ngatinso Adamu adzagwa mu uchimo Ai, sizingatheke.

Izi zikutanthauza kuti anthu ambiri amachepsa (kunyoza) malo a yesu md'ongosolo la Mulunguli. Kubwera kwa Yesu ku dziko lapansi chinali chikonzero cha mulungu kuchokera pachiyambi pomwe dziko lisanakhazikike, adamu kulibe pamodzi ndi Hava.²⁷³ Mulungu sanangovumbuluka mwadzidzidzi kuti akhale mu utatu wake m'chipangano chatsopano ai. Mulungu Atate, Yesu pamodzi ndi mulungu mzimu woyera si ndondomeko yatsopano ya utatu wa ummulungu womwe Mulungu anaupanga ndicholinga choke akonze vuto la kugwa kwake kwa mtundu wa anthu ai. Kubwera kwa Mulungu ku dziko ku dziko lapansi chinali chikonzero cha mulungu choyambayamba ndipo kunalibenso chikonzero china ai.²⁷⁴ Yesu ndi Alefa ndi Omega.²⁷⁵ Yesu anali ali pa mseu kale wobwera kudzakhala thupi (mwa chitsanzo, kudzakhala ngati munthu), pamene Adamu linali lingaliro chabe m'maganizo a Mulungu.

Mulungu anakhala munthu kuti akwanilitse cholinga chake cha muyaya

Choncho, kodi mumachokako bwanji kwa kugwa kwa munthu.

Kodi wina aliyense anayenera kupita ku Gehena chifukwa cha machismo ao- Kwa anthu kolowa kumwamba ndi kukakhala ndi Mulungu? Njira yake ndiyozera ku imfa basi; Mulungu amafuna nzerube ya machismo athu. Yesu sanabwere ku dziko kudzafa kuti adzamsinthe Mulungu ai lye anabwera ku dziko kudzatifera ife ndicholinga choti ifeyo tisinthe. Lye sanapachikidwe pa mtanda paja kuti adzatonthoze mkwiyo wa atate ake ai. Lye anapita ku mtanda kuti aitanire ku mtunda wakugwa wa anthu komsanso kudzazima (kuthetsa) kusocherea kwawo kuchokera kwa Mlengi woyera. Lye anapita ku mtanda kukakhala msembe ya machismo athu.²⁷⁶

Ichi ndicho chinali chikonzero cha Mulungu kuyambira pachiyambi pomwe.

Kugwa kwa mtundu wa anthu Chinali choyembekezera ndi Mulungu. Mulungu anakhala munthu kuti akakwanilitse cholinga chake cha muyaya- Kutitenga ife kulowa m'banja lake kuzera mwa mwana wake, Yesu. Tiyenera kukhulupilira kuti Yesu anabwera ku dziko lapansi kudzakhala chifukwa cha ife, ndi kufa chifukwa cha ife, kuti tikhala mwana wa mulungu.

Satana akutumikira pa cholinga cha Mulungu

Podziwa kuti zonsezi zinali zoyembekezereka, kodi zikutanthauza kuti satana mwa njira ina akukwanilitse cholinga cha Mulungu?

Yankho ndi loti inde. Satana ndi wonyenga, koma siwanzeru ai. Lye sangathe kusanthula momwe angathanire ndi chikonzero changwiro cha Mulunguchi ai. Kuyesetsa kwa satana kuti aononge inu ndi ine zoonza zake kumabala zipatso zosemphana. Mulungu amadziwa kuti anthu adzatsendera chifupi ndi iye pamene mazunzo afika m'moyo mwao. Masautso athu, pamene tili kusautsidwa ndi satana, amaloredwa ndi Mulungu. Ndipo kupyolera m'kuyesetsa kwa satana kotu aononge inu ndi ine. Mulungu amapindula ubale wabwino kwambiri ndi ife - chomwe iye amafuna!

Izi zikuonetsa kufunikira kwa udindo waa satana wochitachita m'chikonzero cha Mulungu. Mulungu amagwiritsa ntchito satana komanso tchimo kuti akwanilitse cholinga chake chachikuru. Mphamvu za satana zimapatsidwa kwa iye ndi Mulungu ndipo ndi thandizo la Mulungu lomwe limalora satana kuchita zomwe amachitazi. Satana ali ndi mphamvu zakutikhudza - koma motengera ndi chilolezo cha Mulunguyo.

Koma angakhale Adamu ndi Hava anachimwa m'munda muja, izi sizitanthauza kuti Mulungu ndiye gwero la uchimo ai. Kapenanso sizitanthauza kuti Mulungu anamuyesa Adamu ndi Hava Kuti achimwe ai. Mulungu samayesa wina aliyense ai.²⁷⁷ Lye amangogwiritsa ntchito satanayo kuti zilinga zake zikwanilitsidwe.

Mulungu amagwiritsa ntchito satana kuti abweretse chilango pa ana ake (disipulini). Satana amaloledwa kuchita chokhacho chomwe Mulungu anachikonza ku ulemmero wake, komanso ku ubwino wathu. Kuzera m'kutsutsa kwa satana ku Malangizo a Mulungu-zolinga za Mulungu zimakwaniritsidwa. Titatha kuzunzika chifukwa cha machismo athu ndi kusamvera Mulungu anatibwezeretsa ife ndikutipanga kukhala a mphamvu, oima nji, Komanso osateketseka.²⁷⁸ Mazunzo athu amabala kukhala nako kudalira pa Mulungu.

Zonsezi zikutanthauza kuti mokhwima momwe satana adzachitira potsutsana ndi uthenga wabwino, mochurukiranso kwenikweni iye amathandizira uthengawu. Mulungu analingilira kupeza kwa satana pamodzi ndondomeko za mulungu kuti akakwanilitse chikonzero chachikuru cha Mulungu.²⁷⁹ Mu china chirichonse chomwe satana amachita, ndiponso kuloledwa kuchichita, zoonza zake ndi zoti iye akutumikira Mulungu.

Kodi Mulungu woyera angakhoze bwanji kukhala ndi uchimo m'mapulani ake?

Taganizirani za ichi. Ulemelero wa Mulungu umaonetsedwa kwathunthu polora uchimo m'dziko lapansi.

- Kukhala ndi tchimo m'dziko lapansi kumalozeka chifundo komanso chisoni za Mulungu.^{280 281}
- Kumalozeka Mulungu kuti aonetsera Chikondi chake komanso chikhululukiro cha machismo athu.²⁸²
- Kumalozeka Mulungu kuti aonetsera Chilungamo chake Komanso mkwiyo wake kwa iwo omwe akumkana iye.²⁸³
- Ndiponso, kudzera mwa satana, zimaonetsera kuti Mulungu salekelera olakwa kuwalanga²⁸⁴ monganso momwe khoti lili lonse la pansi pano limachitira.
- Mulungu kwenikweni amalemekezedwa potsutsa uchimo kufikira Gehena.

Ma khoti athu sakadakhala odalilika ngati sakanati adziwatsutsa anthu olakwa ndi kuwaweruza kuti apite kundende. Choncho makhoti athu amakhala olemekedwa odalilika mwa chigamulo chao cha pa anthu omwe amaphwanya lamulo. Izi zitanthauza kuti mkwiyo wa Mulungu umalungamitsidwa ndiponso Mulungu amalemekezedwa pamene apereka mpata kuti Munthu akhululukidwe, ndipo munthu akana mpatawo.

Izi zitanthauzanso kuti pambali pa satana pamodzi ndi zochita zake zonse zoipa.

Pali Mulungu woyera wachifundo ndi wolungama yemwe amapangitsa kuti zinthu zonse ziwachitire ubwino iwo amene amkonda iye omwe aitanidwa molingana ndi cholinga chake.²⁸⁵

Mulungu anakonza chikonzero chaulemelo chomwe chikuphatikiza ndondomeko yomwe ikukwanilitsa cholinga chake chachikuru. Cholinga chake chamuyaya ndicho kuti atengere ife m'banja lake kupyorera mwa yesu. Si wina aliyense yemwe angathe kulowamo ali iwo okhawa omwe angakhulupilire ndiwo.

Izi zitanthauza kuti mkwiyo wake pamodzi ndi chifundo chake zimaonetsera ulemelo wake - ndipo simungathe kukhala ndi chirichonse cha izi ngati palibe kugwa mtundu wa anthu.

Kuzunzika kwathu ndiyo njira yomwe Mulungu amatikonzero ife kukhala angwiro

Ichi ndicho chikonzero chake kuyambira pa chiyambi. Mulungu anasankha kulora uchimo komanso mazunzo m'dziko lapansi chifukwa iye amafuna ubale ndi ife. Iye amafuna ife kuti timdziwe iye komanso ndi chifuniro chake.²⁸⁶ Amafuna kuti ife timkonde iye.²⁸⁷ Iye amafuna kuti iye tidzitsamira (kudalira) pa iye.²⁸⁸ Amafuna kuti ife tikhale ndi chikhulupiliro mwa iye.²⁸⁹ Amafuna kuti ife tidzitsatira ndondomeko zake.²⁹⁰ Ngati ife tingamachite zinthu zonsezi iye adzatidalitsa.

Kutilora ife kuti titedsedwe ndi satana ndipo pambuyo pake kutilora kuti tikumane ndi zowawa zomwe zimatsatira zikhumbo zathu, zoipazo, zimatitsendelera chifupi kwa Mulungu. Mulungu angathe ngakhale kulorera kuti inu muonongekeretu kwathunthu - chifukwa, iye amatikonda ife kwambiri. Iye adzalora kuti inu mutute zomwe munafesa.^{291 292} Kuti akukokereni chifupi ndi iye.

Monga momwe munaphunzilira m'mutu woyambilira, tiyenera tidzimwa kudalitsika pamene Mulungu atilanga ife chifukwa zimatanthauza kuti iye amatikonda ife.^{293 294} Ngati sikunali kuti amatikonda sibwenzi akutilanga ife ai. Mayesero athu pamodzi ndi masautso athu ndiyo njira imene chikhulupiriro chathu chimatsimikizidwa.²⁹⁵ Choncho kunena mwatchutchutchu, kuzunzika kwathu ndiyo njira yomwe Mulungu amatilungamitsira (kutipanga angwiro) kutilimbisa, komanso kutiamba kuti tifikire pa muyeso womwe angathe kutigwiritsa ntchito²⁹⁶ zomwe zidzatipanga ife kuima chiimire. Mayesero omwewo amene satana amatiikamo kuti ationongere - Mulungu amawatembenuza kukhala chinthu chabwino.

Kodi mukukumbukira mutu woyamba kuti satana amayenera kuyamba wafunsa kaye, yesu asanayambe kutiyesa ife?²⁹⁷ Imeneyi ndi gawo limodzi la chikonzero cha Mulungu chachikuru kuti aumbe chikhulupiliro chanu mwa iye, ndikumlemekeza Mulungu.

Ndingathe kum'dziwa Mulungu, zoon?

Kutsindikizidwa ndi Chizindikiro

Inde, mungathe kum'dziwa mulungu pamodzi ndi chifuniro chake. Kunena zoon, Mulungu amafuna kuti inu mudziwe chifuniro chake.²⁹⁸

Kum'dziwa Mulungu ndicho chifukwa chomwe tinabadwira ndicho chikhalidwe cha kupezeka kwathu (Kukhala kwathu ndi moyo). Palibe munthu ndi m'modzi yemwe amene ena angopezeka pamodzi pano popanda cholinga kapena pulani. Mulungu anatisankha ife dziko lisanalengedwe kuti tikhale oyera komanso opanda banja pamaso pake.²⁹⁹ Mwa iye tinasankhidwa, atatha kutasankhiratu monga mwa chikonzero chake cha iye amene achita zonse molingana ndi cholinga cha chifuniro chake kutero kuti ife amene tinali oyambilira kuika chikhulupiliro chathu mwa christu tikathe kukhala tamando la ulemelero wake.

300

Koma kuti tikm'dziwedi Mulunguyo ndi kuphunziradi mapulani ake a pa inu ndi ine, Tiyenera kulapa machismo athu ndikukhulupilira kuti Mulungu anamtuma mwana wake - Yesu kudzatifera ife. Mukadzipereka Ndiponso kukhala Wokhulupilira mwa Yesu mumatsindikizidwa ndi chizindikiro mwa iye ndipo Mzimu woyera wa Mulungu adzakhala mwa inu.³⁰¹ Mzimu woyerayo ndiye amene adzakhale nkhoswe yanu amenenso adzakuthangatilani inu kuchitira umboni za Mulungu.³⁰² Mzimu woyeranso adzakuphunzitsani inu zinthu zonse ndipo adzakukumbutsani inu zilizonse zomwe Yesu analonjeza.³⁰³

Chifukwa chomwe inu munabadwira

Anthu ambiri amakhala moyo wautali kwambiri koma osatha kudziwa kwambiri koma osatha kudziwa chifukwa chomwe iwo anabadwira. Yankho ndi ili; Kuti mumdziwe Mulungu. Mulungu anakulengani inu kuti mum'dziwe iye. Pamene inu miuchimvetsetsa ichi, moyo wanu ungathe kuyambira pamenepo. Mudzakhala pa mtendere. Mungathe kukhala ndi chimwemwe. Kufunafuna tanthauzo la moyo wanu kudzatha. Ziyembekezo zanu zoti kodi moyo "ukhale wotani" mwakunamizidwa kwanuko, zonse zidzachoka osaonekeranso. Mudzakhala afulu, ndipo izi zidzakupangani inu kuti musangalare ndi chomwe inu muli komanso dongosolo lomwe inu mudzayendemo. Chidzakhala chisangalalo chanu, choncho gwiritsani zimenezi.

Mulungu adzakumasulani inu molingana ndi chisomo chake basi. Palibe ngongole zili zonse zoti mubweze ai. Palibe magoli, palibe ntchito zogwira. Palibe malipiro. Sipasowekekeranso chopeleka ai. Palibe ntchito yosowekeka kuichita. Palibe china chilichonse choti inu muchite kuti chongosowekekeranso ndi choti mumvomereze Yesu, Mphatso yake yaulele ndipo pambuyo pake

muyambe kusangalala ndi Chifukwa chomwe inuyo munabadwira, chomwe chiri kumdziwa Mulungu. Ndipo pamene inu muika kudalira kwanu mwa mulunguyo. Iye akulonjezakukusamilirani inu, ndipo iyenso akulonjeza kukupatsani inu zokhumba za mtima wanu.

Tsopano muli ndi kuthekera kolowa mwachindunji kwa Mulungu

Chinthu chachikuru chokhudza kum'dziwa Mulungu ndicho kuti palibe kuchitapo kanthu kalikonse. Palibe chirichonse choti inu muchite. Yesu anachita chothekera chiri chonse m'malo mwanu pamtanda. Chinachilichonse pamene anafa pa mtanda chigonjetso chotheratu china chitika pa satana ndipo satanayo ankadziwa izi. Iyi ndiyo pulani yomwe inaikidwa m'malo pachiyambi pa nthawi, kuyambikira m'munda wa Edeni, ndipo kutsilizikira pamene Yesu anafa pa mtanda paja ndi kunka kwa akufa.

Yesu anagonjetsa satana ndipo anagonjetsa tchimo. Ndipo kuzra mwa izi zonsezi Mulungu analemekezedwa.

Pa mphindi yomweyo yomwe Yesu anamwalira pamtanda nthawi yomweyonso chinsaru chotchinga polowera ku malo opatulikitsitsa chinang'ambika kuyambira pamwamba mpaka pansi. Mulungu anaching'amba ndi imfaya Yesu pamtanda chikonzero cha Mulungu chinatsirizika, ndipo kung'ambika kwa chimsalu chachikuru chimenechi unali umodzi wa mauthenga ambirimbi a Yesu kwa onse a ife. Imfa ya Yesu pamtanda inachotsa chotchinga anthu chimenechi- chinsalu chopangidwa ndi anthu chomwe chinali chosiyanyitsa pakati pa anthu ndi Mulungu. Pong'amba chinsaluchi Mulungu anali kuti uza ife Kuti, "simulinso okhala kunja ai. Mwana wanga yesu wapanga njira kwa inu kuti mukhale ndi malowedwe a kwa ine. Bwerani mulowe. Ine ndikudikira inu.

Ndikuchoka kwa chinsalu chimenechi inu simukusowekeranso kuzera mwa wina aliyense ai kuti mukafikire Mulungu. Palibe anthu. Palibe zoikika. Palibe zotchinga. Nyumba ina yake yapadera-dera. Palibe chomwe chaima panjira ai. Mungathe kulankhulana ndi mulungu tsopano lino, mu mphindi yomwe iwo kuli konse komwe inu muli. Kumbukilani, mtima wanuwu ndilo khomo lomwe Mulungu adzagwiritsa ntchito kuti alowe ai. Iye adzadikira mpaka inu mutatsegula kuti iye alowe. Iye adzagogoda (kukhudza mtima wanuwu, mwinanso mkutheka kuti akugogoda tsopano lino), ndipo adzayembekezera kuti inu muyankhe inu tangomlalani kuti alowe. Iye adzalowa ndithu ngati mudzamalora kuti alowe. Mutu 5 udzakuphunzitsani momwe mungamlolere kuti iye alowe- onetsetsani kuti mwauwerenga mutu umenewu.

Ichi ndicho chinali chikonzero cha Mulungu kuyambira pachiyambi pamene anatuma mwana wake yesu kudziko lapansi kudzakha ndikudzatifera ife. Kudzera m'chikhulupiliro chanu mu zomwe Mulungu analankhula kuti zidzachitika m'chipangano chatsopano - Mulungu angathe kukhala limodzi ndi

inu tsopano lino. Mulungu komanso Mlenzi wa dziko lonse angathe kukhala nanu tsopano lino. Koma muyenera kukhulupilira inuyo.

Yesu anabwera ku dzikolapansi kudaziulula chomwe iye ali ndiponso kudziatiza momwe tingakhalire ndi ubale ndi iye. Mulungu ndi m'modzi komanso wa muyaya koma amakhala mu ubale wa utatu: Mulungu Atate, mwana wa Mulungu (Yesu), komanso mzimu woyera wa Mulungu. Pamene dziko linkalengedwa, onse atatuwa anali pamenepo. Pamene Yesu anakwera kumwamba pafupifupi patatha masiku makumi anai chiukireni iye kwa akufa, anasiya mbuyo Mzimu wake kudakhala mkati mwa iwo amene akhulupilira³⁰⁵ ³⁰⁶ choncho mzimu wake ungate kutsogora ife ndikutilondolera ife mu chirichonse chomwe ife tichita.

Mulungu watipulumutsa ife tonse osati chifukwa cha zomwe tachita, kapena chomwe tikadatha kuchita ai, koma chifukwa cha chifundo chake basi.³⁰⁷ Ndi kupyolera m'chikhulupiliro chathu pamodzi ndi chifundo chake basi kuti timapulumutsidwa.³⁰⁸ Mulungu mu utatu wake onse amakhala mu umodzi wangwiro, kutipatsa ife moyo, kutilowetsa ife m'banja la Mulungu, ndikutipatsanso chiyembekezo pamodzi ndi tsogolo.

Nzeru yosasanthulika ya Mulungu

Kaya inu muvomereza kapena ai-wina aliyense wa ife amalengedwa ndicholinga choti akamfunefune iye amene anawalenga tonse tapangidwa kuti tikazindikire kuti kodi Mulungu ndi ndani ndiponso kuti tikapeze kukwaniritsidwa pamodzi ndi chimwemwe mwa iye. Ichi ndiye chifukwa chomwe ife tinabadwira. Iye anatipanga ife tonse kukhala osiyanasiyana³⁰⁹ kotero kuti tikathe ku mfuna ndikum'dziwa kuti kodi iye ndi ndani.

Nzeru yosasanthulika ya Mulungu ndi yachionekere mu china chirichonse chomwe tingachione pansi pano, Kumwamba kuthambo, komanso m'madzi a pansi panyanja. Chifukwa cha zonse zomwe Mulungu wazilenga zomwe zingathe kuoneka bwino lomwe pamenepo tiribe chowiringula pakudziwa chomwe Mulungu ali.³¹⁰ Mukadakhala othekera kuyang'ana a mkati mwa thupi la munthu ndi makina aja otchedwa maiko loskopu, mukadaona makina odabwitsa kwambiri ndi zithunzi ting'onoting'ono - tokhala ndi magiya komanso zoyendetsera ndi zina kuti zinapangidwa ndi m'misiri waluso lodabwitsa koposa komanso Mlenzi.

Mverani izi: Pali Vidiyo pa You Tube.com yomwe mungathe kuionetsa maselosi(cells) a munthu omwe ndiodabwitsa kwambiri a makina a minofu ya m'thupi-okhala ndi magiya ndi ma shaft oyendetsera ndi zina zambiri Ngati china chilichonse cha zimenezi chikadasowekerapo pa tsiku la kulengedwa kwa izo, sibwenzi pano tilipo lero lino. Vidiyoyo ndichotchedwa kuti "Micheal Behe-

Lee Strobel - Molecular Machines Disprove Evolution”

<https://www.youtube.com/watch?v=MNR48hUd-Hw>

Ngati muli pa kompyuta pamene mukuwerenga nukuli Mungopanga kiliki (click) pa webisaiti iri pamwambayi (mwina mungathe kufunikira kuti muthabwanye batani lanu la CTL) ndi kumaonera ndikusangalala. Ngati simukuwerenga bukuli pa kompyuta onetsetsani kuti mwaionera vidiyoyi mwai ukapezeka.

Anthu onse analengedwa kuti adziwe Mulungu ndiponso kukhala ndi kuthekera kozindikira kuti iye alipo. Anthu onse angathe kufika pa malo omvetsetsa bwino lomwe zokhudza nzeru yosasanthulika ya Mulungu kuzera pa kuphunzira masamu (Mathematics), sayansi, zounikaunika pamodzi ndi zina zambiri. Tangoyang'anani pa kachinthu kophweka monga tsipe la udzu ndipo muyesere kulingalira mozama za chozingwa chomwe chiri mu tsipe la udzu limenelo. Zimatengera ukadaulo wochuruka komanso maluso ochuruka kuti munthu athe kufotokoza kukwanira komanso kuthekera kwa kaphikidwe ka chakudya mzomera (photosynthesis) zomwe zili mtsipe limeneli. Cholinga cha Mulungu potipatsa madera odabwitsa amenewa a dongosolo la chilengedwe ndi choti akathe kugwira chidwi chathu koterokuti chidziwitso chochuluka chokhuza iye.³¹²

Mulungu adzakuzindikilitsani inu njira ya moyo

Mulungu waikanso umuyaya mmitima mwanu-zomwe zikutanthauza kuti kukhumba komwe ife tiri nako kofuna kumvetsetsa chomwe Mulungu ali sikungalowerane m'malo ndi china chiri chonse. Nagti inu mutayesera kudzalitsa chikhumbo chimenechi ndi china. Chilichonse osati Mulungu ndiye kuti mudzatsiiredwa ndi maganizo opanda kanthu. Ichi ndiye chifukwa chake anthu ambiri amadabwa pamene akula nsinkhu (akalamba) ndikunena “kodi zimenezi ndi zonse zomwe zinalipo basi?”

Kwa anthu ochuruka ichi ndi chifukwa choti iwo sanaitanire mulungu mu mtima mwao. Mulungu akugogoda - inu chofunika ndikungotsegula ndi kumlora iye alowe. Iye akufuna agawane nanu zabiwino zosayerekezeka. Koma mukuyenera kumlora iye kuti alowe. Iye sangadzivumbulutse yekha kwa inu pokhapokha mutamtsegulira mtima wanu. Lekani kudzisanthulira zinthu zomwe kwa inu nokha. Tangoyambani kunkhulupilira iye basi. Iye adzakupangani inu kudziwa njira yake ya moyo.³¹³ Pakuti Mulungu atiuza ife kuzera mwa mneneri wake Yesaya kuti; “Pakuti maganizo anga Sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutali ndi dziko lapansi, momwemo njira zanja ziri kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu”.

Komatu osaiwala kuli mphamvu ina yake md'ziko mdzina la satana yemwe anafunitsitsa kukusungani inu kuti musaphunzire chomwe Mulungu ali satana amadana ndi Mulungu kwambiri koterokuti amafunitsitsa kuononga china

chirichonse komanso zonse zomwe zapangidwa n'chifaniziro chake cha Mulunguyo-ndipo zimenezi ndikuphatikizapo inuyo. Cholinga cha satana ndicho kufuna kukunyengani inu, kukusokonezani, kudetsa maganizo anu,³¹⁴ kuononga zokhumba zanu³¹⁵ kupangitsa zofunika zanu kuti zigwe pansi³¹⁶ zomwe zidzatelodi, ngati inu mutamumvera iye, kukuchiritsani kukhala wopanda phindu kotero kuti Mulungu mwiniyo angathe kusankha kudzitalikitsa yekha kwa inu.³¹⁷ Musalore zimenezi kuti zichitike kwa inu ai. Kumbukirani, satana amakondweretsedwa kwathunthu pamene anthu akhala mu umbuli pa za Mulungu. Pamene ife tikhala mu umburi, apa ndi pamene pomwe miyoyo yathu siikhala ya ife eni, tidzakhala olamuliridwa ndi satanayo.

Ngati ife tidzitcha kuti ndi anzeru mwakukana kuti Mulungu alipo, samasandulika opusa^{318 319 320 321} ndipo kuposera apo timasandulika adani a Mulungu amene timatha kudziwa kuti zoterezi ziri mumtima mwathu. Kumbukilani, malamulo a Mulungu alembedwa m'mtima mwathu. Kudzera mu ufulu wanu wochita chifuniro, mudzatha nthawi zonse ndi kusankha zomkana mulungu. Icho ndiye chisankho chomwe Mulungu wanu wokondeka anakupatsani inu³²² Ngati Mulungu akadaumiliza kuti inu mudzimkonda iye- ndiye kuti sakadakhocha kukhala ndi ubale weniweni ndi inu.

Inde, Mungathe kuzindikira chidziwitso cha Mulungu

Mukamvomeleza Yesu kulowa mumtima mwanu simudzakhala othekera kuyandikira chifukwa kuti iyeyo adzakhala ali nkati iyeyo adzakhala ali mkati mwanu kale.³²³ kuzera m'chikhulupiliro chanu mwa Yesu Khristu mudzakhala ndi chidzalo chonse chothekera kulowa kwa mulungungati³²⁴ mumuvomereza yesu ndikusunga malamulo ake mkati mwanu, kutchera khutu lanu ku nzeru komanso kugwiritsa ntchito malamulowo. Mumtima mwanu kufukira kukuzindikira, ngati zudzapempha chidzindikiritso ndikuchira ndipo ngati zudzafunafuna siliva, ndikuifunafuna monga mukanafunira chuma chobisika, pamenepo mudzazindikira kuopa ansunge ndipo potero mudzamvetsetsa mvemvemve ndikudzindikira chidziwitso cha mulungu.³²⁵

Aefeso 1: ¹⁸ndikunena kuti maso a mitima yanu awalitsike, kuti mukadziwe inu chiyembezo cha kuitana kwake n'chiyani; n'chiyandinso chuma cha ulemelero wa cholowa chake mwa oyera mtima,¹⁹ ndi chiyandinso ukulu woposa wa mphamvu yake ya kwa ife okhulupilira, monga mwa machitidwe a mphamvu yake yolimba,²⁰ imene anachititsa mwa kristu m'mene anamuukitsa kwa akufa, naikhazikitsa pa zanja lake lamanja m'zakumwamba ²¹pa mwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina lililonse lotchedwa, si m'nyengo ina yake ya pansi pano, komanso mwa iyo ikudza; ²²ndipo anakonza zonse pansi pa mapazi ake, nampatsa iye akhale mutu pamtu wa zonse, ²³kwa Eklesia amene ali thupi lake m'dzadziwe wa iye amene adzadza zonse m'zonse".

Kukhulupilira popanda kuona

Kulumikizana pakati pa kumwamba ndi dziko la pansi

Ndipo imfa ya yesu pamtanda ndiyo ulusi umene kudzera mwa iwo kumbuyo ndi kutsogolombali zonse zachulukana pamodzi, ndipo monenetsa, yesu ndiye thonje la chikonzero chonse chathunthu cha mulungu.³²⁶

Popanda yesu tonse tikanakhoza kukodwa ku mbali ya kumbuyo kotheratu-mbali yoipitsitsa kwambiri. Popanda yesu sitikanathanso ife kufunafuna mbali ya kutsogolo ai. Yesu akutipatsa ife madutsidwe a ufulu opita kutsogolo ndipo palbe chilichonse chomwe ife tikhoza kuchita kuti tikafike kumeneko. Ife tikungosowekera kukhulupilira basi. Tikungosowekera kukhulupilira kuti ulusi wachikonzero chachikulu cha mulungu mwana wake, yesu, ndipo kuti kudzera mu ulusi umenewu yesu ndiye njira yathu yotifikitsa kumbali ya kutsogolo kumene tidzaone dongosolo lalikulu la mulungu-komwe ndi kumwa.

Momvetsa chisoni monga mbali ya m'mbuyo iliri lomwe ndi dziko lathu. Lolamulidwa ndi satana ndi dziko, mulungu akupereka chozizwa kwa yense wa ife amene tikukhala m'moyo wa mayesero ndi zopsyinja. Iye anagwiritsa ntchito mavuto ndi zipsynja zathu kuti alimbitse chikhulupiliro chathu mwa iye. kunzera m'zipsynjo ndi m'mavuto ndimomwe iye amasimikizira chikhukupiliro chathu³²⁷ Mayesero omwewa amene satana amagwiritsa ntchito kuti ationonge ife (monga ngati mbali ya kumbuyo ija), mulungu anagwiritsa ntchito ngati chiombolo chathu,³²⁸ m'kukonzekera kwathu za ufumu wake (monga ngati mbali ya kutsogolo ija). Tidzafikira kumbali ya kutsogolo ija kudzera m'chikhulupiliro chathu cha mwa yesu, ndipon yesu yekhan basi.

YESU NDIYE ULUSI WA CHIKONZERO CHACHIKULU CHA MULUNGU

Mwatsoka sitingathe kuona mbali ya kutsogolo ya mulungu bwino lomwe-kufikira tsopano. Tiyenera kukhala ndi chikhulupiliro kuti dongosolo lomwe liri kutsogolo ndilokongola koposa monga momwe iye akunenera kuti ndikotero. Koma ngakhale kuti sitingathe kuona dongosolo lalikulu lokongolo la mulungu patsogolo iye watipatsa ife mfundo zambiri zachikonzero chake. Mfundo zakezi, zomwe zili pena paliponse m'baibulo, zimatipatsa ife kuunika kokoma kotilowetsa m'mbali ya kutsogoloyi m'mene imaonekera. Mfundo zake zikufotokoza kuti iye adzapukuta misozi yathu yonse ndipo sipadzakhalanso imfa, kapena kulira, kapena zowawa,³²⁹ ndipo chilungamo chidzakhazikika,^{330 331} Kudzera m'mau ake ife tilinako kuunika kwabwino kotionetsa kumwamba. Ife sitidzaona dongosolo lake koma kufikira titamuphatika iye, koma pamene tichita izi kudzakhala kuona zinthu zodabwitsa zedi.^{332 333 334} Uku ndiko kunena kuti pamene tidzamvetsetsa kwathunthu chomwe iye wakhala ali m'zaka zonsezi.

Apa ndipomwe tidzaona momwe miyoyo yathu, kuphatikizapo mayeso pamodzi ndi zovuta zonse zomwe takhala tikukumana tikudutsamo,^{335 336 337 338} zonsezi zatiumba ife kukhala chiringanizo chokoma kwambiri kumbali ya kutsogolo lokoma. Mulungu adzatilola ife kuti tiphatizizi nawo m'chikonzero chake chokoma kumbali ya kutsogolo kupsyolera m'chikhulupiliro chathu mwa yesu. Yesu ndiye ulusi wa dongosolo lokoma la mulungu komanso thonje la pulani yaikulu ya mulungu.

Koma, ndi kufikira pomwe adzaona chilinganizo chokoma cha mulungu kumbali ya kutsogolo tidzasowekera kudalira mwa yesu ndikukhala ndi chikhulupiliro mwa iye kuti chikonzero chake, kupsyolera mwa yesu, chinapangidwa kuti chitipulumutse ndikutitenga ife kukhala ana ake m'banja lake momwe iye adzagawana naye chiyeero chake.

Pokhapokha titafika kumeneko, ndinthudi tiyenera kuvomereza mfundo yoti kumbali yathu yomvetsa chisoni ija ya bmbali ya kumbuyo ija kudzakhala, imfa, nthenda, kudwala, kusowa chilungamo, kusweka mtima, komanso zina zambiri. Tiyeleranso kuvomerza kuti tidzakhala mu nkondo pamen tikhalebe mbali ya kumbuyo ndi woipayo yemwe amafunafuna kutitchinga ife kuti tisaone kusogolo. Satana amafunafuna kutitchinga ife kuti tisalebe m'mbuyo komwe iyeyo adzakhala woweruzidwa mpak muyaya. Satana samakonda kuti inu muphunzire zokhuza ulusi, ulusi womwe udzafikitsa kutsogolo.

Choncho, pamene tikhala kumbali ya kumbuyo, sidzizakhala nthawi zonse zokoma, kapena zabwino, kapena zosangalasa. Nthawi zonse sitiitha kumvetsetsa chifukwa chomwe mulungu amalolera mayesero ndi zoopsa m'moyo wathu,³³⁹ koma tiyenera kukhala ndi chikhulupiliro kuti zovuta zonse zomwe tikudutsamo zidzalukidwa ndikukumikizidwa pamodzi kukhala chikonzero chapamwamba kwambiri. Tiyenera kukhala ndi chikhulupiliro kuti tidzakhale pamodzi ndi iye m'paradaizo mosasamala kuti kodi tadutsa muzotani-chomwe chiri chimene yesu anaudza mwa achifwamba aja omwe anapachikidaw pamtanda aja woyandikana ndi iye patangotsala mphindi pang'ono kuti amwalire.

ndikupyolera m'kusweka kwathu kwa mtima m'mene timatsrndezeredwa chifupi ndi mulungu. Ndi kuzera m'kusweka mtima momwe timaphunzira kuti sitingathe kukwanilitsa kupeza moyo popanda mpulumutsi. Ndi kupyolera mukusweka mtima kwathu momwe timaphunzira kuti m'dziko muli choipa-mphamvu yomwe palibe angathe kuihana. Ndikupyolera mwa yesu yekha tingathe kugonjetsa mphamvu ya satana m'moyo wathu. Nthawi zonse tiyenera kukumbukira kuti m'zilizonse zomwe zichitika m'moyo wathu, mulungu amakhala ndi chifukwa potitengera ife kufika ku malo amenewo³⁴⁰ - nthawi zina malo amaeje, nthawi inanso m'malo a see. Zokumana zonse zili ndi kukula kwathu kwa uzimu. Tsopano tikumvetsetsa kuti m'zinthu zonse mulungu anachita kuti zikhale

ubwino kwa iwo amene ankonda iye omwe aitanidwa monga mwa cholinga chake³⁴¹

Kukhulupilira m'chikonzero cha mulungu kumafunikira chikhalidwe

Zambiri za zonse takambiranizi zimafunikira kuti inu mukhulupilire kuti mulungu ali ndi chikonzero. Kodi inu mumakhulupilira kuti mulungu alindi chikonzero, kapena m'makhulupilira kuti zonse za izi ndi nkhani yaikulku yeniyeni kodi inu mukuika chikhulupiliro chanu m'zotani? Kodi mukuika chikhulupiliro chanu mwa mulungu pamodzi ndi mawu ake, kapena mukuika chikhulupiliro chanu m'zinthu zomwe mukuona ndi kumva m'dziko, kapena mwinamwake mukuika chikhulupiliro chanu mwa inuyo? Mwina mwake inuyo-ndiye chonse chomwe inu mumasowa basi. Mwina mwake zinthu zikukuyenderani bwino kotero kuti simungathe china chirichonse, kapena wina aliyense, chifukwa choti muli ndi china chilichonse pansi pa ulamuliro wanu, ndipo china chilichonse chili m'zanja lanu.

Mwinanso mungathe kumakhukupilira kuti kulibe mulungu-choncho ngati inu mungasowenso chikhulupiliro chotani? Izi zimaoneka kukhala zopambana kwambiri kufikira wina wake wapafupi nanu amwalira, kapena kufikira mwagwa pa makwero ndi kulamula chiwalo chanu chimodzi, kapena wina wake wabwera pa sukulu yanu ndi kuombera m/modzi wa ana anu. Pamene zinthu zimenezi zichitika tonse timaumilizika kuitana kwa mulungu.³⁴² Chimenechi ndich chikhalidwe cha moyo wathu. Kudziwa kuti kuli mulungu ndi chithu chokhazikika m'chilengedwe chathu.³⁴³

Aponso pali funso lina lofunikira kwambiri kaw inu; kodi muchita chani pa zokuzana nkhani yomweyi? Kodi mumukana mulungu kapena kukana kuti iye alipodi? Kapena, kodi mudzatenga ka mphindi chabe ndikuyenera kupeza zochuluka za iye? mungathe mumukana mulungu kapena kumaunyoza iye, zonsezo zili ndi inuyo-koma iye sazakukuanani kapena kukunyoza ai. Mulungu adzapitilira kuima kunja kwa mtima wanu ndipo adzadikirabe kuti inu mumuitanire mkati mwanu.³⁴⁴ iye ali pamenepo tsopano lino. Kodi mungathe kumumva? Ali ndi zambiri kuti agawane nanu, koma mukuyenera kumuitana iye. iye angathe kulowa ngati inu mutamuitana kuti alowe. Mungopempha basi. Muzakhoza kutha amuyaya wanu wonse ngati mutalola kuti ku myada kwanu kumuike iye kunja. Muyaya ndi nthawi yaitali kotheratu.

Chilengedwe cha ulemelero cha mulungu cha kumwamba ndi dziko lapansi ndizachidziwikire kwa wina aliyense- choncho ndife osowa chowilingula podziwa kuti alipodi.³⁴⁵ pakuti zaku mwamba zilengeza ulemelero wa mulungu.³⁴⁶

Taonani: ngati inu mumakonda masamu, wasayansi wina pamodzi ndi woziwa masamu analingalira kuti kuthekera koti dziko linakhala komanso ndi lokhala ndi kuthekera kosunga moyo monga umo mmene

tidziwira kuti zimatero-pafupifupi ndi a mulingo okwanira $\frac{1}{10}$.³²²

Zimenezi zikanakhala .000 (kuphatikizapo zina 319 “00”) ndipo kenako 1. Muyang’ane kakhani komwe mutu wake ndi “Evidence for God from probability” (umboni wa mulungu ku zopenekera) pa www.pleaseconviceme.com kanambala kochepetsa kapeneka ndi ka dziko lapansi basi. Nanga kuli bwanji munthu? Ngati mutayang; ana chilengedwe chodabwitsa chopezeka mkati mwa wina aliyense wa ife mwinanso mungathe kunena kuti kupenekera konena kuti anthu amangopezeka okha kopanda m’lengi nkochepe zedi. Kenako mudzawaonanso kuti muchulukitse(kutaimutsa) manambala ang’ono ang’ono awiri amenewa am’dziko ndi anthu kuti mupeze kupenekeleka kwao kopezeka popanda m’lengi. Izi zikanakhala chimodzimodzi kupenekeredwa kofanana ndi mphamvu ya mlengalenga yokola zithu zoponyedwa m’mwamba kubwelera pansi. Ndipo sitingathe ngakhale kukamba za gulugufe, cholengedwa chimene chimayenera kufa kaye kuti chibadwe. Mukuganiza kuti kupenekeredwa kwa gulugufe n’kotani kuti angathe kufa, kukhala moyo, ndikufanso (moyo-imfa-moyo)? Kuti akhale monga timuona lero lino-popanda m’lengi? O, iyitu sopano ikubwera kukhala nambala yaing’ono zedi. Ndipo pali zikwi zikwi za zolengedwa zina m’gulu la nyama(zilombo) touluka ndi tokwawa tomwenso chili ndi chilengedwe chodabwitsa kwambiri, tokhala tambiri ta ito tongosowekerkuthekerak kokhala tsiku limodzi kuti tikhale ndi moyo;

Mudzaziona mukadzazikhulupilira izo

Chifukwa choti ndife anthu, timadzolowera kuika chidaliro chathu komanso, chikhulupiliro chathu m’zinthu zimene tingathe kuziona, osati m’zinthui zimene zomwe sitingathe kuziona. Tonsefe mwina mwake tanenapo mu nthawi ina kapena inzake kuti, “ndidzakhulupilira ndikazaona”

Chabwino, tsoka lake umu sim’mene mulungu amagwilira ntchito ai. Kunena zoonza, ndizosemphana kwambiri. Ndi mulungu timanena kuti, “udzaziona ngati udzakhulupilira.”³⁴⁷ Ndi mulungu, zonse zimatsamira pachikhulupiliro ndi chidaliro basi. Tikakhala ndi bwenzi lapamtima yemwe timam’dziwa bwino ndiye kuti amakhala amene walanda mtima wathu. Ichi chimatipatsa ife chikhulupiliro kunena kuti iye adzachita china chilichonse chomwe wanena kuti adzachichita. Izi sizosiyana ndi momwe mulungu amachitira. Kukhulupilira mulungu tidzasowekera kumdziwa bwino kwenikweni tidzasowekera kuwerenga komanso kumvetsetsa kwa buku lake la malangizo, baibulo. Baibulo limanena kuti iye amasamalira iwo amene amam’khulupilira iye.^{348 349 350}

Chabwino, muli ndi mwai waukulu! Mulungu akadakonda kukhala ndi nthawi yaikulu ndi inu. Mulungu akufotokoza pa yeremiya 29 ¹³“ndipo mudzandifuna ine,

ndikundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wonse” ¹⁴ndipo ndidzapezedwa ndi inu, ati yehova”.

Popandachikhulupiliro zidzakhala zosatheka

Pamene muzaika chikhulupiliro chanu pa mulungu kulemedwa kuchokera ku dziko lapansi kudzachotsedwanso pamapewa anu.³⁵¹ Kukhala ndi chikhulupiliro mwa mulungu kumafunikira chidaliro, Ndipo kukhala ndi chikhulupiliro ndi chinthu chofunikira koposa chifukwa wopanda chikhulupiliro.

Mulungu adzapeleka mphoto kwa amene akumafuna mowona mtima. Tikuyenera kuwerenga mawu ake ndi chikhulupiliro mwa iye tikumumva akutilankhula. Mukapatula nthawi yanu kuwerenga mawu ake zizathandiza kulimbikitsa chikhulupiliro chamwa iye ndipo mukakhulupilira mwa iye ndipamene adzayamba kuyankha mapemphero anu pa nthawi imeneyo adzakuthandizani kupanga ziganizo kolingana ndi zimene akukutsogolerani kuti muchite. Tikamaganiza za muyeso uwu wakudalira pa iye tidzalankhula tokha, sitingathe kukwanitsa kupanga izo ndizovuta kwambiri. Ndingadalire bwanji chinthu chomwe sindichiona?

Ichi chimawachitira athu ambiri komanso ndichotchinga kumvetsetsa kuti mulungu ndindani. Koma mukanadaziwa kuli mulungu ali ndi yankho lomaliza pa inu.

Mukamulandila yesu mumtima mwanu mzimu wa mulungu (uzimu oyera) amapedza malo mumtima mwanu ndipo chifukwa choti mzimu woyera amakudziwani bwino koposa m'mene umaziziwira wekha adzakupatsani zosowa zanu zonse kuphatikizapo kumvetsetsa, kupilira ndi chifundo. Mzimu woyera kudalira mwa mulungu mzimu woyera adzakuthandizani kukugwirani pamene mwazingwa komanso mzimu woyera adzakuthandizani kukupambanitsani. Pamene nthawi zina mungalephere mutha kumanena mwa inu nokha. “izi zikufunikira chikhulupiliro chachikulu kapena zidzatengera chozizwa kuchitika kuti zitheke.

Uthenga wabwino ndi woti: chozizwa ndichopezekeratu pa moyo wanu. Mukungosoweka kum'landira yesu mumtima mwanu. Tsegulani khomo la mtima mwanu ndikum'lola kuti alowe ndipokhapo mungam'lole kulowa mumtima mwanu ndipamene angaziulule kwa inu.

CHIKHULUPILIRO CHOONA

Ambiri a ife ali okonzeka kuika chidaliro chathu pafupifupi koma chilichonse osati pa mulungu. Tidzadalira pa okondedwa anzathu, abwana, adotolo kapena m'bale koma mulungu? Ndizovuta kwambiri ndingadalire bwanji chinthu chomwe sindichiona?

Miyambo 3 vesi⁵ imati khulupilira yehova ndi mtima wako wonse osachilikiza pa luntha lako, vesi⁶ umulemekeze m'njira zako zonse ndipo iye adzawongola mayendedwe ako.

Tikazichilikiza pa nzeru zathu ndipamene timadziłowetsa tokha m'mavuto.

Munayamba mwagwidwapo mnyengo yomazona nokha kuti mwakodwa m'mavuto ena ake m'moyo wanu? Mwina mukumva ngati mukukhala munyengo zovuta zomwezo nthawi ndi nthawi.

Kulandila chimene mulungu akufuna kuti ukhale nacho zimadalira kuti ulumikizane naye. Ngati ungazipereke kwa iye ndikhala ndi chikhulupiliro mwa iye walonjeza kuongola njira zanu 8. njira zake zoongoka zidzakuthandizani kutuluka m'mavuto amgonagona pamoyo wanu.

Komabe kusintha sikukhala kophweka.

Kukhala ndi chikhuluoiliro choona zimatengera munthu kusiya pafupifupi china chilichonse chimene unaonapo, kukhuzapo, unamvapo ngakhale zimene unakhulupilirapo komanso ponena za zimene umaganiza za kuti ndizoonza ndipo zomwe umaganiza za zithu kukubweresera chisangalalo mwakonzeka kusintha. Zochuluka zomwe mwaganizxapo m'mbuyomu ndiza bodza. Kodi satana wakusogolerani ku njira zoyambilira? Kapena ayi. Ndiye sinka zipangitsa moyo wako kukhala kophweka.

CHINSISI

Chinsisi ndikutembenukira kwa mulungu m'china chilichonse umachita ndi lingaliro la likulu limene ungapange⁹. usadalire mumzeru zako¹⁰ kukhala chete ndikumvetsera liwu lake¹¹ osaopa¹² osakhala ndi nkawa¹³ kuwaona ena okuposa¹⁴ kusunga malamulo ake¹⁵ kudalira pa iye akakhala m'mavuto¹⁶ kumkonda iye ndi mtima, moyo, mphamvu ndi maganizo¹⁷ kuti mzimu woyera akuphunzitse zinthu zonse¹⁸ ndikukupatsa zokhumba mtima wako¹⁹ ndati ungachite zonsezi mulungu adzakudzadza ndi mtendere pamene udalira mwa iye kuti udzadze ndi chiyembekezo ndi mphamvu ya m'zimu woyera²⁰ adzakupatsa zonse mochuluka²¹ mwakonzekera kusintha kotere? Ngati yankho lako lili inde,

Umu ndim'mene ungapangire.

MUTU 5

Ndinapangidwira kusankha

Tisanafe tikuyenera kusankha

Timayenera imfa

Chipangano chakale ndipamene mulungu anatipatsa malamulo khumi. Chipangano chakale ndikumene mulungu ananena kuti akhala pakati pathu³⁷³ ³⁷⁴ chifukwa machismo athu asowekera mpulumutsi.³⁷⁵ dongosolo lake lalankhulidwa m'chipangano chakale. Chimene chinalembedwa zaka mazana zapitazo mulungu asanabwere padziko lapansi pano m'kukhala pakati pathu angakhale yesu sakanabwera padziko kuti atiferenso zaka zikwi zina, mulungu anadziwa kuti amasoweka nthawi yochuluka kuphunzira kuti tinasoweka mpulumutsi. Koma mpulumutsi. Koma mpulumutsiyo anadziwika kae.³⁷⁶

Palibe njira ina kapena m'dziko linma lili lonse limene munthu angathe kupulumutsidwa nalo^{377 378 379} wina aliyense angakhulupilire m'dzina la yesu ndikulengeza adzamasulidwa ku tchimo.³⁸⁰

Izi zikuphatikiza kale lanu lero ndi machismo anu onse amtsogolo. Tinapulumutsidwa mwa chisomo cha mulungu³⁸¹ palibe chomwe ungachite kuti ukhale m'chiphatso chopitira kumwamba. Palibe njira inanso imene ingapezere chipulumutso³⁸² kapenanso kuchigula ukuyenera kulengeza chikhulupiliro chako mophweka.³⁸³

Mulungu waika m'phatsoyi mopezekeratu kwa wina aliyense. Koma kuti upulumutsidwe ukuyenera kukhulupilira dondosola la mulungu. Dongosolo lomwe analankhula kale m'chipangano cha kale ndipo linakwanilitsidwa m'chipangano chatsopano mulungu amakupasani chilungamo ndikukupatsani

kumwamba kwa m'yaya naye limodzi kudzera mwa chikhulupiliro chanu mwa yesu³⁸⁵ basi. Kudzera mwa yesu mabala anu atha kuchilitsidwa.³⁸⁶

Nthawi itasala pang'ono yesu asanafe mulungu atate anachotsa maso ake pa yesu ndipo machismo a m'dziko anaunjikidwa pa yesu³⁸⁷ munthawi imeneyi mulungu anachotas chiyero chake pa mwana wake. Iyi inali nthawi imene izi sizikanachitika. Ichi ndi chifukwa atate mulungu sangakhale mbali ya tchimo, tchimo lililonse mu ululu yesu analira "mulungu wanga mwandisiyanji?"³⁸⁸ Kusiya kumeneku kwa mulungu atate ndi kulira kwa yesu pamene amazilira ndi imfa ya ululu zinali choncho kuti yesu asenze machismo adziko lapansi.³⁸⁹

NDONDOMEKO YAKE YOPULUMUTSA YATHA

Iwo amene angakhulupilire mu dongosolo lake loyera adzapulumutsidwa. Iwo amene sakhulupilira inde tsogolo lawo lidzakhala la ulemelero. Imfa ya yesu pamtanda kunali kugonjetsedwa kwa satana ndi tchimo. Dongosolo la mulungu lopulumutsa latha tsopano³⁹⁰ wina aliyense angayike chikhulupiliro chake mwa yesusadzapita ku gahena ndi satana.³⁹¹ Tsiku lachitatu yesu atapachikidwa anauka kwa akufa nazione sera yekha kwa ophunzira ake ndi mazana a wanthu ena.³⁹² Pali mabuku ambiri amene akulongosola kuchokera nthawi anthu anamuona yesu atauka kwa akufa keneko yesu anachezera anthu osiyanasiyana kwa matsiku³⁹⁴ asanakwere kupita kumwamba kumene ali lero kudzanja la manja la mulungu.³⁹⁵

SIMUNACHEDWE

Yesu atapachikidwa palinsi zifwamba zina ziwiri zimenenso zinapachikidwa nawo limodzi china kumanja china kumanzere.³⁹⁶ Wachifwamba winayo anayamba kulankhulira mwano yesu, nati, SIWE MESSIAH? Zipulumutse wekha ndife pamodzi koma wachifwamba winayo anadzudzula nzakeyo nati, suwopa mulungu? Pamenepo mkuti muli pachilango limodzi tikulangidwa moona pakuti yikulandira zotiyenera molingana ndi mmene timachitira koma munthu uyu sanachimwe mkonse keneko wachifwambayu anati, yesu, mundikumbukire pamene mulowa mu ufumu wanu ndipo yesu anayankha indetu, indetu ndinena ndiwe lero lomwe ukhala ndine mu paradizo.³⁹⁷

Yesu m'busa wathu wabwino anabwera kudziko kudzapulumutsa wotayika. Mphindi zocheza asanafe pamtanda anapulumutsa nkhesa yake ina yotauka wachifwamba amene anapachikidwa naye limodzi. Wachifwambayi anamva ndikuzindikira liwu la m'busa wake nakhulupilira.

ZILIBE KANTHU KUTI MWAKHALA NDI MOYO WOTANI

Ichi chikutanthauza chani kwa iwe? Chikuyenera kutanthauza kanthu kapadera. Chikutanthauza kuti zilibe kanthu kuti wakhala m'moyo wamtundu wanjani angakhale munapalamulapo milandu yowopsa mulu ndi mwayi wotembenuzira moyo wanu kwa yesu ndikupulumutsidwa musanafe. Imeneyi ndi mpatso yochokera kwa mulungu kukupatsani chikhulupiliro mwa iye. imfa ya yesu pamtanda inakhala chida chogonjesera satana, satana amaganiza kuti

ndikugonja kwa mulungu ndi ufumu wake. Koma kunali kutha kwa satana. tsopano ndi satana amene akutsutsidwa.^{398 399 400}

Ungakonde kulandila mphatso imeneyi tsopano? Mupemphere pemphero ili momveketsa mawu⁴⁰¹ ndipo pamene muli moyo mulibereza osadikira kumbukirani kuti satana akuyembekeza kuti muchedwetsa kupanga chiganizo chomlandila ndipo chiganizo chanu chizakhala chathunthu. Mwachidule pempherani.

Pemphero ili ndilomveka ndikukhulupilira kuti yesu anabwera pa dziko kuti afere machismo anu okonedwa mulungu sindikumvetsa chilichonse-koma ndikudziwa kuti ndine ochimwa ndinayenera imfa ndikusiyantsika nanu kwathunthu. Zikomo potumiza yesu kuzafa m'malo mwanga ndikhulupilira mwa yesu yekha kuti andikhululukire machismo anga ndipondkum'landila ndi mphatso ya moyo wosatha ndikupempha kuti yesu akhale mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanga. Amen.

Ngati mwavomereza pempheroli ndikukhulupilira mwa yesu mwapulumutsidwa. mwapulumutsidwa kuti mukhale mwamuyaya ndi mulungu ku mwamba m'matsiku otsalawa pokhala padziko palibenso chimene mungachite koma pali zambiri zomwe mungachite. Mwadalitsika tsopano ndipo mzimu woyera walowa mu mtima mwanu ndikukhulupilira kuti m'dalitsowu mupititsa kwa enabe. Auzeni za bukuli kuti maso awo atseguke.

Yesesani kuti muwerenge mutu 6 kuti muphunzire kagwidwe ka ntchitoyi musadandaule. Sintchito yovuta mudzaikonda komanso muzaifuna.

Ngati mwamulandila yesu monga mpukunutsi wanu mulindi mawyi wooti kuwala kwanu kuwonekera kwa wanthu kutinso akaone ntchito yabwino ndikulemekeza atate wanu wakumwamba.⁴⁰²

KUSAPANGA CHIGANIZO-NDI CHIGANIZO (kusasankha-ndikusankha)

Musaiwale kusasankha ndi kusankha komwe. Taganizani mwaka nthawi. Sizingatheke ngati mungathedwe kupanga ciganizo ichi ndichimene satana akuyembekezera kuti muchita. Satana akuyembekezera kuti simulandila mphatso ya yesu ya uleleyi chimene zikutanthauza kuti satana ali ndi mpata. Satana akudziwa kuti mukamulandira yesu mwai wokupititsani kugahena watha. Satana waweruzidwa kale mupulumutsidwa. Mukuyenera kutsegula khomo la mtima wanu ndipo yesu alowemo. Tsopano akufuna agawane nanu ndondomeko ya ulemelero wake.

Ku machitidwe a atumwi 22 amati vesi 16 *ndipo tsopano uchedweranji? Tauka mubatizidwe ndi kusamba kuchotsa machismo ako nuitane pa dzina lake.*

NDINGAKHALE NDI MOYO BWANJI NDITATHA KUDALIRA MULUNGU

AKUFUNIKA KU M'LEMEKEZA

Ngati mwalandila yesu mumtima mwanu ukuyenera kukhala amoyo wosangalasa mulungu ichi sichifukwa ukuyenera kuteru koma chifukwa muzafuna kuteru

Mulungu anakudziwani chifukwa munabadwa⁴⁰³ ndipo anakuonanin kuti munali muchitsokonezo chifukwa cha tchimo la Adamu. Ndipo anabwera kudziko nakhala mu umoyo wosachimwa nakufera, anakufera kuti usakhale ku gahena kwa muayaya komwe ndikumene kumaliyenera kukuphwanya lamulo la mulungu ngakhale limodzi.

Mulungu sakanachita zomwe anachita koma anafuna kuetro chifukwa anakukonda kwakukulu. Ngakhale ukanakhala yekhayo amene akanafera akanabwerabe kuti akupulumutse kuchiwonongeko, monga m'busa wabwino chifukwa cha chimene yesu amakuchitirachi ukuyenera kufunafuna kumulemekeza ndi chisankho chako anakulemekezani ndi imfa yake chithu chochepa chimene ungachule ndicho kum'lemekeza ndi zisankho zako. Ichi ndichophweka kusiyana ndi kufa simukuona choncho?

Baibulo limatipatsa malngizo a mmene tingamakhalire ndi moyo ndinso kuti tikhale nchere ndi kuunika m'dziko kumulemekeza⁴⁰⁴ muzonse zomwe tingachite. Malemba amtipatsa chisogozo cha zitsankho zomwe tingapange kukhala monga ana aamuna ndi ana aakazi amulungun.⁴⁰⁵ Chitsogozo chake kuphatikizapo kukhala mmene iye afunira ndi kukhala kolingana ndi lamulo lake lalikulu lomwe ndi,⁴⁰⁶ uzikonda ambuye mulungu wako ndi mtima wako wonse ndi moyo wako wonse ndi malingaliro ako onse⁴⁰⁷ ili ndi lamulo loyamba ndi lalikulu lachiwiri lake nali, uzikonda mnzako mmene uzikondera iwe mwini apa pali njira zomwe zingakuthandize kuti zisankho zako zizilingana ndi chifuniro cha mulungu:

1. kupititsa patsogolo
2. kuwerenga baibulo
3. kupitiliza kumupempha mulungu
4. khala chete kenako mvetsera
5. funa uphungu wa mulungu
6. kuzindikira nthawi yoti uchite
7. phunzira kuzolakwika zako

Tiyeni tione chimodzimodzi mwa zinthuzi

KUPITITSA PATSOGOLO

Ngati mukukhulupilira mwa yesu kodi ndi zinthu ziti zomwe ungazipititse patsogolo.⁴⁰⁷ Kolingana ndi yesu lamulo lalikulu ndikumkonda mulungu ndikumkonda pakutastira lamulo limeneli kukhala kuyamba kwabwino pamene

mwayamba kutsema njirazi udzafuna kupanga ziganizo zomwe zingamlemekeze mulungu kenakonso ziganizo zomwe zingamlemekeze ndikukonda banja lanu ndi amzanu monga inu mwini. Zoonza ndizakuti mulungu watilamulira kukonda amzathu monga tizikondera tokha.

Mulungu amakukondani. Ichi chikutanthauza kuti azafuna kukuthandizani m'china chilichonse mungachite⁴⁰⁸ akupatsani zisankho ndiponso akupatsani mphoto pachisankho choyera chimene mwapanga mnyengo zambiri sipazkhala zisankho zoipa kapena zabwino.^{409 410} Za munthu zokha zonse zili m'dongosolo la mulungu Ndi chifuniro chake pamoyo wanu ndipo zonsezi zidzatsogolera kukwaniritsa cholinga cha mulungu pa moyo wanu⁴¹¹ makamaka mukamasatila.

KUWERENGA BAIBULO

*Mawu ndi kuunika kwa ku mapazi anga kuwala pa njira yanga.*⁴¹²

Pakupanga chiganizo chilichonse pali funso lofunikira oyenera kuzifunsa nokha, KODI MULUNGU AKUTI CHANI ZA ICHI ukamakumana ndi ziganizo zofunikira nthawi werengani baibulo ndikuona chimene mulungu akunena za chiganizochi zitha kuthandizanso kufunsa anthu ena amene atha kukhala ndi ndikumvitsa bwino pachimene baibulo likunena kuposera iwe ukuyenera kuchita kafukufuku m'baibulo chifukwa ndimene chitsogozo ch mulungu.⁴¹³ Lembala lililonse adaliuzira mulungu ndipo lipindulitsa pachiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo ch chilungamo kotero kuti khazikitsani mapazi anga m'mawu anu.⁴¹⁴

PITILIZANI KUMUPEMPHA MULUNGU

Ngati ukufuna kudziwa chimene mulungu akufuna-mupemphe ali nawe mwanjira ina pemphera!⁴¹⁵ Kenako umuyembekeze kuti akuyankhe pemphero lako koma usayembekezere yankho pompo nthawi zina amayankha kudzera mwa munthu wina kapena kuzera munyengo yosayelekezedwa pamene angayankhe pemphero lako. Atha kukulankhula kudzera kwa mizako kapena kuzera mwa munthu amene sumadziwa. Mulungu ndiwa bwino pazimenezo. Mulungunso ali nmdid zosangalatasa kuti utha kulandira yankho lako kudzera munjira zowawa.

Utha kukhala pamalo oti sunakhalepo ngati malo ogulitsira petulo kapena dizilo (filling station) zomwe sunalingalirepo chiyambire unangokhala ndi teyala lakuphwa) kuzungulidwa ndi anthu ndi anthu osadziwa. Achinyamata ochuluka ataima kuti agule ma sweet. Lakho lake laperekedwa ukamva yankho la mulungu yesesa kumulemekeza pa kuyankha ndi chikondi chake pa iwe kenaka seka mutu wako m'mene anayankhira pemphero lako. Amangokondfa kuchita izi kwa anthu amene amamukonda.

Komanso uwonetsetse kuti kupempha mulungu nzeru⁴¹⁶ pakuti nzeru izalowamumtima mwako ndipo moyo wako uzakondwa ndi kudziwa nzeru ya mulungu imayamba ndi kuopa yehova.⁴¹⁷ Kuopa yehova ndiko chiyambi cha kudziwa usakhale opusa, opusa anyoza nzeru ndi mwambo.⁴¹⁸ mulungu afuna akutsogolere ndikukuthandiza kupanga ziganizo zofunikira m'moyo wako, ndipo walonjeza kukuphunzitsa kuzera m'mawu ake.⁴¹⁹ pakuti ndidziwa malingaliro amene ndilingalira inu ati yehova malingaliro a mtendere si achoipa akukupasani inu mdzukululu ndi chiyembekezo⁴²⁰ mulolere akusogolere kuzera m'mawu ake.

KHALA CHETE NDI KUMVETSERERA

Ambiri aife timapemphera koma sitimvetsera, timaliwona pemphero ngati kulumikizana kwa mbali imodzi koma mulungu sangatilankhule ngiti tikupitilira kulankhula kotero kuti timaimika pempherolo ndikumvetsera. Kumvetsera ndikofunikira kwambiri polumikizana. Kuphunzira kudziwa liwu la mulungu ndi imodzi mwa zofunikira kwa wokhulupilira.

Tizapitilizabe kuvutisa ndi malingaliro amene timawapanga ngati amene timazipanga ngati sitiziwa liwu la mulungu. Kumbukirani ana ankhosa amene amanva liwu la m'busa wawo ndipi zimasala liwu la m'busa wawoyo? Ana ankhosa omwe samva liwu la m'busa wawo saziwa kusatira liwu la m'busa wachilendo. Tikuyenera kudziwa liwu la m'busa wathu kuti tisasochere pakuti mulungu amadziwa kuti iwo amene amudziwa amadziwa liwu lake.⁴²¹

FUNA UPHUNGU WA MMAWU A MULUNGU

Zolingalira ziziwika mopanda upo, koma pochuluka aphungu azikhazika.⁴²²

Pa ziganizo zenizeni m'moyo wanu ndich nzeru kupeza uphungu kwa atsogoleri a mulungu, kholo, abusa kapena bwenzi limene limadziwa bwino malemba litha kukhala thandizo lopambana. Atha kukuthandiza kuchotsa chikaiko china chilichonse chimene ulinacho chithu chotsiriza mchakuti usamangolora uphungu ochokera kwa munthu wina aliyense usanamudziwe bwinobwino.⁴²³

Uphungu wa mphamvu ndi umene unglandire kuchokear kwa yesu⁴²⁴ ndiye usaope kumpepha iye. pitiliza kucheza ndi anthu amene akhala m'chikhulupiliro kuposera iwe. Uphunzire pa nzeru ndi chidziwitso chawo, makamaka pamene ukupunthwa pezelanipo mwai pa uphungu wawo. Ndikuphunzira pazimene anapunthwa (zomwe analakwitsa) kuti kuphunzira kwako kukhale kopambana. Udziwenso kuti kulephera kwako kuzathandiza enanso azunzika uzawapasa chitonthozo chimene mulungu anakupatsa.⁴²⁵

KUZINDIKIRA NTHAWI YOTI UCHITE

Kodi chitsakho cha nzeru kwambiri ndi chiti? Limeneli ndi funso gwiritisa ntchito malingaliro odzadza ndi mzimu kuganiza chithu ndikupanga ziganizo pa chithu ch nzeru kwambiri. Chifukwa mzimu woyera akukhala pakati pako ngati wamulandila mumtima mwako, uli nnzeru zomwe zimakhala muzimu mwake imene ingathandize kukutsogolera ndikukulondolera kotero kutipempha chitsogozo. Timadziwa bwanji kuti tikupanga zinthu mu nthawi yolondola, mnthawi ya mulungu, mulungu amadziwa nthawi ikakhala yolondola.⁴²⁶ Tikuyenera kupemphera kenako timvetsera, tikuyenera kukhala wofufuza m/mene mulungu angatisogolere. Kuchit zinthu munjira ya mulungu zizatithandiza kusunga nthawi, mphamvu ndi ndalama. Osatchula zakupewa zambiri.

YESANI CHIKHULUPILIRO CHANU

Mukuyenera kukumbukira kuti kupanga chiganizo ntchito yotenga nthawi yaitali mukuyenera kupereka chifuuro chanu pafupipafupi kwa mulungu munthawi yonse imene mukupanga chiganizo kenako mukhale ndi chikhulupiliro ndi kulimba mtima kuti avumbulutse chifuniro chake kwa inu. Perekani kwa mulungu chinachilichonse chimene mukuchichita ndipo adzakhazikitsa dongosolo lanu.⁴²⁷ sizingatheke kuti akuiwalireni zolinga zake ngati akudziwa kuti simumvera. Ndizofunika kwambiri kuti zolinga zanu mwazipereka ku chifuniro chake. Zolinga zako ukazipereka kwa mulungu mutha kukhala ndi chilimbikitso kuti iye adzawalitsa zolinga zathu.⁴²⁸

Musaiwale kuti kopanda chikhulupiliro mkosatheka kumkondwewesa mulungu⁴²⁹ chimene akupempha ndichoti mukhale ndi chikhulupiliro monga kambeu ka mpiru ndipo ngati suchita kanthu zizakhala zosatheka kwa inu.⁴³⁰

PHUNZIRANI PAZIMENE MWALAKWITSA

Nthawi zonse muzalakwitsa ndipo muzalakwitsa zambiri. Koma kukhala womusatila yesu sizikuchotsa paudindo wokhala munthu wopanga ziganizo zabwino chifukwa cha zinthu zomwe umalephera kukhala munthu wopanga chiganizo simunthu chimene ukuyenera nthawi zonse kuchita nthawi zina mukungofunika kukhala chete kuti mulungu aike nzeru zake pa inunso.⁴³¹ Zitachitika kuti mwalakwitsa yesesani kuvomereza pamaso pa mulungu ndikupempha kuti akukukhululukireni. Musamulore m'daniyo kukutsutsani^{432 433} mumupempe mulungu kuti akupatseni nzeru. Mulungu akufuna kuikiza nzeru zake pa inu koma mukuyenera kumupempha.⁴³⁴ Ngati mukupanga chiganizo ndipo mwadalitsidwa kuti mulungu amene angalandire ulemelero. Komanso muyembekeze kuti enanso azayang'ana pa moyo ndikuphunzira m'mene mupangila ziganizo za mzeru zimene zinapatsa mulungu ulemelero. Pang'ono ndi pang'ono muzakhala mu mzeru zochokera m'mau a mulungu.⁴³⁵ Pamene mukumukhulupilira,⁴³⁶ mudzayambatso kuona zotsatira zounikira ziganizo zanu ngati mumukonda mulungu.⁴³⁷ Odala ndi amene aopa mulungu.⁴³⁸

MUKUTANTHAUZA KUTI MULUNGU ATITETEZA? NDIKUTITONTHOZA?

Kodi mulungu angakutetezeni mwantheladi Koma angakutetezenidi Chabwino zonsezi zingatengele chifunilo cha mulungu. Ndipo simungaziwe chomwe chili chabwino kwambiri kwa inu.

Mulungu sanalonjeze mwe zikuchitika mdziko lapansili. Chimene analonjeza ndi choti adzayenda nafe munthawi yomwe tikukumana ndi mavuto, ndipo watsimikiza kuti sazatisiya kapena kutisiya⁴³⁹ ndipo adzatipatsa mphamvu ndi mtendele wammtima tikamakumana ndi zovuto.

Chimene tikutanthauza ndi choti angakhale kuti Mulungu ali ndi kuthekela kotiteteza ku zoopya zathupi, ndikutimasula kumavuto chitha kusakhala chifunilo chake. Nthawi zina atha kugwilitsa ntchito mayeselo ndi zovuta kuti

atiyeletse. Mulungu nthawi zina amayesa chikhulupiliro chathu kuti tikhoze kupilira ndikukula kufikila kukhwima muuzimu.⁴⁴⁰ Kutakhala kuti mulungu watiteteza limenelo siphindu lathu. Mulungu atalola chivutiko pa miyoyo yathu nthawi zonse ndi mwai kwa ife kuti atipatse mphamvu yodalira mwa iye.⁴⁴¹

KUTIWOMBA

Chitetezo chake ndichoposa kanusu kachikhulupiliro kathu mwa iye. Akufuna mumuziwe iye ndiponso akufuna musandulizike kuti mudziwe chifunilo chake. Inde Mulungu akufuna mudziwe chifunilo chake.⁴⁴² Mutha kudziwa chifunilo chake nga mwasanudulizika ndipo kusandulizidwako kudzatengela mayeselo ndizovuta.

Nthawi zowawa kuvutika zitha kugwilitsidwa ntchito pofuna kumusiyanitsa munthu ndi njila zake zimene anazizolowela, ndipo mavuto amene angakumane nawo angawapangitse kuti akumane ndi Mulungu mwabwino ndi mnjila yatsopano kapena kunena kuti kuphwanya zikhalidwe zakale zachabe. Izi zitha kumakuchitikilani. Tikufunika kugwilitsa ntchito zowawa ndi zovuta kuwonetsa machitachita achikhulupiliro chathu. Tisaone mavuto ngati zophinja koma ngati chochitika chauzimu. Pamene mugwilitsa ntchito chikhulupiliro chanu mudzayamba kumanga minofu ya uzimu ndikukhala wamphamvu mmnofu wa uzimu wanu ndikukhala wokhwima muuzimu ndikuyamba kuthokoza mulungu pazimene akuchita pamoyo wanu. Mukachita izi mulungu adzakupatsani mtendele umene uposa kumvetsetsa konse.⁴⁴³ Mtendele umene amakupatsani ndiwaulele. Chamwayi kwa inu chifukwa mtendele umenewu sudalila pamavuto aliwonse ndipo utha kugwilitsidwa ntchito munyengo iliyonse.

MUSACHITE MANTHA

Tikuyenela kukumbukila kuti Mulungu amachita zambiri mumiyoyo yathu zoposa zimene tingazione. Chitetezo chake ndichachikulu kwambiri ndichosafikilika moposa kaganizidwe kathu kakangono. Mulungu sanalonje kutipasa kumwamba padziko pompano. Chimene mulungu watilonjeza kwa onse amene amukhulupilira ndikumulandila Yesu muchipulumutso chao.⁴⁴⁴

Yesu anatimveketse bwino kuti tipitilizebe kumpempha Mulungu zomwe tikufuna. Koma sizikutanthauza kuti nthawi zones azitipasa. Chifukaw zomwe timapempha sinthawi zones kuti ndizabwino.⁴⁴⁵ Mulungu azakuzungululani ndikukondela kwake ngati mthuzi. Ngati mungaitane pa dzina lake ndikuziwa dzina lake Mulungu adzayankha.⁴⁴⁶

AMBUYE ADDZADALITSA AMENE AKUMVELA MAMVELA MAWU AKE

NDICHIFUKWA CHİYANI MULUNGU AMADALITSA ANA AKE?

Pali chifukwa chimodzi chimene Mulungu amadalitsila anthu ake. Zimakha Choncho kuti ana akewo abweletse ulemelero ku dzina lake.⁴⁴⁷ Amadalitsanso ndi kupeleka mphatso kwa ena kuti nawonso akatumikile ndikudalits enanso. Koma kuti Mulungu atidalitse tikuyenela kukhala omvela mawu ake.

Mulungu walankhula mobwelezabweleza kuti adzatidalitsa mochuka.⁴⁴⁸ Kuti tikakule muntchito zones zabwino kuti mulungu akwanilitse lonjezo lake tikuyenela kukhulupilira kuti atha kutidalitsa. Malonjezano amulungu atha kuoneka ngati ndi osatheka kwa inu, koma kwa Mulungu amene analenga chilengedwe chonse ndi dziko palibe chomlephleka.⁴⁴⁹ Mulungu walonjeza kupeleka zokhumba za mtima wanu.⁴⁵⁰ Koma mukuyenela kumpempha. Simulandila chifukwa simupempha.⁴⁵¹

Mwazizizi kwa anhu ambiri nthawi yokhayo imene mulungu anamva kwa ife ndinthawi imene tili ndi chosowa. Pamatha kutha milungu, miyezi ngakhale zaka tisanayitane pa dzina lake. Komano chovuta china chikafika pamoyo wathu taonani timayitana kwandani? Kwa Mulungu. Izi zizakhala ngati kukhala ndi chigwenzi chomwe sunachionepo kwa zaka akukuitana ndikumapempha ndalama. Yankho lako lingakhale lotani? Ngati muli oona mtima mutha kunena kuti, mmmm ndakuziwa ali chikhalidwe chondifuna zikamvuta kapena akafuna ndalama. Ndichifukwa chiyani chikanakhala chosiyan ndi mulungu? Mukuganiza kuti mutha kungoitana paye mu miyezi ingapo kapena mu zaka zingapo. Komanso kumamufuna pokhapokha choipa chakugwelani pa moyo wanu ndiye kumuitana kuti akuphimbeni pavuto lanu. Zitha kukhala zosasamala kwenikweni sichoncho abale. Koma ndi zimene timachita. Ndipo ngati Mulungu sayankha mapemphero athu timapenga pafupifupi kunyoza mulungu, kenako timanena kuti mulungu sathandiza tikakhala ndi chosowa. Ganizani bwinobwino izi ndi zimene timachita. Koma iye kuti akudalitseni akuyenela kukudziwani ndipo ndikukudalilani. Amafuna adziwe muchita chimene angakupempheni pamene angakupempheni.

Kusazindikila kwathu kwa Mulungu ndi kusamvela mawu ake chizakhalabe chotchinga kuti tisalandle madalitso ake. Tikuyenela kuchita zomwe mawu ake akunena. Wina aliyense amene amayangana mawu amulungu ndikuiwala chimene mwuwuwo anena azinyenga yekha.⁴⁵² Koma iwo amene ayangana mawu ake ndikuchita chimene mawuwo anena adzadalitsidwa muzinthu zones zimene angazichite.⁴⁵³

KODI MULUNGU AMAYANKHA MAPEMPHERO

Palibe kukaika kulikonse Mulungu amamva mapemphero athu khaya muthuyo amakhulupilira mwa Yesu kapena ayi. Mulungu ndiwodziwa zones zomwe zikutanthauza kuti amamva ndikuona chinachilichonse chochitika padziko lapansi.⁴⁵⁴ Pali malo padziko pano pamene ungabisalekumene Mulungu sangamve pemphero lanu? Ayi palibe.⁴⁵⁵ Chinachilichonse chimene mungachiute kapena kuganiza chayalidwa pamaso pamulungu kumene tsiku lina mudzayankha mlandu.⁴⁵⁶ Ndiye pasapezeke munthu wokaika kuti mulungu amayankha mapemphero. Koma mulungu kodi amayankha mapemphero onse? Kodi mulungu amayankha mapemphero a omkhulupilira okha chimozimozi ndi amene samkhulupilira? Yesu sikuti amangomva kokha mapemphero kwa iwo omkhulupilira amayankha mapempherowo komaosati mmene timafunila nthawi zones kapena mmene tamupemphera. Amawauza okhulupilira kuti adzifika kuchimando chake molimba mtima kuti atithandize munthawi yachosowa.⁴⁵⁷

Ku buku la Luka 11 tauzidwa kuti ^{verse 9} “Ndipo ine ndinena ndinu Pemphani ndipo adzakupatsani funani ndipo mudzapeza gogodani ndipo adzakutsegulilani.”¹⁰ Pakuti yense wakupempha alandila ndi wofunayo apeza ndi iye wogogodayo adzamtsegulira. Yesu akupempha okhulupilira iye aike mitima yawo pa iyechufukwa iye ndipopulumukilapo pathu.⁴⁵⁸

MAPEMPHERO ATHU AKHOZA KUONONGEDWA

Koma izi sizitanthauza kuti yankho ku pemphero lanu lidzakhala inde. Nthawi zina yankho lidzakhala ayi ndipo nthawi zina yankho lidzakhala losiyana ndizimene tikuyembekezela izi zimachitika chifukwa Yesu amadziwa zabwino zapatsogola mosiyana ndimmene mumadziwila.

Chinthu chabwino pamapemphero athu ndichoti Mulungu amadziwa malingaliro athu sizisowekanso kuti tigwilitse ntchito mawu abwino. Ngati malingalilo anu siabwino ndi iye awonelatatu. Adziwa kuti kuti kuyankha pemphero kukhala bwino kwa aliyense kapena ayi amadziwa kukhutitsa pemphero kutha kukuza ufumu wake kapena ayi. Amadziwanso kuti kutiyankha pemphera autilola kuti titumikile ndikudalitisa enanso. Izi zikutanthauza kuti simapemphero onse amene ali olingana ndi chifunilo chake kotelo kuti ena atha kusayankhidwa.

TINASANKHIDWA DZIKO LISANALENGEDWE

Yesu anafa kuti atiwohole ku tchimo. Izi zikutanthauza kuti machismo athu anatengedwa ndi imfa yapamtanda ndipo ngati tikhulupilira mwa iye chitsutso cha tchimo lathu chidzachotsedwa. Komanso mmaso ayesu machismo athu sawonekanso ngati machimo. “Ngakhale machismo anu adzafiila ngati kapenzi adzayela ngati matalala.”⁴⁵⁹

Ichi chikutantauza kuti Mulungu sada anthu ake akachimwa amene akhulupilira mwa Yesu chifukwa ana ake ali mwa mwana wake Yesu. Pakuti mulungu anasankha okhulupilira mwa yesu kuchokela kudziko kuti oyela ndi opanda banga kwa iye.⁴⁶⁰

Palibe funso lakuti mulunguamamva ndikuyankha mapemphero aanthu amene akhulupilira mwa iye.^{461 462} Pakuti mapemphero aana ake ndi amphamvu komanso ochitachitana.⁴⁶³

SIZIMENE MUKUGANIZA

Mateyu 5 Imati,

¹Ndipo mmene anaona makamuwo, anakwela m'phiri; ndipo m'mene anakhala pansi anadza kwa iye ophunzira ²ache ndipo anatsegula pakamwa nawaphunzitsa iwo nati:

³Odala ali osauka mumzimu chifukwa uli wawwo ufumu wakumwamba.

⁴Odala ali achisoni chifukwa adzasangalatsidwa.

⁵Odala ali akufasa chifukwa adzalandila dziko lapansi.

⁶Odala ali akumva njala ndi lunzu la chilungamo chifukwa adzakhuta

⁷Odala ali akumva chifundo chifukwa adzakhuta.

⁸Odala ali oyera mtima chifukwa adzaona mukungu

⁹Odala ali akuchita mtendere chifukwa adzatchedwa ana amulungu

¹⁰Odala ali akuzunzidwa chifukwa cha chilungamo chifukwa uli wawo ufumu wakumwamba

¹¹Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu nadzazunza inunazakunenelani zonama zoipa zili zones chifukwa cha ine

¹²Sekelelerani sangalalani chifukwa mphoto yanu ndiyaikulu kumwamba pakuti potero anazunza aneneanakhalawo musanabadwe inu

Ngakhale ambiri timafuna kukhala ndi chipambano, kuchuka, chuma, nyumba yaikulu, galimoto yokongola, ndi zinthu zambiri zodula zonsezi si mtundu wa madalitso umene mulungu akufuna kuti tikhale nazo. Mulungu akufuna tikhale ndi iye. Akufuna tikhale ndi chikondi chake, chikhululuko chake, chifundo chake, utumiki wake kwa anthu ena, ndi zochuluka, chifukwa zinthu izi ndi zimene zizakhale zofunikila mu ufumu wake tsiku lina.

Tikawaona anthu akuoneka osangalala ndi chifukwa cha zinthu za mtengo wapatali sizikutanthauza kuti ndi osangalala ndipo adzakolola mphoto yake ya muyaya. Kunja atha kuoneka okondwa koma maonekedwe akunja ndi onyenga.

Ngatia uli mkupezeka kwake udzadalitsidwa mmadela oyenela ana ake. Udzakhala ndi chimwemwe ndi mtendere woona m'moyo wako. Sudzasowa kanthu kena iye yekha kuti akupangitse kukhala wokondwa. Mutsatileni yesu ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.⁴⁶⁴

MUKHOZA KUKHALA OSIYANITSIKA NDI MULUNGU

Izi ndizofunikila kwambiri: Sungakhale mfulu pokhapokhapo yesu atakumasula.⁴⁶⁵ Pokhapokha mutamulandila mphoto ya yesu, munasiyanisika ndi mulungu chifukwa cha machismo anu.⁴⁶⁶ Wina aliyense amene wasankha kukhala bwenzi wa dziko amakhala mdani wa Mulungu.⁴⁶⁷ Kwa amene sanapulumsidwe kuti mudzipeza ngati mungamufune ndi mtima wonse.⁴⁶⁸ Mulungu sasangalala ndi imfa ya munthu wochimwa.⁴⁶⁹

NANKHA KWA WOKHULUPILIRA AMENE APITILIZABE KUKHALA MUTCHIMO

Nankha kwa iwo amene anamvelapo malamulo amulunga munthawi ina koma anagwa mchisomochi.⁴⁷⁰ Ndipo agwanso mutchimo?⁴⁷¹ Kodi mulungu amawakondabe? Yankho ndiloti Inde Mulungu amawakondabe komabe amakonda owomboledwa ngakhale atachimwa chifukwa mzimu wa mulungu amakhala mwa iwo kuwapembezela.^{472 473}

Koma pali kusiyana pakati pa munthu amene wagwa ndipo akuvutika kuti kuti akhalenso kapolo wa mulungu ndi muthu amene wagwa ndipo salota kubwelela kwa mulungu. Tinganene kuti uyu ndi munthu amene wasankha kupiluzza mofuna yekha kukhala muuchimo. Kwa okhulupilira amene akukana kumvela mawu amulungu Mulungu amamva mapemphero awo koma sawayankha.⁴⁷⁴

Kwa iwo amene anagwa koma akuyesesa kubwela kwa mulungu pemphero lachikhupiliro chabwino lidzampangitsa munthuyo kukhala bwino ndipo ambuye adzamuzutsa ndipo adzakhululukidwa.⁴⁷⁵ Mapemphero adzamvedwa ndikuyankhidwa.

Kusamvera mulungu zitha kuonesa kuti uli mzosangalasa zambir munthawi imeneyo koma sizimabweletsa madalitso ake. Mulungu adzapeleka chibalo kwa okhulupilira akachimwa.⁴⁷⁶ Pakuti mulungu amalanga amene amawakonda.⁴⁷⁷ Wina aliyense amene akhalabe muuchimo amaonetsela kuti sakutsatila malamulo kotelo kuti mulungu sangayankhe mapemphero awo.⁴⁷⁸ Koma mkwiyo wake sufulumila. Mbiri zisangudwa kotelo kuti wochimwa adzalankhulapo pachina chilichonse chimene anachichita patsiku lachiweluzo.⁴⁷⁹ Ili lidzakhala tsiku lachison kwa iwo amene anakhulupililipo yesu ndikumapitilizabe kuchimwa

mofuna okha. Mulungu sadzayankha mapemphero awokhulupilira amene wasankha kukhala muuchimo.⁴⁸⁰

KODI MULUNGU AMADALITSA BWANJI AMENE AMUTSATILA?

Pali madalitso okongola tikamatsatila mawu amulungu. Tikamatsatila mawu amulungu ndikuika chidalilo chathu mwa Yesu zimatipangitsa kukhala ndi chimwemwe choona mu chinachilichonse tingachite, chimene chingatipangitse kulemekeza Mulungu. Ndipo tikamlemekeza mulungu ndipamene amawunjika madalitso ake pa ife. Ndipo tikalandila madalitso zimatipatsa chimwemwe chochuluka. Ndiye ndichimwemwe chathu chochulukacho mmm tiamulemekezabe mulungu, inde mukutha kuona zimene zikuchitika pamenepa.

Amene salemekeza Mulungu adzapitilizabe kuyenda mundima ndipo adzakhala opanda chimwemwe mumiyoyo yawo.

Pakuti Masalmo 128 imati, ^{verse 1} Wodala yense wakuopa yehova m'njira zache. ² pakuti udzuya za ntchito yamanja ako wodala iwe ndipo kudzaku komera. ³ mkazi wako adzanga mopesa wopatsa mmbali za nyumba zako ana ako azanga timitengo ta azitona pozinga podyela pako. ⁴ Tawonani mmwemo adzadalitsika munthu wakuopa yehova.

Kukhala wodalitsika ndikukhala mmoyo mwa ambuye ndikukhala mmoya umene ukugwira ntchito. Ndi moyo wodzadza ndi chimwemwe ngakhale zovuta zitaza panjira yako. Ndimoyo umene umakhala ndichikhalidwe chokondwa ndipo umaona mavuto akutheka ndi mulungu kusiyana ndi amene akukumana nao alibe yesu. Ndimoyo umene umaona kutsogolo ndikumaona zimene zingachitike kutsogolo mmalo momayang'ana pa kalilole ndikumati zikanatha bwaji.

Mantha apa mulungu ndikumlandila yesu mumtima mwako ndi fungulo kuchuma chozazachi.⁴⁸¹

Yohane 15 amati ^{verse 1} Inu simunandisankhe ine koma ine ndinakusankhani inu ndipo ndinakuitanani, kuti mukamuke ndikubala chipatso chochuluka ndikutichipatso chanu chikhale kuti chimene chilichonse mukapempha Atate m'dzinz langa akakupatseni

Ndilonjezo lodabwitsa

NDICHIFUKW CHIYANI ZIKUONEKA NGATI SUKULANDILA MADALITSO?

Ukuyenela kukhala womvera mawu ake kuti ulandile madalitso.⁴⁸² Kukhala osamvera ndikukhala muuchimo nthawi zonse chidzakhala chotchinga kuti usalandile madalitso amulungu.^{483 484} Mulungu amadana ndi tchimo ndipo

amapsa mtima ndi oipa.⁴⁸⁵ Komanso mulungu amakonda wina aliyense ndipo ndi khumbo lake kuti wina aliyense alape ndikupulumutsidwa kotelo kuti adzakudikila modekha kuti utelo.⁴⁸⁶ Mulungu walankhula mobwelezabweleza kudalitsawinw aliyense moposela mmene angaganizire ngati angatsatile malamulo ake.^{487 488}

Kulandila madalitso a mulungu zimatengela kudekha.⁴⁸⁹ Nthawi ya mulungu sinthawi yanu. Nthawi zambiri khumbo lathu ndilokhala ndi madalitso amulungu mwachangu koma mulungu sagwila ntchito chomwecho. Adzakudalitisa nthawi yabwino ikakwana. Ngati ungadikile pa iye inde atha kukhala mulungu akuyesa chikhulupiliro chako.⁴⁹⁰ Kuthekela kwanu kodikila pa iye kudzatengela inu kukhala odalila chimene iye ali ndi ziimene akuchita mmoyo wanu. Mudzidalila nzeru yake, nthawi yake, chikondi chake, chikhululuko chake, ndipo udalile mfundo zake, malonjezo ake, ndi mphamvu zake. Mukuyenela kukhala ndi chikhulupilira monga kambeu ka mpilu. Ngati ungakhale ndi chikhulupiliro ngati kambeu kampilu walonjeza kuti palibe chingakhale cholepheleka ndiwe.⁴⁹¹

Mulungu atumiza madalitso ake kwa amene amufuna ndikumudikila.⁴⁹² Kudikila pa mulungu kumatiphunzitsa kukhala ndicholinga chimodzi ndichokhazikika pa iye monga mwini moyo wathu. Pamene ukudikila usaone ngati ena akupambana ndinjila zao zachitaiko.⁴⁹³ Mulungu atha kukhala tanthwe ndi linga lanu. Ngati muika chidaliro chanu mwa iye maziko anu sadzagwedezeke.⁴⁹⁴ Mutha kutha mphamvu ngatingati mungayese kuchita nokha. Koma mulungu adzapeleka mphamvu kwa otopa ndipo amaonjezela mphamvu kwa ofooka.⁴⁹⁵

MWINA SIMUNAZIPELEKE

Ndizotheka kuti simukulandila madalitso amulungu chifukwa simudzipeleka kwa Mulungu ndi kuziphunzitsa zake.mu maso amulungu mutha kuoneka ngati wofunda.⁴⁹⁶ Zithu zikamakuchitilani bwino mumamukana kenaka choipa chikakuchitikilanimumoyo wanu mumalila ndikumupempha kut chonde konzani vuto langa.” Ndiwe wozizila wofuna kenakonso wozizila kenakonso wofunda ndiye chifukwa sumudalira popanga chiganizommoyo wanu iyeyo angakukhulupilileni bwanji?

Mulungu akufuna kudzipeleka kwanu. Akufuna kudziwa pamene mwayima ndikuonananso ngati mukudalila mumfundo zake. Kusadzipeleka kwa Mulungu ndi mfundo zake ndi vuto lalikulu mdziko lathu lero. Wina aliyense zikuoneka kuti akufuna chilichonse ndipo akuyesesa kuchita zotheka kuti kuti apeze chomwe akufuna, kuphatikizapo bodza, kunama, kukhala osaona mtima angakhale ngugulitsa ena kumene.

Anthu ambiri akuoneka kuti akukhala mmoyo osadzidzipeleka kwenikwen kapena kukhala ndi mffundo. Anthu ambiri amanena chomwe akukhulupilirakoma kuchimvetsela sungatolepo kanthu. Atha kunena kuti

amakhulupilira Mulungu koma sakhala kolingana ndi mfundo za mulungu amatsatila mfundo za mulungu zomwe akufuna ndikusamvera zina ngati kuti zinazo zilibe tanthauzo. Munthu atha kukwatila kungokhala nthaw yochepa banja latha. Atha kupita kuchurch ponyamuka pampando amatha kudula wina ndikugwedeza nkonya izi ndi zovuta komanso ndimoyo wdsadzipoleka umene mulungu amadana nawo.⁴⁹⁷ Mulungu akufuna kudzipoleka kwanu. Ngati simuli watunthu kwa mulungu ndikuzipoleka ku mfundo zake pamenepo mukutsutsana naye. Mudziwe ichi ngati simukukhala mmoyo wodzipoleka umene mulungu atha kukudalilani nawo simungalandile madalitso amulungu.

MUNGACHITE CHANI KUTI MULANDILE MADALITSO AMULUNGU

Mulungu akuyenela kukudalila.

Ungadalilike ndikuyang'anila ndalama zambiri popanda kubwelekapo kapena kuchita nazo umbombo?

Ungapatsidwe udindo watsopano kunchito ndi ulamuliro wowonjezela kopanda kuvulaza anthu kapena kuzitumikila wekha?

Ungasunge chinsisi chofunikila kopanda kuphwanya chidalilo chamunthu?

Izi ndi zina mwa zinthu zimene Mulungu namayang'ana mwa munthu asanakudslitse. Amayenela kudziwa kuti etha kukudalila ndi zinthu zimenezi ndi zambiri. Ndizokhuza khalidwe. Khalidwe lanu ndilokhuza zisankho zomwe mungachite pamene munthu aliyense sakukuona. Khalidwe lanu ndilokhuza ziganizo zimene ungachite ndipo ziganizo zizikhala zokhazikika ndizodalilika ndi mulungu. Mulungu akufuna anthu apamtima pake. Ngati mulungu sangakudalile ndi zisankho zako ndie kuti madalitso adzangokuononga.

Izi ndi zitsanzo zinanso...

Ngati sukhulupilika ndi ndalama akudziwa kuti suzigwilitsa bwino ntchito atakukupasa.

Ngati sukhulupilika ndi ulamuliro adzdzwa kuti atakupasa udzaugwilitsa ntchito udyo.

Ngati sukhulupilika ndi ulamuliro akudziwa kuti atakupasa udzagwilitsa mtchito udyo udindo wako ndi mphamvu.

Ngati sukhulupilika pogawana ndi ena akudziwa kuti atakupasa udzakhala waumbombo ndi zinthu zimene anthu ena anayenela kudalitsidwa nazo.

Ngati sukhulupilika ndi chisinsi cha wina anzako azaphunzila kuti sangakukhulupilire chimozi mozinsu mulungu.

Kuti mulumguapitilize kukukhululukila zochimwa zako akuyenela kudziwa kuti iwenso ukhululukila akakuchimwila.

Kuti mulungu akutumizile madalitso aake ukuyenela kukhala wodalilika ndiponso adziwe kuti nthawi zonse udzachit zolondola angakhale zili zopweteka.

Akuyenela kudziwa kuti akakudalitsa iwenso ukhalanso mdalitso kwa ena.

Ngati nthawi zonse umachita ndikusangalasa gulu mmalo mochita chimene chili chabwino Mulungu adzadziwa kuti sangadalile paiwe kuti upange chiganizo choyenela pamene akuchifuna. Ngati sangakudalire sangakudalitse pamene akudziwa kuti madalitsowo awonongeka.

Mulungu atha kuyesa chikhulupiliro chako kuti akuwone ngati ungadalilike.⁴⁹⁸ Kuyesa chikhulupiliro chako ndi mmene mulungu amapezela muyeso woti atha kukudalila ndi zokakala kapena zoonda, kudzela mmavuto ndi zovuta, kudzela m'zowawandizopweteka'kudzela muzolephela ndi zokhumudwitsa ndi zina zambiri.

MUDZALITSIDWA MUKAZACHITA IZI...

Pamene muli kumapet kwa chungwe chanu⁴⁹⁹

Pamene musunga mtendere pakati pa amene akukutsutsani ndikupanga⁵⁰⁰

Pakuzunzika uku mutagwilitsitsa chikhulupiliro chanu⁵⁰¹

Pakuonesa chifundo kwa amene akuzuzani⁵⁰²

Pakuthandiza osowa⁵⁰³

Pamene mumva mau amulungu ndikuwamvera⁵⁰⁴

Pamene malingalilo anu ndi mtima wanu zili bwino ndi mulungu⁵⁰⁵

Mumupemphe mulungu kuti aike maganizo ndi mtima wanu mofanana ndi mtima ndi malingalilo ake. Muvomeleze khalidwe lanu lowonongeka ndikumupempha mulungu kuti akhululuke machismo anu. Mupemphe nzeru. Mmallo modalila mphamvu zanu tembenuzilani moyo wanu kwa yesu ndikudalila mphamvu zake. Ngati mwatopa mupeza mpumulo wa moyo wanu mwa mulungu.⁵⁰⁶

Ndikuzela mwa mulungu yekha kumene mungazazitse mmalo opanda kanthu onse amoyo wanu. Malo opanda kanthu onse amene mwayesesa kuwadzadza ndi zinthu zachitaiko. Musayese kudzadza malo opanda kanthu amumoyo wanu ndi zinthu za chitayiko. Ndi yesu yekha amene angadzadzitse malo opanda kanthu amumtima wanu.

MPHATSO YA MTENGO WAPATALI KWA ANA ANU

Umakhala mdalitso wa mtengo wapatali pamene tikusamala ena. Anthu ambiri amaganiza kuti ndi anthu okhawa amene akusamalidwa ndi amene amadalitsidwa. Koma kunena zoonza ndizotsutsana. AMene amadalitsidwa ndi amene amasamala ena. Ndi kulimbana ndi kuzikonda kuganizila za zosowa za ena pamwamba pa zosowa zako. Zikutanthauza kudalitsa ena chifukwa wadalitsidwa. Ndikulola madalitso amulungu kudutsila mwa iwe kupita kwa ena.

Kuthandiza ena ndi mphatso ya mtengo wapatali imene tingawapatse ana athu. Ana anu adzaphunzila kuti akadalitsa anthu ena, akuzidalitsa okha. Ndi danga labwino la madalitso limene mulungu watiphunzitsa. Kupatsa kutidalitsa koposa kulandila. Pemphani nzeru ndipo mudzakonda moyo ndipo wosung luntha adzalemela.⁵⁰⁷

Koma osaiwala kuti ngakhale tikudzipeleka kwa mulungu ndipo tikuchita mwakuthekela kwathu kudalitsa ena tizakumanabe ndizovuta, zopweteka, kuzunzika zolimba, chisalungamo ndi zina zambiri. Tikamakumana ndi mayeselo mulungu adzapeleka mphamvu kwa otopa ndipo adzawonjezela mphamvu kwa ofooka.⁵⁰⁸ Tikamakumana ndi zovuta zimakhala zophweka kuyamba khalidwe loyipa ndikumkwiya mulungu, komabe tikuyenela kupitilizabe kukhala ndi khalidwe labwinondi kumukhulupilira mulungu. Mayeselo ndi kuzunzika ndi mipata yomwe tikuyenela kukumana nayo kuti tipeze bwino mwa mulungu.

MUTU 6

KUPANGIDWA NDI CHOLINGA CHOTI NDIGWIRE NTCHITO

MUNALI MU DONGOSOLO LA MULUNGU- MUSANABADWE

MU BUKU LAKE

Munayamba mwadabwapo kuti ndi chifukwa chiyani munabadwa? Munayamba mwadabwapo kuti ndi chifukwa chiyani mulungu anakuikani mu dziko lapansili ndikuti ndichifukwa chiyani mulipo? Pofupifupi tonse tinaganizapo zinthu zimenezi, ndipo nyengo zina pamoyo wathu timakhumba kulumikizana ndi amene anatilenga.⁵⁰⁹ Kutithandiza kuti timvetsetse chifukwa chimene tinabwadwila ndikutithandiza kupeza ntchito yathu ndicholinga cha moyo wathu.

Mulungu ali ndi dongosolo pa moyo wanu. Anali kale ndi dongosolo kale pa moyo wanu musanabadwe.⁵¹⁰ Moyo umene mwakhalamo ndi mavuto amene mwakumana nawo sanangobwela mwa ngozi. Zonsezo ndi mbali imodzi ya dongosolo la mulungu. Kubadwa kwanu ndi tsogolo lanu zinaikizidwa.⁵¹¹ Zonsezo zinapangidwa ndi dongosolo lamulungu ndi cholinga chapadeledela. Zonse zimene mwadusamo zinapangidwa kuti mukule mmoyo wauzimu.

MZIMU WATHU ULI MOTI NDI CHIFUKWA CHIYANI MULUNGU ANABWELA KUDZIKO

Tikayamba kufunsa mafunso otelewa ndiye kuti mzimu wathu ukutikakamiza kuti tiphunzire chifukwa chimene chimene tinalengeledwa ndikufufuza cholinga chathu. Ndi mzimu wokhala mkati mwathu umene mulungu amafuna kuupulumutsa; mulungu anabwela pa dziko lapansi chifukwa cha mzimu wathu. Mulungu sanabwele padziko kudzafela matupi athu. Anabwela padziko kudzafela moyo wathu umene uli mzimu wathu. Matupi athu ndi akanthawi chabe. Matupi athu ndi ofooka ndipo nthawi zonse adzadza ndi mavuto. Zofooka zathu zina zinapangidwa ndi.⁵¹² Matupi athu azapitililabe kulephela chifukwa sanapangidwe kukhala amuyaya. Koma mzimu wathu unapangidwa kukhala wamuyaya, Ndi mzimu wathu umene umapele ka chitsimikizo cha zinthu zili kubwela.⁵¹³

Kukhumba mumtima mwathu kuti tidziwe kuti ndife ndani ndi chifukwa ninji tinabadwa kumayambila njila yatsopano mmiyoyo yathu. Tonse tinabadwa kuti tigwire ntchito. Koma mulungu amazisiya kwa ife kufufuza ntchito kuti ntckitoyo ndi yotani? Mulungu amatipasa mzimu wake kuti ukhale mkati mwathu⁵¹⁴ kutithandiza kupeza yankho la funso lofunikilali. Koma kuti mzimu wa mulungu utithandize, tikuyenela kukhulupilira kuti mulungu anaza padziko mmaonekedwe a yesu kudzatifela. Lyi ndi njira yokhayo imene mulungu angatithandizile. Sangalowe mumtima mwanu pokhapokha mutamuitana kuti alowemo.

Pakuti mwawelenga buku ili kufika pamenepa mutha kuyamba kufufuza mayankho a mafunso amenewa Mutha kumakhumba kuti muphunzire chifukwa chimene munabadwila ndi kuti dongosolo la mulungu pa moyo ndilotani-makamaka ngati mwakhala munyengo zovuta. Mavuto amene mwakumana nawo itha kukhala njila imene mulungu waigwilitsa ntchito kuti mubwelele kwa iye. Anakulengani ndipo amakudziwani, ndipo akufuna kuti mukhale mumoyo wodzadza ndi cholinga ndi moyo watanthauzo. Koma kuti achite zimenezo mukuyenera kumudziwa.

Mulungu akukhumba kuti tonse tisandulike mwakukonzanso kwa mitima yathu⁵¹⁵ kuti tilumikize ndi mzimu wathu ndi kuphunzira cholinga cha mulungu pa miyoyo yathu. Wina aliyense wa ife amadziwa kuchokela pansi pamtima wake kuti pali zambiri koposa kukhala mmene takha tikukhalila. Mulungu sanakhumbepo kuri tifiye pamwamba pa utsogoleri wa maslow wotchedwa kudzikhazikitsa nokha {self actualization} kuzikhazikitsa nokha ndi mawu otsutsana ndi chifunilo cha mulungu pa moyo wanu. Kudzikhazikitsa nokha ndi chimene satana amagwilitsa ntchito kutiwononga.

KULENGEDWA NDIKUTHEKELA KWA MPHAMVU KOMANSO MWAYI

Titayamba kumva zinthunzi menezi mzimu wathu unayamba kudzutsidwa. Ndife mzimu koma ambiri aife sitinazindikile mfundo imeneyi. Mzimu wathu ndiwofunikila kwambiri kuposa thupi lathu, koma mzimu wathu sichinthu chimene tikuyesa kuchimvetsetsa. Koma tikuyenela kuchimvetsetsa. Tili ndi mkati mwabwino ndimokongola mkati mwa mzimu wathu. Ndizovuta kwa ife kuzimvesesa. Koma mulungu akufuna tiphunzire za munthu wamkati mwathu. Mulungu akufuna munthu wamkati mwathu alumikizane ndi mzimu wake. Ndipo kudzera mwa yesu izi zitha kukwanilitsidwa. Moyo wathu wakale ukulukidwa ndi ukadaulo wa mulungu wa kutsogolo, ndipo yesu ndi ulusi umene ungatifikitse kumeneko.

Chifukwa talengedwa mchifanizo cha Mulungu, mzimu wokhala mkati mwathu uzapitilizabe kutitakasa kuti tifike pachi indeinde. Litha kukhala liwu lochepa limene mumutu mwanu mu mphindi imeneyi limene likukutakasa kuti usinthe, kupanga kafukufuku ndikpeza chimene uli. Usakane zimene ukumvazo. Atha kukhala Mulungu akukukankha kukuchotsa mudela limene umamva bwino.

KUMVA KWA KUSAKHUTTSIDWA

Kodi muli ndi vuto kumvetsetsa chifukwa chimene munabadwila? Kusakhuttsidwa kumene mukukumva atha kukhala Mulungu akukulanhkulani kuti mufunefune chifunilo cha mulungu choona pa moyo wanu, musakane zimene mukumvazo. Atha kukhala mulungu akuyesesa kuthandizani kuti musafanizidwe ndi dzikoli⁵¹⁶ kotelo kuti muphunzire chifunilo chake pamoyo wanu. Anakusankhani dziko lapansi lisanalengedwe kuti mukhale oyera ndi opanda bangaku mbali yake. Mwa iye munasankhidwa, owomboledwa kolingana ndi dongosolo lake komanso ndi cholinga cha chifunilo chake.⁵¹⁷

Chifunilo cha Mulungu cha moyo wanu ndichachikulu koposa mmene mungaganizire. Madalitso amulungu adzadutsila mmoyo wanu ndi kudzela mmoyo wanu mukamusatira. Utha kukhala mzimu wa mulungu wokhala mkati mwanu ukukukakamiza kuti mupeze cholinga chimene munabadwila.

Mvetsetlani chimene mzimu ukukuuzani ndipo mukhale ndi chikhulupiliro pakusinthira moyo wanu kuti mukhale ndi moyo ndikuphunzira chifukwa chimene munalengeledwa. Pali golide woona kumapeto kwa mtawaleza, koma zizafuna chikhulupiliro kuti mukafikile.

ZIZATENGA NTHAWI NDI TCHITO

Kunena zoonza kumvetsetsa chifunilo cha mulungu pa moyo wanu sichinthu chimene mudzangopatsidwa mopweka. Padzakhala ntchito yoti mugwire.

Mulungu akufuna mudziwe chifunilo chake; Sakudzibisa kwa inu. Koma mukuyenenela kuzifufuza. Mukuyenera kufufuza kuyambira pakusafanizidwa ndi

zinthu za dzikoli, kumbukilani kuti satana ali ndi ulamuliro pa dziko limene tikukhalali-chimene chikutanthauza kuti ngati mungapitilize kumvela mauthenga adzikoli satana adzasokoneza njira zanu kuti mufanizidwe ndi dzikoli, ngati mungapitilize kufanizidwa ndi njira zake ndi kumvera mauthenga ake adzakutsogolerani kungsi kwa njira zake, ndipo tikudziwa kumene njira zake zikuthera.⁵¹⁸ Njira zake zimatitsogolera ku mdima. Zidzakutsogolerani kutali ndi mtetezi ndi mbusa wanu yesu kristu.

Mulungu akufun wina aliyense kuti apeze cholinga cha moyo wake, koma si wina aliyense amene angapeze kapena kufunafuna. Ndi udindo wina aliyense kupeza cholinga cha Mulungu pa moyo wanu. Palibe wina amene angakuchitileni kupatulapo inu mwini. Kutu muchipeze mukuyenera kuchifunafuna. Mumapeza bwanji chinthu ngati sukuchifunafuna.ndi kuti ntchito ili pakunafunafunako. Njira yabwino imene ungachipezere ndikuwelenga buku la malangizo ake BAIBULOBukuli lapangidwa kuti likuthandizeni ndikukupatsani maso oti muone chimene baibulo likulankhula, baibulo lamaliza kale ndipo ndi mawu amulungu op[and chilema.

MUYITANITSE CHAKUDYA CHATUNTHU

Bukuli linayamba ndikunena kuti chiganizo chachiwiri chimene mungapange-ndikutsegula mtima wako. Pakuwelenga bukuli mwayambapo ndipo mtima wanu mwautsegulaMulungu sadkakamizani njira yake mumtima mwanu. Nthawi zones adzadikila mumuitane kuti alowe. Akudziwa kuti munalengedwa kuti mumudziwe iye kuti ndindani. Mtima wanu ukuyenera kukhala wotsegulabe kuti muphunzire, kumva, ndikukhumba kuti mumudziwe Mulungu kuti ndani. Pali zambiri zoti muphunzire. Pamene mukufufuza kuti mulungu ndindani mudzaphunzilanso kuti mulungu amakukondani kwambiri. Palibe chimene munachita kale kapena chimene mungachite mtsogolo ngati mungalandile mphatso yauleleyi chimene chingakulekanitseni ndi chikondi cha mulungu.⁵¹⁹

Kodi munalandila mphatso yauleleyi? Ngati simunalandile bwelelelani klu mutu 5 pamene pali pemphero loti mupemphere kuti mumulandire yesu ndipo chomwe mungachite ndikukhulupilira kokhs basi. Chitanai ichi tsopano lino. Mudzakhala wokondwa kuti mwapanga ichi. Mukatero ntchito yanu yatha.

MUNGOKHULUPILIRAA

Pano mwadziwa tsopano chifukwa chimene mulungu anabwelelera padziko lapansi pano ndikudzakhala pakati pathu. Ndichifukwa choti amakukondani⁵²⁰ ndipo anabwela kuti adzakupulumutseni. Anabwela kuti adzakupulumutseni ku machismo chinthu chomwe simungachichite pa inu nokha. Ndi Yesu yekha amene angakupulumutseni ndipo ndichimene anachichita. Mulungu anabwela kudziko lapansi kudzapeleka dipo lamachimo anu. Anakufelani.

Ichi chimatitsogolera ku chiganizo chofunikila kwambiri chimene mungachipange kuphunzira kuti mulungu ndindani. Yankho ndilophweka - Ndikukhulupilira mwa Yesu. Mukuyenera klukhulupilira kuti mulungu anaconda dziko lapansi mwana wake yekhayo, Yesu kuti akupulumutseni ku machismo anu, kuti yense wokhulupilira iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha.⁵²¹

Mulungu akuyang'ana. Anakulenga ndipo akuyang'ana kudziipeleka kwako. Ana bwela padziko kudzakufera, nipo chifukwa cha chimene anachichita akufuna adziwe kuti wamkhulupilira. Akufuna adziwe kuti wadziipeleka. Mpaka utadziipeleka ndiponsoatadziwa kuti wakhulupilira mwa iye, adzakuthandiza.

Dongosolo lake linali ndiloyera. Ndi dongosolo limene linalipo kale Adamu atachimwa. Dongosolo la mulungu ndiloti tonse tikhale ndi mpulumutsi. Koma kuti tipulumutsidwe tikuyenera kukhulupilira. Linali ndipo ndi dongosolo loyera, lopangidwa ndi Mulungu woyera. Tikungosoweka kukhulupilira. Yesu ndi ulusi umene ungatengele kumwamba.⁵²²

Palibe njira ina kapena dzina lina limene tingapulumutsidwe nalo.^{523 524 525} Wina aliyense amene angakhulupilire ndikuitanila pa dzina lake adzamasulidwa.⁵²⁶ Izi zikuphatikiza machismo ako akale, atsopano ndi amtsogoro. Timapulumutsidwa mwa chisomo cha mulungu yekha basi.⁵²⁷ Palibe chimene ungachite kuti upeze chiphatso chopitila kumwamba.⁵²⁸ Sungakhale nacho kapena kuchigula. Zikungosoweka kulengeza chikhulupiliro chako mwa yesu.⁵²⁹

ZIMAYAMBA NDI MAWU A MULUNGU

Mutha kumadzifunsa kuti ndingapeze bwanji chifuniro cha Mulungu pa moyo wanga? Chabwino zonsezi zimayamba ndi mawu a mulungu pakuti mawu a mulungu ndiwo chifuniro chake. Musakhale wopusa ndikusamvetsetsa chifuniro cha mulungu pa moyo wanu.⁵³⁰ Chinthu choyambilira pamoyo wanu ndicho kukhala kolingana ndichifuniro chake, ndipo mukamakhala kolingana ndi chifuniro chake mtendere ndi chimwemwe chakumwamba zidzadza mumiyo wako. Apanso ndi pamene madalitso amulungu angayambe kulowa mumoyo awako-ukamakhala kolingana ndi mfundo zake ndipo ukuchita chimene anakuitanila^{531 532}.

Palibe ndondomeko yapadeladela imene ungaitstate kuti upeze chifuniro cha mulungu pa moyo wako. Ukuyenela kukhumba moyo umene walumikizika ndi iye ndikukhala moyo wofanana ndi ndoindomeko zake; Izi zidzayambitsa kafukufuku wauzimu. Ukachita izi mulungu adzayamba kuvumbulutsa mayankho amene wakhala ukuwasaka. Utatha kutsegula mtima wako pemphera ndikupempha mayankho ndipo udzayamba kulandila mavumbulutsa amene angakupatse. Mwachidule mupempheni adzakupatsani. Ndi mzimu wamulungu umene watenga malo mumoyo wanu umene ungakupatseni muyeso wakumvetsetsa ndi chidziwitso chimene umakhumba. Kumvetsetsa kwatsopanoku kudzakupatsani tanthauzo ndi cholinga.

PAMENE MUKUYAMBA ULENDU WANU-MUYESESE KUYENDA PANG'ONO PANG'ONO

Ukachita izi adzabweletsa kuunika mumoyo wako⁵³⁴ ndipo adzakhala kuunika panjira yako.⁵³⁵ Kuunika kwa mulungu kuzakutsogolera pa china chilichonse ungachite⁵³⁶ ndipo kuunika kwake kudzakulola kuti muwalire ena kuti muwadalitse monga mmene mwadalitsilidwa.⁵³⁷ Pakuti ndi mzimu wake umene uli nyali ya A mbuye imene inggabweletse mthunzi mkati mwa mtima wanu.⁵³⁸

Musakhumudwitsike ngati chifunilo cha mulungu sichinachitike nthawi imene mwayambapo ulendo wanu. Mayankho azimene mwakhala mukupemphelera abwela alindila nyeng yoyikika - zili ngati kuyenda ulendo wautali pa mitengo motalika mmene ungayendele umakhalanso wosamala umaonanso zambiri munthawi imene mukuchita kafukufukumuyesese kuyenda pang'onopang'ono chifukwa chuma ndi mayankho amulungu pamapemphero ako ali kuseli kwa mbewu ndi kuseli kwa tanthwe mu mtengo uliwonse, ndi mntsinje uliwonse. Komanso uyesese kuti uwone mitambo yokongola pamene ikuzungulila.

Chuma cha mulungu ndi madalitso ake adzabwela kwa iwe mu njira zosiyanasiyana. Kuti udziwe madalitso amulungu ukuyenera kukhala watchuru, ndipo ukakhala tcheru madalitso ake ayamba kukulankhula.⁵³⁹ Nthawi zambiri timayenda timafulumila zomwe zimapangitsa kuti tisawone madalitso ake. Izi zimachitika tikalola dziko kusukunula miyoyo wathu ndipo timayenda mofulumila. Chimodzi cha zolinga za satana ndikutipatsa khungu kuti titanganidwe ndi ntchito, kanema[tv], kompyuta, magazine, fesibuku, whatsapp ndi zinthu zina kuti tisawone kapena kuwona madalitso amulungu, kapena kumuona mulungu kumene. Kumbukilani kuti satana safuna kuti mumuone mulungu pa moyo wanu ndiye satana adzachita chotheke kukupangitsani kuti muyende mwachangu kuti musamuone madalitso amulungu. Chepetsani liwiro ndipo mumukanizekutanganidwa kwa satana adzakuthawani.^{540 541}

Pamene mwayamba ulendo wanu dalilani ambuye kuti avumbulutse zochuluka za chifuniro chake pa inu. Khazikikani kuti iye amene anayamba ntchito yabwino pa inu adzaimalizitsa.⁵⁴² Pakuti cholinga cha mulungu ndichoti mwana wake yesu alemekedzedwe ndikuti uthenga wake wabwino ulalikilidwe dziko lonse lapansi.⁵⁴³

CHIFUNIRO CHA MULUNGU SICHINGAGANIZIRE ZA LUSO LANU KAPENA KUTHEKELA KWANU KWA CHILENGEDWE

Tsopano tikudziwa kuti mulungu wapeleka kwa wina aliyense mphatso yosiyana, luntha losiyana, ndikuthekela kosiyana.⁵⁴⁴ Tonse tinapangidwa mosiyana. Ena mwa ife tinapatsidwea mphatso za zojambulajambula ena za sayansi, ena kuthekela kosamala anthu ena, ena ndi aluso kukhala mayi kapena bambo ndikulera ana ena amachita bwino pankhani za masewero, ena kuphunzitsa, ena

amakaniko, ndipo mndandawu ukupitilira. Tonse maluso athu akuchokela kwa mulungu.⁵⁴⁵

Kulakwitsa kumene ambiri a ife timachita ndi koti timaona ngati chinthu chimene timatha kuchichita bwino ndichimene chilli chifuniro cha mulungu pa moyo wathu. Timaganiza kutingati timatha bwino chinachske zitha kuthandauza kuti mulungu akufuna agwilitse ntchito chimenecho kuti tikudze ufumu wake. Izi inde zitha kukhala zoonza koma tiyelekeze kuti zikhala choncho. Mulungu wapeleka kwa wina aliyense luso kuthekela talenti zomwe ndizabwino, koma ngati maso athu angakhale pazimenezo pamene tikufunafuna chifuniro cha mulungu pa moyo wathu-tiha kuphonyana ndichinthu chofunikila kwambiri pa moyo wathu. Tikuyenela kudalira pa mulungu kuti atikwanise mumadela amumoyo wathu.⁵⁴⁶
^{547 548 549 550 551} Chifunirocha mulungu ndikuphatikizapo ubale pakati pa ife ndi iye, kumufuna kumutsatila,⁵⁵² ndikukhala mumoyo wolingana ndi mfundo zake.

MUSASEMPHANITSE ZINTHU KAPENA KUPANGA CHIDULE

Ngati timachita bwino pa china chake ndipo nga bwino kuti sitisowa thandizo kuchokela kwa munthu wina apa ndi pamene tingalakwitse zinthu zimene mulungu akukhumba kuchita pamoyo wathu. Chifuniro cha mulungu pamoyo moyo wathu ndichachikulu kusiyana ndikuma khala ndi chidwi pa luntha ndikuthakela kwathu. Mulungu akufuna tikhale ndi chikhulupiliro mwa iye. Mulungu akufuna tikwanilitse zinthu zimene sitikanakwanilitsa kopanda iye [monga kulemba buku]. Tikakwanilitsa zinthu zimene kopanda iye sitikanakwanisa zimalimbikitsa chikhulupiliro chathu mwa iye ndipo tidzadza ndi mathokozi.⁵⁵³

Cholinga chathu chikhale kukhala mumoyo umene ungamusangalase Mulungu ndikulola mzimu woyera mkati mwathu kuti handiza ndikutsogolera ziganizo zathu za tsiku ndi tsiku. Pakuti ambuye aakuti adzadalitsa amene amutsatila iye.^{554 555}

MADALITSO ADZATULUKA

Mukamakhala kolingana ndi chifuniro cha mulungundipo mukugwila ntchito kukwanilitsa cholinga chanu. Mulungu adzakupatsani mtendere ndi chimwemwe chake.^{556 557 558} Iyi ndi mphatso ya mulungu kwa inu, kuti mudalitsidwe ndikuti mukadalitse enanso. Mphatso yake idzaphatikizidwa ndi kulumvba mtima mu chinachilichonse chimene mungachite.⁵⁵⁹ Mulungu akuthandizanso kupanga ziganizo zofunikila, ziganizo zopheka kulongosola-chimene chingakuwonjezeleni mtendere.

Khulupilira yehova ndi mtima wako wako wonse, osachilikiza ku luntha lako. Umlемеkeze m'njira zako zonse, Ndipo iye adzaongola mayendedwe ako.

Miyambo 3:5-6

Koma izi sizitanthauza kuti simudzakhala ndi zovuta ndi zolimba. Musaiwale nthawi zone mudzakhala ndi mavuto koma monga wokhulupilira dzikondweletseni mwa muzofooka zanu, zolimba, masautso, ndizovuta-paakuti pamene muli ofooka mutha kukhala wamphamvu.⁵⁶⁰ Mukapilira mupilira muzovuta mudzalandila chimene wakulonjezani.⁵⁶¹ Pakuti yesu wawina nkondo. Nkhondo yatha.⁵⁶² Yesu waligonjetsa dziko lapansi.⁵⁶³

Chimwemwe cha mtima wanu chidzapeza chifunulo cha mulungu pamoyo wanu. Sungani mawu amulungu monga maziko pamoyo wanu ndiyang'ana dongosola la mulungu pa moyo wanu. Apa ndipamene mungayambe kulandila zina zowonjezera momwe moyowako umakhalira mu zomangamanga zake zaulemelero wake. Kutsogolo kakukongola kwake.

MPHATSO ZIMENE MWALANDILA SIZANU

KHALANI MOGWILIZANA

Tinaphunzira mu mutu 2 kuti mulungu anatilenga mosiyana ndi wina aliyense ndipo mulungu analenga munthu wina aliyense mwapadeladela ndiwamtengo wapatali ndicholinga. Tinaphunziranso kuti ali ndi dongosolo ndi cholinga pw munthu aliyense ndipo dongosolo lake likhala kufikila mibadwo mibadwo.⁵⁶⁴

Mutha kumazifunsa nokha: Pakuti ndife osiyana tingagwire ntchito limodzi motani kuti tilemekeze mulungu? Zikumveka ngati ukukhala ndikugwila ntchito limodzi mgwilazano⁵⁶⁵ ndi wina ndi mzake chifukwa umu ndi mmene mulungu anatipangila kuti yikwanilitsane wina ndi mzake.

Chitsanzo chachikulu ndi thupi lanu. Thupi lanu lili ndi zikwi za ziwalo ndipo chiwalo chilichonse zinapangidwa modabwitsa ndipo zimatha kugwilira ntchito limodzi mu umodzi komanso mogwilizana. Zili chimodzimodzi inu ndi ine ndi wina aliyense womkhulupilira Yesu. Ndichozizwa cha kusiyana kwathu zizatilola kugwilira ntchito limodzi ndi muumodzi mwachikhulupiliro mwa Yesu. Ndikudzela mwa Yesu yekha kuti kusiyana kwathu kutha kupangidwa ndikukhala kwapumphu muumodzi kolingana ndi cholinga chake.⁵⁶⁶

MUKAKHULUPILIRA - MULUNGU AMAKUPATSANI MPHATSO YA PADERA

Pamayambiliro penipeni pamene mwapemphera pemphero pa mutu 5. Apa ndi pamene mzimu wa mulungu akhazikika mu mtima mwanu⁵⁶⁷ pa nyengo imeneyi ndi pomwe mulungu amakupatsani mphatso yapaderadera.⁵⁶⁸ ndipo mphatso imeneyi idzapeereka mfundo zenizeni za kupezeka kwa yesu m'moyo wanu⁵⁶⁹ zomwe zingathandize kumvetsetsa komanso kukhala mu chifuniro ndi nzeru za yesu.⁵⁷⁰ mphatso yapaderayi ndiyo madalitso ochokera kwa mulungu. Izathandiza kutumikira ena ndipo inunso kumanga ufumu wake mu ngwirizano komanso kuzichepesa ndi ena okhulupilira.

Pakuti mphatso ya uzimu imeneyi izathandiza kumanga zolinga pa moyo wanu. Ndizofunikira kuti muzindikire mphatso yomwe mulungu anakupatsani⁵⁷¹ chifukwa pa mphatso zosiyana zambiri zimene mulungu anapereka kwa anthu ake.⁵⁷² Anthu ena adzalandira mphatso imodzi, ndipo ena analandira mphatso zambiri. Koma kuthekera kulipo kuti aliyense azalandila mphatso ya uzimu imodzi kuchokera kwa mulungu mukamulandila yesu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu.

Mphatso yomwe mulandire ndi ntchito yochokera kwa mulungu⁵⁷³ ndichikhumbokhumbo kuchita ntchito mkatikati mwa thupi la khristu. Mphatso yanu iperekedwa kwa inu pamodzi ndi mphamvu zapadera zomwe zingapangitse kuti ntchito yanu isakhale yopanda ntchito komanso ya chimwemwe. Mwamvetesa zimenezo? Mungagwiritse ntchito mphatso yanu potumukira ena ndipo muzakondwera nawo pa kuti zimenezi simuyenera kusankha mphatso yanu chifukwa mwini wake mulungu anakusankhirani koma musadere nkhowa chifukwa mudzakondwera ndi mphatso yomwe muzalandila.⁵⁷⁴

Mukazalandila mphatso yanu muzapasidwa mwayi kuti mukhazikike nawo. Ndipo mudzakhala nawo ukadaulo. Zimene zikutanthauza kuti ngakhale mulungu ngapereke mphatso ya mphamvu ya padera muzakhala ndi mpata ochita kuposera pamenepo. Zindikirani mphatso yanu ndipo muimvetse chomwe ikukamba komanso momwe mungaigwiritsire ntchito.⁵⁷⁶ Munadalitsidwa pa cholinga.⁵⁷⁷ Mulungu akufuna mukhale mu ntchito yake iye ndiwa mtengo wapatali kotero anapeleka mphatso kwa aliyense amene wapulumutsidwa ndi mphatso yodabwitsa imeneyi.

LUSO LANU NDI KUTHEKERA KWANU SIZOMWE INUYO MUMAGANIZIRA

Musaganize kuti luso lanu kuthekera ndi mphatso ya uzimu. Mphatso ya uzimu yomwe mulandile pamene mwalndila yesu pa moyo wanu ndi chifundo cha mulungu chimene chingakupangitseni kukhala wa m, phamvu ndi kutumukira ena. Mphatso yanu ya uzimu imapelekedwa kwa inu pofuna kukulimikitsani mu dera lanu kuzera mwa yesu. Kupeleka mphamvu kuti muthandize anthu ena, mosakakamiza.

Mwachiziwikire tikamagwiritsa ntchito luso lathu lawambali sitifunanso mulungu thandizo lake. Koma mulungu amafuna kuti tizinfusa kuti atithandize kukwanilitsa zinthu zomwe zimaposa iwo lathu komanso kuthekera kwathu. Mphatso ya uzimu yomwe amapeleka yomwe amapeleka mulungu imatipatsa mphamvu kukwanilitsa mphamvu zake. Lzi ndi zina mwa mphamvu za uzimu zomwe mulungu amapeleka kwa okhulupilira ake. Pali mphatso za uzimu zoposa 20 zomwe zili mu baibulo ndi m'ndandanda uli m'musiwu ndi ochepa chabe. Anthu ena amalandila imodzi mwa mphatso zimenezi ndipo ene amalandila zochulukira, mukawerenga m'ndandandawu muzaona kuti muli ndi imodzi kapena zambiri

mphatso zimenezi ndipo mumasangalala pozipanga, zimaoneka zosakakamiza kwa inu, zingathe kukhala mphatso yanu ya uzimu.

Mu dongosolo lake:

1. Mphatso ya utsogoleri: mphatso yosogolera

Chofanizira: 1 Akorinto 12: ²⁸ Ndipotu mulungu anaika ena a eklesia, poyamba, atumwi, achiwiri, aneneri, achitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso za machilitso, mathandizo, maweruzo, malilime a mitundu mitundu.

2. Mphatso ya zaluso: mphatso ya kupanga zinthu za luso.

Chofanizira: Eksodo 31: ³ Ndipo ndamdzadza ndi mzimu wa mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi chidziwitso, ndi ntchito zilizonse, ⁴ kulingalira ntchito za iwo, kuchita ndi golidi ndi siliva ndi mkuwa ⁵ kuzokokota miyala yoikika, zokokpta imapangitsa

3. Mphatso ya kuzindikira: kudziwa chomwe chili choipa komanso chabwino cha cholinga cha mulungu.

Chofanizira: 1 Akorinto 2: ¹² koma sitinalandila ife mzimu wa dziko lapansi koma mzimu wa kwa mulungu kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi mulungu kwa ufulu.¹³ zimenezo tilankhula si ndimaphunzitsidwa ndi mzimu, ndi kulinganiza zamzimu ndi mzimu.

4. Mphatso ya utumiki: mphatso yomwe imapangitsa okhulupilira kufikira ena osakhulupilira kuti akhale a khristu odalilika

Chofanizira: Aefeso 4: ¹¹ Ndipo iye anapatsa ena kuti akhale atumiki ndi ena aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena aphunzitsi,¹² kuti akonzekere oyera mtima ku ntchito ya utumiki, kumangilira thupi la khristu, kufikira ife tonse tikafikire ku umodzi wa chikhulupiliro, ndi wachizindikiro cha mwana wa mulungu kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha khristu.

Komanso 2 Timoteo 4: ⁵ Koma iwe khala maso n'zonse, imva zowawa, chita ntchito ya ulaliki w uthenga wabwino, kwaniritsa utumiki wako.

5. Mphatso ya chilimbikitso/kuzoza

Chofanizira 3 Yohane 1: ⁷ Pakuti chifukwach dzinali anatuluka, osalandila kanthu kwa amitundu. ⁸ chifukwa chache ife tiyenera kulandila otere, kuti tikhale othandiza nacho choonadi.

6. Mphatso ya chikhulupiliro: mphatso yomwe imapeleka maso kwa okhulupilira kuona mzimu ndikutha kugwilitsa ntchito.

Chofanizila: Aefeso 2: ⁸ Pakuti muli opulumusidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiliro, ndipo ichi chosachokera kwa inu chiri mphatso ya mulungu.

7. Mphatso yakupeleka: mphatso yomwe imapangisa okhulupilira kuzindikira madakitso amulungu ndikutha kugwiritsa ntchito pakukhala opeleka nthawi ndi luso

Chofanizila 2 Akorinto 9: ⁶ Kom ndi ti ichi kuti iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso azatuta, ndipo iye wakufetsa molowa manja, molowa manjaso azatuta ⁷ yense achite monga anasimikiza mtima, mwa chisoni kapene mokakamiza, pakuti mulungu akoda wopereka mokonderera ⁸ ndipo mulungu akhonza kuchulukitsa chisomo chake kwa inu, kuti inu pokhala nacho chikwaniro chonse n'zinthu zonse, nthawi zonse mukchulukire mu ntchito yonse ya bwino.

8. Mphatso ya kuchilitsa: mphatso yomwe okhulupilira amagwiritsa ntchito mphamvu ya kuchilitsa ya ambuye.

Chofanizira 1 AKORINTO 12: ⁷ Koma kwa yense kwaperekedwa maonekedwe a mzimu kuti apindule nawo. ⁸ pakuti kwa m'modzi kwapatsidwa mau a nzeru koma kwa nzake mau a chidziwitso monga mwa mzimu yemweyo. ⁹ kwa wina chikhulupiliro, win mzimu mmodziyo. ¹⁰ ndi kwa wina mahitidwe a mphamvu, ndi kwa wina chinenero, ndi kwa wina chidzindikiro cha mizimu, kwa wina malilime a mitundu mitundu, mamasulidwe. ¹¹ koma zonse izi achita mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense pa yekha mmene afunira.

9. Mphatso ya kulandila: mphatso ya kulandila alendo, makamaka omwe ali osowa chomwe akhulupilira alinawo.

Chofanizira: Aroma 12: ¹³ patsani zosowa oyera mtima, chezelani aulendo.

10. Mphatso ya kupembeza: mphatso yopangitsa wokhulupilira kupemphera zolinga kuti mapemphero awo ayakhidwa.

Chofanizila: Aefeso 6: ¹⁸ mwa pemphero lonse ndi pembezera mupemphere nthawi zonse mwa mzimu, ndipo pochezera pamenepo tichezere ndi kupembedza oyera mtima onse.

11. Mphatso ya nzeru: mphatso yakuzindikira komanso kumvetsa ziphunzitso ndi malonjedzo ayikidwa m'baibulo

Chofanizira: 1 Akorinto 12: ⁷ koma kwa yense kwapatsidwa monekedwe a mzimu kuti apindule nawo. ⁸ pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa kwa mzimu mau a nzeru, koma kwa nzake mau a chidziwitso monga mwa mzimu yemweyo. ⁹ kwa wina chikhulupiliro mwa mzimu mmodziyo, ¹⁰ ndi kwa wina malilime a mitundu mitundu, ndi kwa wina mamasulidwe a malilime. ¹¹ koma zonse izi achita mzimu yemweyo nagawira yense a yekha monga afuna.

12. Mphatso ya utsogoleri: mphatso yomwe imapereka chilimbikitso kwa okhulupilira kukonzekera za patsogolo.

Chifaniziro: 2 Timoteo 4: ² lalikira mau, chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndikuleza mtima konse ndi hiphunzitso. ³ pakuti idzafika nthawi imene sazalola chuphunzitso monga mwa zilakolako za iwo okha ⁴ ndipo adzaluza dala pa choonadi nazapatukir kusata nkhani zachabe, ⁵ koma iwe khala maso n'zonse, imva zowawa, chita ntchito ya mlaliki wa uthenga wabwino, kwaniritsa utumiki wako.

13. Mphatso ya chifundo: mphatso yolimbikitsa okhulupilira kukhazikika maka kwa omwe ali osowa ndikupanga zotheka ndikuthandiza p mabvuto.

Chifaniziro: Luka 10: ³⁶ uti wa awa atatu, uyesa iwe, unakhala mnasi wa iye uja anagwa m'manja mwa achifwamba. ³⁷ ndipo anati kwa iye wakuchitira chifundo, ndipo yesu anati kwa iye, pita nuchita iwe momwemo.

Komnso Mateyu 25: ⁴⁰ ndipo mfumuyo idzayankha nizati kwa iwo, indetu, ndinena kwa inu, chifukwa munachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale ng'onoang'ono awa munanduchitira ichi ine.

14. Mphatso ya maimbidwe: mphatso ya kupereka kuthekera kolimbitsa ena kuzera m'maimbidwe ndi zipangizo.

Chofanizira: Masalmo 100: ¹ fuulirani kwa yehova, inu dziko lanu lapansi. ² tumikirani yehova ndi chikondwelero, idzani pamaso pake ndi kuyimbira mokondwera.

Komanso: Masalmo 150: ³ lemekezani ndi kulira kwa lipenga, mlemekezani ndi chisakasa ndi zeze ⁴ mlemekezani ndi lingaka ndi

kuthira mang'ombe. ⁵ mlemekezeni ndi nsanje zomveka, mlemekezenindi nsanje zoliritsa.

Komanso: Masalmo 149: ³ alemekeze dzina lache ndikuthira mang'ombe ayimbire zolemekeza ndi lingaka ndi zeze.

15. Mphatso ya kulosera: mhatso yomwe okhulupilira amalosera za patsogolo zoon.

Chofanizira: 1 Akorinto 13: ² ndipo ndingakhale ndikhoza kunenera, ndipo ndingazinve zinsisi zonse, ndi nzeru zonse, ndipo ndili nacho chikhulupilira chonse, kuti ndikasendeza mapiri, koma ndiliba chikondi ndiri chabe.

Komanso: 1 Akorinto 12: ⁷ Koma kwa yense kwaperekedwa maonekedwe a mzimu kuti apindule nawo. ⁸ pakuti kwa m'modzi kwapatsidwa mau a nzeru koma kwa nzake mau a chidziwitso monga mwa mzimu yemweyo. ⁹ kwa wina chikhulupilira, win mzimu mmodziyo. ¹⁰ ndi kwa wina mahitidwe a mphamvu, ndi kwa wina chinenero, ndi kwa wina chidzindikira cha mizimu, kwa wina malilime a mitundu mitundu, mamasulidwe. ¹¹ koma zonse izi achita mzimu mmodzi yemweyo, na gawira yense pa yekha mmene afuna.

16. Mphatso ya kutsogolera ndi kutumikira: mphatso yomwe okhulupilira kuthekera kopleka utsogoleri wa mzimu ndinso kupeleka njira kwa anthu komanso gulu.

Chofanizira: 1 Timoteo 3: ¹ mawuwa ali okhulupilika ngati munthu akhumba udindo wa oyang'anira, aifuna ntchito yabwino.

Komanso: 2 Timoteo 4: ¹ ndikuchitira umboni pa maso pa mulungu ndi yesu khristu amene adzaweruza amoyo ndi akufa, ndipa maonekedwe ake ndi ufumu wake ² lalikira mau, chita nuopa nthawi yake, tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima, konse ndi chiphunzitsa.

17. Mphatso ya kuchita ntchito: mphatso yomwe imapangitsa okhulupilira kutumikira ena kuti ntchito yake ya mulungu ikwaniritsidwe.

Chifaniziro: Aroma 16: ² kuti mulandile iye mwa ambuye, monga kuyenera oyera mtima, ndikuti muthandize n'zinthu zilizonse adzazifuna kwa inu, pakuti iye yekha anali osungira ambiri ndi ine ndemwe.

Komanso: Filipi 2: ¹⁹ koma ndiyembekeza mwa ambuye yesu kuti ndizatumiza timoteo kwa inu nsanga, kuti inenso nditonthozeke bwino

podzindikira za kwa inu. ²⁰ pakuti ndiliba wina wa mtima womweo, amene adzasamala zakwa inu ndi mtima woona, ²¹ pakuti onsewa asata za iwo okha, siza yesu khristu.

18. Mphatso ya zaluso za manja: mphatso yomwe imapangitsa kuti okhulupilira kupanga, komanso kukonza zinthu zoonongeka.

Chifaniziro: Eksodo 31: ³ Ndipo ndamdza ndi mzimu wa mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi chidziwitso, ndi ntchito zilizonse, ⁴ kulingalira ntchito za iwo, kuchita ndi golidi ndi siliva ndi mkuwa ⁵ kuzokokota miyala yoikika, zokokota mtengo, kuchita nthito zilizonse.

19. Mphatso ya kuphunzitsa: mphatso yomwe okhulupilira amalumizana komanso kumvetsetsa zinthu kuti zizkhala kuti zizkhala zapamwamba komanso zosavuta kumvetsetsa kwa ena.

Chofanizira: 1 Akorinto 12: ²⁸ ndipotu mulungu anaika ena m'lekezi, poyamba atumwi achiwiri, aneneri achitatu, aphunzitsi, pamenepo zozizwa, mathandizo, maweruzo, malilime a mitundu mitundu.

Komanso Machitidwe 18: ²⁵ iyeyo anaphunzitsidwa m'njira ya ambuye, pokhala nawo mzimu wachangu, ananena ndi kuphunzitsa mosamalira zinthu za yesu, ndiye odziwa ubatizo wa yohane wokha, ndipo iwo anayamba kulankhula molimba mtima musunagogi, ²⁶ koma pamene anamumva iye puliskila ndi akulu anamtenga nanfototera njira ya mulungu wosamalitsa.

20. Mphatso ya nzeru: mphatso yomwe okhulupilira amapeleka nzeru pa zinthu.

Chofanizira: Yakobo ¹³ munthu poyesedwa, asananena, ndi ziyesedwe ndi mulungu sakhoza kuyesedwa ndi zoipa, ndipo iye mwini sayesa munthu. ¹⁴ koma munthu aliyense ayasedwa pamene chilakolako chake iye chinkozera ndi nichim'nyenga.

21. Mphatso ya kulemba: mphatso yomwe ipereka kuthekera kwa okhulupilira kuonetsetsa ziganizo, maganizo ndi zoonza zazolembedwa.

Chofanizira: 1 Yohane 2: ¹² ndikulemba tiana popeza machismo anakhululikidwa kwa inu mwa dzina lake ¹³ ndikulamberani atate, popeza mwazindikira iye amene ali kuyambira, pachiyambi, ndikulembani anyamata, popeza mwalaka oipayo. Ndakulembani ana popeza mwazindikira atate.

Komanso: 1 Timoteo 3: ¹⁴ koma chisomocha ambuye wathu chizachulukatu pamodzi ndi chikhulupiliro ndi chikondi chiri mwa khristu yesu. ¹⁵ mauwa ali okhulupilira ndi oyenera konse kuti awalandire kuti khristu yesu anadza ku dziko lapansi kupulumutsa ochimwa wa iwowa ine, ndine woposa.

Komanso: Oweruza 3: ³ anasiya mafumu asanu Afilisiti ndi Akanani onse ndi Asideni ndi Alivi okhala kuphiri la Lebano kuyambira phiri Baulaherimeni mpaka polowera ku Hamani.

MPHATSO YANU YA UZIMU ILIBE PHINDU KWA INU NOKHA NDIYOTI MUTUMIKILE NAYO ENANSO

Musanayesere kudziwa kuti mphatso yanu ya uzimu ndi chani ndi bwino kukumbukira kuti, simphatso yanu yokhayo yomwe ndiyo funika potumikira mulungu. Mulungu anaitana tonsefe kuti tikhale omvera pomutumikira mbali zonse osati mbali yokhayo yomwe ukukhulupilira kuti mphatso yomwe mulungu anakupatsani choncho sungapeze ndipo ungazakodwe mu mphatso yomwe umafuna kuti uzamutumikire mulungu.

Pofuna kukukonzekeretsa kuchofunika cha padera monga kulimbikitsa anthu ena. Umu ndi m'mene mulungu angakupasire mphatso ya uzimu ndi m'mene ungaigwiritsire ntchito ndipo palibe njira ya masenga yomwe ungaziwire mphatso yako ya uzimu. Mzimu woyera umagawa mphatso monga momwe amadziwira kuti izi ndizo zabwino⁵⁷⁷ pali njira zambiri za uzimu zomwe zingathandize kudziwa mphatso yanu ya uzimu koma njira zimene ndizo zosadalilika kuti zingapereke yankho lolondola kuti mphatso yanu ndi iyi.

Kodi mukuziwa njira yabwino yodziwira mphatso yanu? Pezani malo otumikira ndikuyamba utumiki wanu⁵⁷⁸ ndipamene wayamba kutumukira m'pamene umadziwa kuti iyi diyo mphatso yanga monga kuyerekeza zimafuna kuyetsera ndi kulephera ndipo pamapeto pake umadzaziwa mphatso yako ya utumiki koma uyenera kukhazikika potumikira anthu ena osati iwe mwini.

Ukhonza kufunsa, nthawi zina anthu ena amadzaona mbali yomwe ukutumikira mwa mphamvu mbali yoti wekha sungaiziwe. Zomwe anthu ena amona zitha kukuonetsera komwe utumiki wako uli. Ngati sunalimbikitsidwe pamene ukugwiritsa ntchito mphatso yako mbali inayake, mulungu sakuitane kuti umutumikire mbali imeneyo pakuti amadziwa mphatso yako ndi mzimu woyera yekha, fusain mulungu kuti akuonetsereni kuti mwadalitsidwa bwanji.

Ngati chikumbutso chabe kudziwa mphatso yako sichozitetezera pomutumikira mulungu mu utumiki omwe si mphatso yako, kulimbikira kwambiri mphatso yako ya uzimu kuntha kukusemphanisa ndi mwayi ofunika kwambiri kutumikira mulungu.

Monga Afilipo 2 anena nati, ¹³ “poti ndi mulungu akugwira ntchito mwa iwe muchifuniro chake ndi kuchita mokwanilitsa cholinga chake.

Ngati ukukwanitsa kudziwa mphatso yako ya uzimu zidzakuthandiza kugwira ntchito yabwino yomwe mulungu anakukonzera.⁵⁷⁹ Mphatso yako ya uzimu imagwira ntchito mogwirizana ndi nzeru komanso kuthekera kwako kwa chibadidwe zomwe mophatikizana zidzakhala za mphamvu yovuta kumvetsetsa mu ufumu wa mulungu. Molumukizana ndi anthu ena okhulupilira mphatso yako ya uzimu zidzathandiza kudziwa chifuniro cha mulungu nndi moyo wako kungofunika kukula m'chikhulupiliro ndi kudalira ambuye kuti akulondolere njira ndi dera lomwe analitsankha kuti ukatumukire.

MPHATSO YANU SIYANU

Choipitsitsa chimene mungapange ndikubisa mphatso yanu osaigwiritsa ntchito kapena kugwiritsa ntchito mphatso mopindulira iwe mwini zimenezi sizomwe mulungu amafuna, mulungu amafuna aliyense mwa ife kuti tigawane mphatso zathu pomutumikira⁵⁸⁰ munapatsidwa mphatso kuti mukawalitse ndikulemeletsa dziko makamaka pogwiritsa ntchito kutumukira ena. Poti ndizodabwitsa za kusiyana kwathu mwa ambuye wathu yesu khristu ndikukhala ndikutumikira mwa umodzi.

Mphatso yanu iyenera ifalitsidwe ndi kudalitsa ena mu ntchito zanu osati imatanthauza kuti ibweretse chisangalalo kwa inu nokha, mwanjira ina mphatso yanu ndu ulemelero wa mulungu ndipo ngati mukugwiritsa ntchito mphatso yanu potumikira ena mukubweretsa umodzi wa thupi la yesu khristu ndipo ngati thupi lake lili mu umodzi uzathandizira kukulitsa mzimu oyera m'mitima ya okusatira.

Izi ndizofananirapo ndi kupanga masewero olimbitsa thupi pamene ukupanga masewerowa thupi limakhala lolimba ndi lochangamuka ndipo timakhala anthanzi ngakhale mafupa ndi ziwalo ndi zimodzi, miyendo ndiyosiyana ndi maso ndipo maso ndiosiyana ndi mtima. Masewero olimbitsa thupi amapangitsa kuti ziwalo zonse zikhale zanthanzi ndikugwira ntchito bwino, tingalemekeze mulungu ngati timutumikira mogwirizana⁵⁸¹ chikhulupiliro chathu chimakula mwasanga ngati tinyozedwa ndi okhulupilira ena ndipo ngati tikhala molemekeza mulungu mzimu woyera amene ali mwa ife adzatilimbikitsa ndi kutilimbitsa mu uzimu.

Kukula ndi kukhwima mu uzimu ndi nkhani yaitali pamene chikhumbokhumbo chofuna kudziwa chifuniro cha mulungu ndi moyo wako chikukulirakulira pameneso mulungu amaulura zambiri pa moyo wathu. Choncho tiyenera kudzikhutula kwambiri pokweza mulungu pokulitsa moyo wathu wa uzimu.

MOYO WANU UMAKHALA OSAVUTA

Munakhalapo ndi nzanu yemwe anakulonjezani amakhala wodabwitsika ndipo ndizoona Pali zinthu zina zomwe m'moyo wathu timakumana nazo zomwe

ndizodabwitsa ndipo zimakweza mphamvu zathu nthawi zina ngakhale ife osadziwa. Nthawi zina zakhala zikukuchitikirani nkhalani ndi kuganizira chomwe chayambitsa kuti zichitike mwina zingakhuzane ndi mphatso yanu ya uzimu.

Kodi ndi zinthu ziti zomwe mumachita bwino kuposa ena zomwe zimakubweretserani chimwemwe? Mwina ndi kusamalira ana kapena kumanga zinthu. Mwina kuimba gitala kapena piyano kapena chida choyambitsa chilichonse. Mphatso yathu ya uzimui iri ngati mbeu yomwe tizala ndikuthira feteleza kuti zikule ndikubeleka zipatso zokongola ngati tingatero zilibwino ngati sitiziwa mbeu yathu sitingathire feteleza oyenera, kuithilira ndi madzi ambiri kapena kuipatsa dzuwa lochepa kapena lochuluka kwambiri ndipo ngati tingonvera mphatso yathu singabeleke monga mabere.

Tiyenera kudziwa mbeu yathu (mphatso yathu ya uzimu) kuti ikule m'meme imakulira ngati tikusamalira mbeu yathu ndipo mosatira udindo wathu, mulungu adzaona kukongola kwa mauwa omwe zingatulutse ndipo adzaulula malo ena omwe mauwa angazazidwe ndi kudalitsa ena pamene titsatira mulungu tizalandira mphatso zopanda malire kuti tipange ndi kugawa mauwa kwa anthu ena.

MWINA MUNGALAKWE MAYESO ANU

Pangakhale nthawi zina zomwe mungapange kuti mphatso yanu ndiyokhayo yomwe ilindikuthekera ndikuti okhulupilira ea omwe ali ndi mphatso yosiyana ndi inu safunikira zomwe inu mukutumikira koma zimenezi sizolondola chifukwa sitikumvesa ndipo sitizamvetsetsa mphatso zomwe ena apasidwa.

Tonse tapasidwa mphatso zofanana koma chifukwa choti wina alindi mphamvu zosiyana ndinu sizikutanthauza kuti iye sanadzipereke ngati inu koma zikutanthauza kuti mphatso yake ndiyosiyana ndi ine ndipo zikutanthauza kuti munthuyo sanalimbikisidwe ndi mzimu oyera ngati momwe inu munalimbikisidwira, koma kuika mphatso yawo mu utumiki oyenera kupangitsa kuti akhale opambana kuposainu.

Tikagwiritsa ntchito mphatso ya uzimu monga mwa chizolowezi tizagwira ntchito pansi pa mphamvu ndi malimbitso a mulungu, m'malo mwa pansi pa mphamvu ndi malimbitso athu koma tikugwiritsa ntchito mphatso yathu moyenera zidzakhala zodabwitsa ndipo tizatumukira ni chimwemwe.

PEMPHERO NDI KUPEMPHA

Tsopano ndi chifukwa chani timapemphera?

Mulungu amaziwiratu chomwe tikufuna ndiye ndichifukwa chiyani timapemphera? Ndi chifukwa choti timaganiza kuti mulungu sadziwa zimene

tikufuna ndipo tadziwa kuti tikunva kuphweka? Mwina timaganiza kuti atikondera mwapadera pamene tampempha mozichepetsa kuzera mpemphero.

Yankho lake ndi ili, pemphero lowona mtima, ndi kupempha ndi chikhulupiliro, tizipemphera ndikupempha kuti atipasadi.

Mulungu amafuna kuti tizimupempha, ndipo tikamupempha tikaonetse kuti timadalira ndipo tikudziwa kuti iye ndiye mwini zonse, ndipo e tikudziwa kuti kuti amadziwa zifuna zathu ndikuti alowelerepo ndipo tikudziwa kulowelera kwake, pemphero di kuonetsa chikhulupiliro, ndikudziwa adzasegula ndikutipatsa zomwe tikufuna.⁵⁸² pamene tisasira chifuniro chake ndi kumvera malamulo ake tikudziwa adzatidalitsa ndikukweza pamwamba pa maiko.⁵⁸³

Tingokhala achilungamo chifukwa mulungu amadziwa chomwe tikufuna osati tisiye kumupempha tiyenera ku pemphera chifukwa tikufuna tigwirizanitse chifuniro chathu ndi chake. Tiyenera kupemphera chifukwa tikufuna tikudze ubale wathu ndi mulungu. Lye adati, adzatisintha kuti tiziziwa chifuniro chake⁵⁸⁴ tiyeni tibweleze mfundo yofunikayi, kuzera m'pemphero ndikudalira iye maganizo athu osasithidwa ndipo tizatha kudziwa chifuniro chake.

SIMUKUSOWA ZOKONGOLORA KUPEMPHERA

Mungakhale mukuganizira nokha kuti mukufunafuna kupemphera koma simukudziwa kuti mungapemphere bwanji kapena mumaganiza kuti pemphero lanu simunalithe mu mawu oyera, iyi ndiwo nkhani yabwino mulungu anakusungira pamene muvomereza yesu kulowa mu mtima mwanu mzimu oyera uzakhazikika mu mtima mwanu⁵⁸⁵ ndipo chifukwa mzimu oyera amakudziwa kuposa m'mene iwe umadziziwira adzakuthandiza kuziwa kupemphera⁵⁸⁶ mzimu oyera adzakunenerani ndikuika chomwe mukufuna kunena m'mawu oyenera.⁵⁸⁷ Ndi m'dalitso wanjii uyu! Zomwe zikutanthauza kuti tizilora kugwiritsa ntchito mau oyenerera kumudza mulungu zomwe mukuganizazo. Zingofunikira chikhulupiliro⁵⁸⁸ mzimu oyera amadziwa zomwe mufuna ndi chomwe ukusowa ndipo akufunitsitsa mosavuta ndi mulungu pakuti umadziwa mmene tingapemphere.⁵⁸⁹

TIYENERA KUPEMPHERA CHIFUKWA KUDZAKHALA KUSALEMEKEZA MULUNGU POSACHEDWA

Cholinga cha pemphero ndi kusatira malangizo ndi kukhulupilira pa mulungu. Iye amafuna kuti tizipemphera ngakhale tili pamavuto⁵⁹⁰ ngakhale pa mtendere⁵⁹¹ tikadwala⁵⁹² ngati tachimwa⁵⁹³ ndipo pofuna machilitso. Lye anenanso kuti tiyenera kupemphera mosazionetsera.⁵⁹⁴ Ndikupemphelera otisautsa⁵⁹⁵ adatiphunzitsa kuti ngati tipemphera omwe satikonda ndi mphatso yanji yomwe tingapeze? ⁵⁹⁶ Tiyenera kupemphelera omwe satikonda ndikukonda adani athu ndikupemphelera onse otilonde ndipo mulungu anatiphunzitsanso kupemphera.⁵⁹⁷

Monga tayandikira kumapeto mulungu akufuna tipemphere kwambiri ndikupemphelerana wina ndi nzake. Adati kudzakhala kusalemekeza mulungu padziko pano posachedwa monga sitinaonepo ngakhale pachiyambi⁵⁹⁸ tiyenera kuzindikira kusafunikira ndikupanda mphamvu kwake popanda mzimu oyera pakati pathu.⁵⁹⁹

Pempherani tsiku ndi tsiku kuti mzimu wa mulungu akudalitsen. Ndikuthandizana kusintha miyoyo ya anthu omwe saziwa chinkozero cha mulungu. Chinthu choyamba kuchita chikhale kuuza anthu za bukuli.

KHALANI OWALA / ONG'ANIMA

Nyimbo Iyi

Pamene tikufika ku mapeto kwa bukuli, ndi chinthu chofunikira kuti mumvetsera nyimbo iyi, “Kupangidwa kuchita Utumiki.” Nyimbo iyi ndi nsanamila ya bukhu lonseli ndipo nyimboyi imathandiza kufotokozera zomwe Mulungu amafuna kuti ife tonse tichite. Mukhoza kumvetsera nyimbo imeneyi pa makina a intanet pa bebsite yathu:

<https://understandgodswill.com/our-song.html>

Pa chiyambi cha bukuli munawerenga za momwe olemba bukuli ndi yemwe andayimba nyimbo imeneyi adakumanirana - osati chifukwa cha mwayi - koma chifukwa cha chikonzero chake posonkanitsa uthenga wa m'bukhuli.

Mu nyimboyi muli mauthenga ambirimbiri omwe akukambidwa mu zigawo zotsala za ku mapeto a bukuli. Chonso tirindi chikhulupiliriro kuti mukhala ndi nthawi kuti muyimvetsera. Koma ngati simungathe kumvetsera nyimbo imeneyi pa zifukwa zina, ayi mawu a nyimoyi ndi awa:

Nyimbo:

KUPANGIDWA KUTI NDIKACHITE UTUMIKI

Woyimba ndi Wolemba Nyimbo:

Nikki Chapin Frizzell

Mowona mtima ndinalibe njira ndi mawu

Osati yokhutira nayo kwenikweni

Komanso yosati nkusuntha magazo

Ndiye ndi chifukwa chiyani ndingakhulupilire kuti ndingamufikire wina

Ndipo ndingamuphunzitse wina

Ndipo ndingawalondolere ku ufumu

kuwala kochepa mu m'dima

Ka liwu kamodzi
Ka lingaliro kamodzi
Koma ndikukhulupilira m'ku ng'anima
Ka lawi kakang'ono komwe kamayambitsa moto

Ndipo ndinapangidwa kuchita utumiki
Ndinalengedwa pa chifukwa
Ndidapulumutsidwa kuti nditumikire Mulungu
Ndipo adzadalitsa chiganizo changa
Ndipo ndidzamuwona wina wakeyo ngati wochepa
Ngati ine ndipangidwa kuchita utumiki

Sindingathe kuyerekeza momwe zingakhalire
Popanda chiyembekezo cha ku Mwamba
Ndipo popanda Liwu la Yesu Khristu
Choncho ndipita kunja ndikadali ndi nthawi
Ndipo ndikawafikira
Ndipo ndikawalondolera ku Ufumu

kuwala kochepa mu m'dima
Ka liwu kamodzi
Ka lingaliro kamodzi
Koma ndikukhulupilira m'ku ng'anima
Ka lawi kakang'ono komwe kamayambitsa moto

Ndipo ndinapangidwa kuchita utumiki
Ndinalengedwa pa chifukwa
Ndidapulumutsidwa kuti nditumikire Mulungu
Ndipo adzadalitsa chiganizo changa
Ndipo ndidzamuwona wina wakeyo ngati wochepa
Ngati ine ndipangidwa kuchita utumiki

Iye sadanene kuti ndikadadzapita mu ulemerero
Iye adangoti pita kunja pa pamazi ako
Ndikukabwera ndi munthu wina kwa Iye pobwerera ku nyumba.
Kotero, ine, ine, ngakhale ine, ndiwakuti ndikachite utumiki
Ndinalengedwa di cholinga
Ndidapulumutsidwa kuti nditumikire Mulungu
Ndipo adzadalitsa chiganizo changa
Ndipo ndidzamuwona wina wakeyo ngati wochepa
Ngati ine ndipangidwa kuchita utumiki

Chifukwa chiyani chiri chovutitsitsa?

Ndi chifukwa chiyani chimakhala chinthu chovutitsitsa kuti tikambe za chikhulupiliro chathu, kapena za Yesu? Timawopa kuti anthu ena aziti chiyani kapena kuti aziganiza chiyani? Timakhala ndi mantha kuti wina atitsutsa - kapena ali ndi maganizo osiyana? Timakhala ndi mantha kuti mwina sadzatifumanso?

Kapena tiri ndi chidziwitso chochepa pa za zomwe Baibulo limanena, kapena za kuti Yesu ndi ndani.

Izi si zinthu zomwe tidandaule nazo popeza Namalenga ali ku mbali yathu.⁶⁰⁰ Palibenso wina aliyense yemwe amapereka moyo. Taganiza izi mwa kanthawi. Tiyenera kumulambira iye yemwe amapereka moyo. A Mbuye amatiwuza kuti ngati muchita manyazi kwa anzanu pokamba za Iye. Iye adzakuchitiraninso manyazi akabwerera ku ulemmerero wa a Tate. Chinthu chosakhala bwino.⁶⁰¹

Ndi chinthu chovuta kwa anthu ena kugawana chikhulupiliro chawo ndi anthu ena chifukwa samvetsetsa chomwe Baibulo limanena. Sadakhalepo ndi nthawi yoti awerenge kapena kuphunzira Baibulo. Anthu ambiri samaphunzira Baibulo chifukwa ndi bukhu lovutirapo kuwerenga. Simungatsegule Baibulo ndi kuwerenga pa masamba angapo, kaya ma gawo angapo, ndi kumvetsetsa chomwe likunena. Baibulo ndi bukhu lokhala ndi mabukhu ena okwana 66 omwe amayenera kuwerengedwa monga momwe alirimo apo ayi ndiye kuti pakhala kusamvetsetsa kwakukulu pa chomwe Baibulo limanena.

China chosokoneza ndi chakuti mabukhu onse 66 sadasanjidwe mu ndondomeko ya nthawi choncho mukatsegula Baibulo ndikuyamba kuwerenga ngati bukhu wamba, mukusinkhasinkha mogwirizana ndi nyengo. Ichi chikhoza kukhala chinthu chosokoneza ndipo chingapangitse kuti anthu ambiri asamawerenge Baibulo - chomwe ndi chinthu comvetsetsa chisoni.

Kuyesa kufotokozero anthu ena za Yesu popanda kumvetsetsa cholinga chake chachikulu - zikhala ngati kuyesa kukamba za munthu womwalira pongowerenga za mbiri yake pa nthumbira yake. Sizingachitike. Alipo yemwe angakambe za munthu yemwe sakumudziwa? Kuti tikambe za munthu tiyenera kudziwa zomwe adanena, zomwe adachita, chinali chofunika kwa iwo ndi chiyani, chomwe iwo amayimirira, momwe adasamalirira anthu ena, chomwe adakhulupirira, ndi zina zambiri.

Izinso ziri chomwechi pamene wina wake m'kukambirana ayambitsa nkhani ya Yesu, kaya wina wake kutifusa ife za chikhulupiliro chathu. Timakhala a mantha. Mtima wanthu umathamanga. Timafuna tisinthe nkhani kuti tiyambe kukamba ina. Koma sizimayenera kukhala choncho. Timayenera kumvetsetsa chomwe Mulungu adatichitira ndipo timayenera kukhala omasuka kukamba za ichi. Uyu ndiye Mulungu wolenga kumwamba ndi pansu, Mulungu yemwe tikukambira

nkhani yakeyi. Ali ndi cholinga chachikulu, ndipo tiyenera kuwawuza anthu ena za cholinga chimenechi.

Mwina bukhu iri lithandiza, koma mukuyenerabe kuwerenga ndi kuphunzira Baibulo. Baibulo ndi Liwu la Mulungu, ndipo Liwu la Mulungu limakamba za cholinga cha Mulungu. Bukhulu iri liri ngati ka m'bulu kamankhwala kakang'ono pa zomwe Baibulo limanena. Tikuyenera kukhala okonzeka kuwafotokozera anthu ena pa chiyembekezo chomwe tiri nacho.⁶⁰² Apatsemi anthu ena bukhuli kuti nawonso aphunzire zomwe inu mwaphunzira. Musasunge nkhani yabwinoyi kwa inu nokha. Auzeni ena za bukhuli. Mukhoza kupita pa makina a intaneti pa *website* yathu ndikukapeza bukhu limeneri pochita download mwa ulere - kenako ndi kuwatumizira anthu ena mu njira ya e-mail. Mukhozanso kuyitanitsa kathumba koyikamo bukhuli.

Ngati muli nkusautsidwabe kukhulupirira za kuti mudalengedwa ndi cholinga - chonde werenganinso Gawo 4 komanso ndime yomwe ikukamba za kuthekera kwa kuti simudapangidwe mwa Ngozi popanda Mlengi. Potengera Masamu amenewa a kuthekera (*Probability*), yankho lake ndiye ndi ka nambala kakang'ono kwambiri kosamvetsetseka. Potengera masamu amenewa a kuthekera, kunena kuti dziko lapansi ndi zonse zokhalamo zidapangidwa mwa ngozi, yankho lomwe lingapezeke ndi ka nambala kakang'ono kwambiri kotero kuti sitingamatayenso nthawi kukamba za kameneka. Tikapita mu Gawo 4 yankho lake linali $1/10^{322}$. Nambalayi ndi chimodzimodzi ndi .000 (kuphatikizaponso ma zero ena okwana 319) kenako 1. Ndipo kanambala kochepe chotereka komwe kakufutokozera kuthekera kwa kuti munthu analengedwa mwangozi kalinso chomodzimodzi ndi zolengedwa zina zonse monga nyama ndi zomera. Choncho ndi ka nambala kakang'ono kakuti sitinganene kuti munthu kaya zolengedwa zina zinabwera mwangozi. Ndikukhulupirira kuti izi zakutsegulani m'maso kuti simunabadwe mwa ngozi. Inu ndi ntchito ya luso lapamwamba yopangidwa ndi cholinga ndi Mulungu wachikondi chodabwitsayo. Mukungoyenera kufufuza kuti kodi cholinga chanu ndi chiyani ndikuyambapo kukwaniritsa cholinga chimenechi.

Mungapange chiyani tsopano

Tikuthokozeni kwambiri pokhala ndi nthawi, kuwerenga bukhu iri ndipo tsopano mukumvetsetsa kuti Yesu ndi ndani. Komanso mukumvetsetsa chomwe Yesu adakupangirani inu komanso chifukwa chimene adapangira chimenechi. Tikukhulupirira kuti mwalandira mphatso yake ya ulerereyi kotero kuti mukhoza kuyamba kukhala moyo wanu ndi cholinga. Ngati simudalandire mphatso yake ya ulerereyi, pempherani kuti Mzimu wa Mulungu akuthandizeni kuti muvomere chowonadi chake. Musalole woyipayo kuti azikunyenganibe.

Satana ndi wamakani kwambiri. Satana akhoza kumakupatsani ma bodza ake ngakhale mu nthawi ino - kukuwuzani kuti bukhu iri ndilosafunikira kaya kukuwuzani kuti dikirani kaye mupangabe chiganizo chani nthawi ina. Iyi ndiyo

ndale yake: kuchedwetsa, kusokoneza, kukupangani inu kuti mutangadidwe ndi zinthu zina, komanso kukusocheretsani. Chitani ichi tsopano. Werengani pemphero lomwe liri mu Gawo 5 ndi kulola Mulungu kuti alamulire moyo wanu. Kukhoza kukhala kophweka kusiyanana ndi kuti mulamulire moyo mwa inu nokha. Mulungu adzakutsoyokerani, kukudzadzani ndi m'dalitso, kukutonthozani, ndi kuwalitsa njira yanu. Pamene mulandira Mulungu mu mtima mwanu mzimu wanu udzapulumutsidwa ku moyo wosatha. Muyaya! Musalakwitse kuti mukaponyedwe kuchiwonongeko cha muyaya. Muyaya ndi nthawi yayitali kwambiri.

Choncho mutalandira Yesu kukhala Mbuye ndi Mupulumutsi wanu, mukhoza kukhala onyadira podziwa kuti mwapulumutsidwa ndi kusunga nkhani yokomayi kwa inu nokha, Choncho?

Cholakwika

Pali anthu ambiri, kuphatikizaponso a bwenzi anu, mwinanso a bale anu, ndi anthu ena ambiri omwe akaponyedwe ku ng'anjo ya moto ngati sadaphunzire zomwe inu mwaphunzirazi. Tiyenera tiwapeze ndikuwawuza za zomwe Yesu adatichitira ife tonse. Pakhoza kukhala anthu mu dera lanulo, anthu omwe mumagwira nawo ntchito, anthu omwe mumasewera nawo limodzi, anthu omwe mumachita nawo masero olimbitsa thupi limodzi, anthu omwe mumawawona mu sitolo la khofi, anthu omwe mumapita nawo ku sukulu, anthu omwe mumadutsana nawo mu msewu, mwina anthu omwe mumakumana nawo mu sitima kapena mu busi pamene mukupita kapena kuchokera ku ntchiti. Aliyense mwa anthu amenewa ayenera kuphunzira zomwe inu mwaphunzirazi - weina aliyense. Ndi anthu ambiri. Kwa ambiri a ife iyi ikhoza kuwoneka ngati ntchito yosatheka. Zingatheke bwanji kuti tikafikire munthu wina aliyense - mu dziko lonse lino? Izi nzosatheka, sichoncho?

Ayi, sichoncho.

Tamvetseraninsu nyimbo ija, ndipo mukhulupirire. Khulupirirani kuti mukhoza kukhala ong'anima. Kukhala ong'anima ndi chinthu chozavuta kuchita. Wina aliyense wa ife akhoza kukhala kuwala / ong'anima - tangoganizani za ka mtengo ka machesi kakang'ono komwe kamabuka kukhala lawi, lawi lomwe limayambitsa moto. Ka mtengo ka machesi kameneka mukhoza kukhala inu. Mwina simunakhutitsidwepo, kutembenuzidwa, simuchita bwino polankhula. Nkosavuta kuganiza kuti simungachite zenizeni chifukwa ndinu achichepere, ndipo izi ndi zomwe Satana amafuna kuti inu muziganiza. Mukhoza kudabwa kuti kodi munthu wina mungamufikere bwanji, kumuphunzitsa, komanso kumulondolera ku Ufumu.

Tamvetseraninsu nyimboyo, Mukhoza.

Eya, ndinu kuwala kochepe mu m'dima. Eya, ndinu ka liwu kamodzi kochepe. Eya, ndi kaganizo kamodzi kochepe. Koma tsopano mukudziwa kuti mukhoza kukhala ong'anima, ka lawi kochepe komwe kamayambitsa moto. Mudapangidwa kuti mukachite utumiki. Mudapangidwa ndi cholinga. Mudapululumutsidwa kuti mutumikire Mulungu ndipo adzakudalitsani chifukwa cha chiganizo chanu.

Kwa munthu wina ochepe ngati inu, okhala ndi kachikhulupiro kochepe, kachikhulupiro kochepe nga ka mbewu ka mpiru,⁶⁰³ mudzawona kuti munthu wina ochepe ngati inu akhoza kubweretsa kusintha. Ichi chikhoza kukhala kuwala kwanu komwe kumayambitsa moto mu mzinda kapena tawuni yanu, kudera kumene mukukhala, ku malo anu a ntchito, m'basi yanu kapena mu sitima yanu pamene kupita kapena kuchokera ku tchito, pa kalabu yanu ya za umoyo, kapena ku sitolo lanu la khofi, kamanso m'malo ena ambiri.

Sitidzachita ichi um Ulemerero

M'modzi wina aliyense wa ife akhoza kufikira wina wake, anthu omwe tikuwadziwa, komanso anthu omwe sitimawawona kawirikawiri - mwina anthu omwe akuzungulirani, abwenzi ndi anthu ena. Pamodzi tikhoza kufikira wina aliyense. Chomwe tiyenera kukhulupirira ndi chakuti tiyenera kukhala ong'anima / owala, kuwala komwe kumayambitsa lawi, lawi lomwe limayambitsa moto, moto omwe sungazimitsike. Moto umenewu ukhoza kuyaka dziko lonse lapansi, kwa munthu wina aliyense, ngati tikhulupirira.

Monga nyimbo ikunena, Mulungu sadanene kuti izi tidzazichita mu Ulemerero. Sitidzakhala otchuka. Iye adangonena kuti tipite pa mapazi athu ndi kukabweretsako munthu m'modzi kwa lye pamene tibwerera ku nyumba. Chifukwa chiyani tikadachita ichi? Chifukwa chiyani tikadawawuza anzathu kuti ena kuti awerenge bukhu iri? Ndi chifukwa chakuti - Yesu adakuferani. Adapita pa mtanda ndipo adali ndi misomali yokhomedwa m'manja ndi m'mapazi ake pamene adapachikidwire pa mtanda kufikira pamene adamwalira. Pamene adapachikidwa pa mtanda adatenga zochimwa za dziko lonse la pansi pamodzi ndi lye ku imfa yake⁶⁰⁴ - ku nthawi zonse. Ndipo zonsezi adakuchitirani inuyo komanso ine. Adatenga machimo anu onse a m'mbuyomu, a lero komanso a mtsogolo. Ngakhale machimo anu a m'tsogolo. Chomwe inu mukuyenera kuchita - ndi kukhulupirira.

Nthambi ya mtengo yomwe adapachikidwapoyo adayilenga ndi lyeyo. Phiri la miyala pomwe mtanda wake udazikidwa, adalenga ndi lye. Misomali yomwe idakhomedwa m'mapazi ndi m'manja ake idapangidwa ku cholengedwa chake chapamwamba (Chitsulo). Adatiwuzwa kuti izi zidzachitika zaka 800 lye asanabwere ku dziko la pansi.⁶⁰⁵ Ndipo kudzera mwa Mneneri wake Yesaya, adatiwuzanso kuti adzamwalira - kuti "adzakhomedwa chifukwa cha zochimwa zathu."

Ndipo atabadwa mwa Maliya, izi chidachitikadi ndendende monga momwe adanenera. Izi zonse adazichita chifukwa amakukondani kwambiri. Inu. Inu nokha. Izi akadachita ngakhale kuti munali inu nokha - munthu m'modzi - pa dziko lonse lapansi. Inu ndi cholengedwa chake cha mtengo wapatali. Adabwera ku dziko la pansi kudzapulumutsa mzimu wanu, mzimu womwe adawulenga kuti udzakhale ndi lye mpaka muyaya. Koma - muyenera kukhulupirira. Ndipo muyenera kulandira mphatso yake. Ndipo adzadalitsa chiganizo chanu ndipo akufuna kuti mudziwe kuti wina wake wochepa ngati inu nomwe adapangidwa ndi cholinga.

Ndi chifukwa chiyani Mulungu amafuna kuti inu mukhale owala / ong'anima

Pali zifukwa zambiri:

- (1) Chifukwa a Mbuye adatiwuza ^{606 607}
- (2) A Mbuye adatiwuza kuti nthawi zonse zizikhala okonzeka kufotokozera chiyembekezo chomwe tiri nacho. ⁶⁰⁸
- (3) Ambuye adatiwuza kuti tichitire anthu ena zomwe ifeyo tikufuna kuti anthu ena atichitire. ⁶⁰⁹
- (4) A Mbuye adatiwuza kuti tiwawuze anthu ena - Kaya afufuna kumvetsera, kapena. ⁶¹⁰
- (5) Ngati muchita manyazi kukamba za lye, lye adzachitira inu manyazi mu Ulemerero. ⁶¹¹
- (6) Chifukwa chimodzi cha zipatso za Mzimu ndiye kufotokozera anthu ena. ⁶¹²
- (7) Chifukwa kufotokozera anthu ena ndi chinthu cha nzeru. ⁶¹³
- (8) Chifukwa kufotokozera anthu ena zidzawathandiza kuti asadzaponyedwe ku kanjo ya moto. ⁶¹⁴
- (9) Chifukwa kufotokozera anthu ena kudzakondweretsa Mulungu. ⁶¹⁵
- (10) Chifukwa kufotokozera ena kumapereka mwayi oyanjana ndi Mulungu. ⁶¹⁶
- (11) Chifukwa kufotokozera ena kudzakondweretsa Angelo. ⁶¹⁷
- (12) Chifukwa kufotokozera ena kuthandiza kupeza anthu ochuluka ogwira ntchito m'mundamu ntchito yopulumutsa miyoyo yotayika. ⁶¹⁸

Njira zina zomwe inu (inde, inu!) mungachite kuti mukhale owala / ong'anima ndi izi:

Pali njira zambiri zakuti inu mukhoza kuchita kuti mukhale owala / ong'anima. Zochepa chabe nazi. Mosakayikanso mudzakhala mukuganiza za njira zinanso.

Muzisonkhana pamodzi ndi anzanu okhulupirira ndikulemba zinthu zonse zomwe mukufuna mutazichita ndi njira zomwe mungatsate kukwaniritsa ntchito zimenezi. Khalani owala / ong'anima - ndipo yatsani moto!

- (1) Awuzeni anzanu komanso ngakhale anthu rna omwe mumangowadziwa pang'ono za bukhu iri. Apatseni bukhu limodzi, kapena muwatumizire pa e-mail bukhu lathu laulere la pa intanet, kapena auzeni za bukhu lathu lomvera laulere. Mwina mumvetsera bukhu limeneri ndi anzanuwo?
- (2) Asiyireni anzanu bukhu mu bokosi lawo la makalata. Mwina muphatikizapo ka kalata kolemba kuti wina wake amawakonda.
- (3) Tumizani mabukhuwa ku magulu auzimu a achinyamata omwe mukuwadziwa.
- (4) Tumizani mabukhuwa ku mabungwe a za chifundo omwe mukuwadziwa.
- (5) Tumizani bukhu limodzi kwa atsogoleri anu a Mpingo mu mzinda wanu komanso kwina kuli konse kuti awuzenso anthu ena za bukhu.
- (6) Yambani kagulu kakang'ono ndipo werengani ndi kuliphunzira bukhu nonse pamodzi.
- (7) Tumizani mabukhu ena ku magulu kapena mabungwe ena a auzimu a kunja.
- (8) Tumizani mabukhu ena kwa abale anu omwe sadziwa kuti Yesu ndi ndani.
- (9) Werengani kapena mvetserani bukhu limeneri pa nthawi ya madzulo pomwe mukucheza ngati banja ndi ana anu.
- (10) Tumizani mabukhu ena ku nyumba za anthu okalamba (Mwina muwayendere ndi kukawawerengera?).
- (11) Tumizani mabukhu ena ku nyumba za ndende.
- (12) Apatsekoninso bukhu anzanu omwe mukukhala nawo chinyumba chimodzi.
- (13) Apatsenikonso bukhu anthu m'maphando a mu mzinda ngakhaleonso m'misonkhano ya boma.
- (14) Wonetsetsani kuti bukhu likupezeka ku ma tchalitchi ndi malo ena opempheramo.
- (15) Wonetsetsani kuti bukhu likupezeka m'malo ogulitsiramo zakudya ndi m'makwalala (monga kwa osowa, amayi ndi abambo ndi ena otere).
- (16) Wonetsetsani kuti anzanu ogwira nawo ntchito ali nalo bukhu.
- (17) Wonetsetsani kuti a bamboo ndi a mayi omwe ali okha ali nalo bukhu.
- (18) Wonetsetsani kuti magulu a amayi ndi a bamboo a khofi ali nalo bukhu limeneri.
- (19) Nthawi zonse muzitenga mabukhu ena ndikuwapatsa anthu omwe Mulungu wakonzani ku mukumane nawo.
- (20) Tumizani mabukhu ena kwa anthu ogwira ntchito za boma kaya mabungwe m'makwalalamu ameni mukuwadziwa.
- (21) Tumizani mabukhu ena kwa ma dotolo ndi a phungu a za umoyo omwe mumawadziwa.
- (22) Tumizani mabukhu ena kwa anthu a ndale omwe mumawadziwa.

- (23) Tumizani mabukhu ena kwa a phunzitsi a za mabizinezi komanso atsogolleri a ma buzinezi omwe mumawadziwa.
- (24) Tumizani mabukhu ena kwa a phunzitsi komanso a phunzitsi a m'sukulu za ukachenjede omwe mumawadziwa.
- (25) Zungulirani mu mzinda wanu kapena tawuni yanu kugawa mabukhu ameneri.
- (26) Nyumba za Mabukhu m'dera lanulo zidziwe za bukhu limeneri.
- (27) Nyumba za kanema, nyumba zofalitsa nkhani ndi nyumba zowulutsira mawu zidziwe za bukhu limeneri.
- (28) Perekani ngati mphatso bukhu limeneri m'zikondwerero - kukondwerera masiku obadwa, ma ukwati ndi zina Zotero.
- (29) Kwa iwo amene akusinkhasinkha zothetsa ukwati wawo akhale nalo bukhu limeneri.
- (30) Amene akusinkhasinkha zokwatira akhale nalo bukhu limeneri.
- (31) Odwala, omwe ali kunyumba kaya mchipatala akhale nalo bukhu limeneri.
- (32) Kwa iwo amene ataya okondedwa awo (monga, mwana, mkazi, mamuna, kaya ena otero) akhale nalo bukhu.
- (33) Alangizi a anthu osweka mtima akhale nalo bukhu.
- (34) Yambani gulu lophunzira Mawu a Mulungu ndipo muzigwiritsa nthcito bukhu limeneli komanso Bukhu lotsogolera pa ma gulu a uzimu (Lomwe li pa pakina a intanet pa *website* yathu) kuti zikitsogolereni pa maphunziro anuwo.
- (35) Pezani kagulu ka ana a sukulu pa sukulu panu ndipo phunzirani bukhu iri pamodzi. Ndipi auzeni ana ena omwe Sali nawo pa gululi kuti akuphonyana ndi mdalitso. Khalani kuwala kwa onse ndipo auzeni ana a sukulu ndi a phunzitsi omwe za bukhu limeneri. Auzeni kuti ndi bukhu lakuti ayenera kuliwerenga basi. Auzeni kuti ndi laulere - ndi kuti akhoza kupita pa *website* pathu mu intaneti ndi kuwerenga ena mwa mabukhu athu aulerere kaya kumvetsera ena mwa mabukhu athu pogwiritsa nthcito ma foni a makonowa ndi zipangizo zina zomvetsera mawu.
- (36) Auzeni anthu kuti akhozanso kuyitanitsanso kathumba koyikamo mabukhu.

Ena aliwonse mwa maganizo amenewa ndi njira yakuti inuyo mukhale owala / ong'anima, kuti muyatse moto dziko lonse la pansi, koma, zowonadi mukuyenera kupezanso njira zina zambiri zakuti zingakupangitseni inu kukhala ong'anima.

Khalani "Oyambitsa"

Pali njira zambiri za momwe mungakhalire owala / ong'anima monga zalembedwera pamwambapa, koma pali njira imodzi ya kuwala komwe kukhoza kukhudza miyoyo zikwizikwi kapena mazanamazana. Uku ndiye kukhala oyatsa moto - kukhala oyambitsa. Kukhala oyambitsa ndiye kuti muli ndi kuthekera okokopa anthu ena ndi zomwe mwadalitsika nazo - mwina chuma chanu, mwina kuthekera komatanthauzira zinenero (Tikufuna zimenezi, chonde tifikireni), kaya

kuthekera kwanu kosindikiza ndi kugawa zinthu (monga bukhuli), kaya mwina muli ndi luso lina.

Kulemera sikuti, nthawi zonse, ndi ndalama. Pali anthu ambiri m'madera ambiri a pa dziko lapansi omwe sikuti ali ndi zambiri koma amadzitenga kuti ndi olemera. Ali ndi banja. Ali ndi a bwenzi. Ali ndi Chimwemwe chenicheni cha mu mtima mwawo. Ali ndi chakudya chokwanira kudyetsa banja lawo madzulo anu. Ndipo ali ndi chikhulupiro chomwe chimawapatsa chitsimikizo.⁶¹⁹ Sali olemera pa makobidi, koma akhoza kodzitenga ngati olemera mu njira zosiyanasiyana. Ena a ife tikawona mmene akukondwera, ndi zinthu zochepa zomwe ali nazo, timadabwa kuti kodi chisangalalo choterechi tingachipeze kuti. Mukhoza kukhala nacho. A Mbuye adzawunjika m'dalitso wake pa inu kudzera m'malonjezano ake.

Chuma, inde chikhoza kutanthauza kuti muli ndi ndalama zochuluka (chomwe ndi tanthauzo lodziwika bwino), koma kulemera kukhoza kukhala kuchuluka kwa pafupifupi china chiri chonse. Mukhoza kukhala ndi kudzazidwa ndi chikondi cha kwa anthu ena, mukhoza kukhala ndi mphamvu zambiri zokopera anthu ena, mukhoza kukhala ndi luso lopanga zinthu zaluso lochuluka, mukhoza khala munthu wachikondi kapena wachifundo kwambiri. Choncho kukhala oyambitsa ndikugawa chuma chanu mu njira yayikulu. Ndiye kupeza njira yogwiritsa ntchito chuma chanu kuti chipindulire anthu ambiri osati ochepa chabe.

Khalani a nzeru ku chofunikira ichi

Kukhala oyatsa / oyambitsa zimafanana ndi munthu yemwe wanyamula muni / sakali - ndipo pamene ayenda kudutsa nyumba yomwe muli zochitika zambiri zophulitsa phulitsa (*Fireworks*) amayenera kudziwa kufunikira kwake kwa momwe angayendere mu nyumba imeneyi. Woyatsa amadziwa kuti akhoza kuyambitsa moto wambiri mu njira yake yayikulu. Amadziwa kuti kamoto kochepe (iyeyu) kakhoza kupangitsa phokoso lalikulu la zophulitsaphulitsa pena paliponse. Zophulika zina zilowera kum'mawa, zina kumadzulo, zina kumpoto ndipo zina kumwera. Zina zipita m'mamba, zina pansi. Ndipo zina sizingayake nkomwe (monga iwo amene asankha kusakhulupirira).

Oyatsa wanzeru amadziwa kuti ndi ka moto kakang'ono akhoza kuyambitsa ma lawi ambiri, ma lawi ambiri omwe okhoza kuyambitsa moto wambiri omwe sungazimitsike. Oyatsa ali ndi masomphenya ndi chilakolako chofuna kusintha dziko lapansi chifukwa akudziwa kuti adadalitsika ndi chikhulupiro, kapena kulemera pa makobidi, kapena zonse zimene. Oyatsa amafunitsitsa kugawa chuma chawo kuti apititse patsogolo Ufumu wa Mulungu chifukwa iwo akudziwa kuti adapulumutsidwa - ndipo kuti ntchito yokhayo yatanthauzo yomwe yatsala pano pa dziko la pansi ndiyo kutumikira uyo amene adawalenga.

CHIFUNIRO CHA MULUNGU CHICHITIKE MUNGAZIWE ZA UBWINO

KUKONDA NDI KUPANDA BANGA KWA MULUNGU

Nthawi zonse mutilangiza malangizo a mulungu kuti mudziwe za chifuniro chake. Baibulo ndi mau a mulungu wokhao tingapezemo chifuniro, ubwino, kukonda komanso kupanda banga kwake.⁶³² Chifuniro cha mulungu sichachinsisi kapena chobisika pa iwe ai koma kungofunika kuchisakasaka ndi kuchigwiritsa ntchito pa moyo wako.

M'baibulo ndi momwe tingapeze chifuniro cha mulungu ndi moyo wathu. Mwasegula ndi kuwewrenga baibulo tsopanoli? Mwina ndi nthawi ya bwino, pezani magulu ophunzitsa baibulo kapena yambani kupeza nthawi tsiku ndi tsiku yowerenga baibulo pa inu kuti kuti musapusisidwe pophunzira kuti mulungu ndi ndani.^{633 634}

Musaiwale kuti satana akukupangani kuti mukhale osadziwa mau amulungu ndi chifuniro chake pamoyo wanu. Mungapewe zonyenga za satana pokhala angelo akuunika⁶³⁵ koma zitengera kulimba mtima komanso nhawi yaitali. Mukaonetsa kulimba mtima mulungu adzakudalitsani mphantho ya moyo wosatha.⁶³⁶ Ngati mwakhazikika mukuwerenga mau a mulungu kumbukirani kuti mau a mulungu Sali ngati mpikisano kuti mwakanthawi kochepa muwerenge zambiri koma zili ngati mankhwala ophera tizilombo tononga mbeu (marathon) zomwe ndi zanthawi ndi nthawi osati zongoganizira.

KODI MUMAKHULUPIIRA?

Mumakhulupilira kuti baibulondi mawu a mulungu? Yankho kufusoli sungangotengera m'mene umalionera baibulo koma zitengera kuti umalola baibulo kusogolera moyo wako⁶³⁷ ngati mwakhulupilira kuti baibulo ndi mau a mulungu uyenera kuliwerenga, kuli chikhulupiliro ndi kulimekeza.

Baibulo likhale chosokoka kuchipinda chako chogona komanso chowulamulira. Mulungu sangalore kuti udutse munyengo zosiyanasiyana ndi zomwe baibulo likunena chifukwa baibulo ndi mau a mulungu. Nthawi zonse gwiritsani ntchito baibulo kuti musiyanitse ndi zomwe mwazona ndikuzimva kuti ndizoonaka kapena ndizosiyana ndi zomwe baibulo likuphunzitsa.

Gwiritsani ntchito baibulo kukhala muyeso oyenera pa chilichonse chomwe mukuchita ndi pa ziwano zikuluzikulu zomwe mukupanga. Kukhala osakhulupilira baibulo kuti baibulo ndilo choonadi, kumapereka mpata kwa oipayo kuti aikunyenga zomwe zingakusephanitse ndi m'busa wako.

Khumbo la mulungu ndiloti akapululumuke⁶³⁸ koma mwasoka koma mwasoka a sionse amene angapululumuke chifukwa cha chifuniro cha ulere chomwe mulungu

anachipereka kwa paife, anaziwiratu kuti anthu ena ambiri azanamidwa.⁶³⁹ anadziwanso kuti anthu ena azapiliza kukhala m'moyo osadziwa, musaloew kuti zichitike kwa inu.

MULUNGU AFUNA ONSE A IFE

Kuti ukhale chifupi ndi mulungu uyenera kupanga zomwe akunenadi.⁶⁴⁰ sungangosankha ndi kusatira okhawo malamulo a mulungu omwe ukufuna koma ayenera kusatira onse. Kungosankha ndi kusatira malamulo omwe ukufuna zilingati kuti sichifuniro mulungu koma changa. Ngati ukuganiza kusatira malamulo omwe akusangalatsa ndi kulemekeza mulungu-pepa m'bale sichoncho pampeto pake yesu adzanena kuti sakudziwa.⁶⁴¹ Kusunga malamulo ake onse ndi njira yokhao tingaonetsere chikondi chath pa mulungu-ndipondichokhacho ndingakhalebe m'chikondi chake. Kusunga malamulo ake zipangitsa kuti madalitso ake afikire miyoyo yathu.

Mulungu akufuna akhale chifupi ndi iwe ndipo pamene ukupemphera siya kusamvera kwako azakumva ndi kukuchiza.⁶⁴² Ukakhala nzake adzakululira zolinga zake ndi zomwe wakonzera moyo wako⁶⁴³ Ngati ndiwe nzake wa yesu chilichonse mulungu wamuululira yesu adzakuchilisanso.⁶⁴⁴

NTCHITO YATHU PA DZIKO LINO LAPANSI

Ntchito yathu pa dziko lino la pansi zaikidwa mu pemphero la ambuye wathu. M'menemo ndi momwe tingapempherere:

“atate wathu mulikumwamba, dzina lanu liyeretsedwe, ¹⁰ ufumu wanu udze, kufuna kwa nu kuchitidwe, monga kumwamba, chomwechonso pansi ano, mutipatse ife lero chakudya chathu chalero, ¹² mutikhululukire ife kudzochimwa zathu, monga ifens tiwakhululukira adani wathu, ¹³ musatitengere ife kokatiyesa koma mutipulumutse kwa oipayo.

MATEYU 6

Mukaona mu ndime ya 10 yomwe ikuti ntchito yathu ndikubweretsa ufumu wa mulungu ku dziko lapansi? Chipulumutso chathu chalonjezedwa pamene tangoika chikhulupiliro chathu pa yesu koma wanthu pa dziko lino lapansi adalira zomwe mulungu watulonjezera chikatha chipulumutso kuzera kumvera kwathu mau ake ndi kusiya zintchito zakale pambuyo ndi kusegula maso pa ulemelero wathu uli nkuzawo.^{645 646} Zomwe zikukanika kuti tikhale mu nzeru za yesu.⁶⁴⁷ Zomwe zikufunika kuti tiziwerega baibulo kuti tisamachite manyazi pamene tikupereka mwayi powauza anthu ena.^{648 649} Kuphunzira kwathu mau a mulungu kukulitsa kuthekera kokondana, kopereka chimwemwe ndi chisangalalo komanso kuthekera komvetsetsa kukhala ndi kuya kwa chikondi cha khristu kuti chopatsa nzeru zonse.⁶⁵⁰

Ndiye monga mukuona, yathu pa dziko lino la pansi ndi kubweretsa ulemelero kwa mulungu ndi umboni kwa munthu aliyense tingakumane naye zonsezi ndi ndizotheka ngati tamphunzira ndi kugwiritsa ntchito zomwe baibulo limanenera ndipo timagwiritsa ntchito zimene tikuphunzira ndi chikhulupiliro chathu mu chilichonse tingapange.

Izi ndi mbali zina zomwe baibulo limanenera kuti tisatire maphunziro ake komanso tilore mzimu oyera kuyenda kwa ife:

- Khulupilira ambuye mulungu wako⁶⁵¹
- Tikhale mu chifuniro cha mulungu⁶⁵²
- Sankhani ufumu wake muchilichonse mukuchita⁶⁵³
- Yamikani mulungu mu nyengo zonse pamabvuto ndi pamtendere⁶⁵⁴
- Lemekezani mulungu mu chilichonse, lemekezani ukulu wake⁶⁵⁵
- Lemekezani ndi kugwira ntchito yake muchifuniro chake.^{656 657 658}
- Fufuza zabwino za ena.⁶⁵⁹
- Lola kuwala kwako kuwalire ena kuti aone ubwino wa ntchito zako ndikulemeza atate wathu wakumwamba.⁶⁶⁰
- Khazikitsani bata pa zoyankhula za wanthu osakhulupilira kuzera mu ntchito zanu zabwino.⁶⁶¹
- Usachite chigololo.⁶⁶²
- Phunzitsa, dzudzula, ndipo konza zolakwikaza ena moyera mtima.⁶⁶³
- Pemphera moona ndi moyera mtima ndi chikhulupiliro kuti mulungu kuti mulungu adzakuyankha.⁶⁶⁴
- Pemphera chikhulupiliro, madalitso ndipo khala ndi chikhulupiliro pokhala chifupi naye.⁶⁶⁵
- Pakamwa pako patsatulutse mau oipa⁶⁶⁶ ndipo usatchule dzina l mulungu wako pachabe.
- Pangani chifuniro cha mulungu nthawi zonse ngakhale muznzidwe.⁶⁶⁷
- Khala ndi mtima opatsa ndi wachikondi usadzisungire chuma pa dziko lapansi koma kumwamba.^{668 669}
- Khala opilira.⁶⁷⁰

DALITSO LOSILIZA

Tinaymba bukuli ndi kunena kuti pali ziganizo ziwiri zofunika kwambiri kupanga kuti udziwe kuti mulungu ndi ndani.

Chiganizo cha chawiri chomwe tangochikwaniritsa kumene chinali chotise gula mtima ndipo ukhale oseguka mu nthawi ya bukuli, sangalalani pokwaniritsa ntchitoyi panopa pitilizani kudziwa kuti mulungu ndu ndindani ndipo chifuniro chake ndi chotani ndi moyo wanu. Tangosegula mtima wako kuti mulungu ayakhule nawe, akutsogolere ndikuti akudalitse chifukwa ali ndi zambiri kuti ayankhule nawe akufuna ukhale nzako, ndipo akufuna adziulure kuti iye ndi ndani pa ife. Tangopeza nthawi ndi kumvetsetsa zomwe zatchulidwazi. Namalenga akufuna akhale nzako ndiwe ntchito ya manja ake, mzeru zake, ndiwe chimodzi cha zolengedwa zake, ndipo ndiwe luso lake. Akufuna kuti udziwe chifuniro chake ndikuti akufuna kugawana nawe ufumu wake pothandizira kuti udziwe zonsezi anakulenga ndi chikhumbokhumbo chofuna kudziwa chifukwa chani anakulenga ndi cholinga chako ndichai, ndipo bukuli di chiyambi chabe, zitengera iwe kuti upititse ulendo wako opita nufuza.

Tsopano pa ziganizo zikuluzikulu zomwe ungapange chopambana kwambiri ndi kukhulupilira kuti mulungu anatuma mwana wake yesu ku dziko lapansi kudzafera machismo athu. Chimenechi ndi chiganizo chokhacho chingakupulumutse ku uchimo wako. Mulungu anapanga iwe mukulimbika kwake konse choncho uyenera kukhala okhulupilira. Mulungu anapanga malingaliro ndipo malingalirowa anaonetsera kupanda banga kwake kwa yehova. Chomwe munthu anagapange kuti apaeze chipatso cholowera kumwamba.⁶⁷¹ Palibe njira ina iliyonse yopezera kapena kugulira chipulumutso. Tangoonetsera chikhulupilira kwa yesu.⁶⁷² Mulungu anapanga mphatso kuti apereke kwa aliyense koma kuti⁶⁷³ upulumusidwe uyenera ubvomereze mphatso yake kuzera mwa yesu⁶⁷⁴ mabala ako achilidwa, sunavomereze mphatso yake bwelera ku mutu 5 ndi kumphunzira m'mene ungavomerezere mphatso yakeyo udzalandira mphatso yaikulu.

KUKHALA NDI CHOLINGA

Aliyense wa ife ali ndi moyo umodzi kuti akhale ndipo ambiri a ife akufuna akhale moyo umeneu ndi cholinga. Ndinu m'modzi mwa iwo? Ukufuna kudziwa cholinga chako kuti ndichani? Ukhoza kudziwa koma uyenera kumudziwa mulungu ndipo adzamba pempho ndi pemphero lako ngati ukukhulupilira kuti anatomiza mwana wake yesu ku dziko lapansi kuti akaulumutse iwe kumachimo ako.

Ukangopanga chisankho chimenechi mulungu adzalowa mu mtima mwako ndipo mzimu ndipo mzimu woyera wa mulungu adzakuthandizira ndi kukutsogolera ndi nzeru kuti umudziwe iye kwambiri^{675 676} koma sizikutanthauza kuti uzalandira maitanidwe posachedwa ayi ukufunikira kuti upilize kuwerenga mau a mulungu udziwe kuti mphatso yanji ya mzimu yomwe mulungu apkupatsa

